Chisindikizo
Chachisani Ndi Chiwiri



Zikomo inu, m'bale. Pamene ife tiri chiyimire, tiyeni tipemphere.

2 Mulungu Wamphamvuzonse, Mwini wa Moyo, ndi Wopereka wa mphatso zonse zabwino, zauzimu, ndithudi ife tiri oyamikira tsopano chifukwa cha nthawi yodabwitsa kwambiri iyi, yaikulu, ya chiyanjano mu Kukhalapo Kwanu; zikupanga nthawi yopambana kwakukulu mmiyoyo yathu, Ambuye, nthawi yomwe ife sitidzaiyiwala konse, ziribe kanthu kaya tikhala nthawi yotalika chotani. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti pa usiku wotsekera uwu . . . Ife tikulizindikira Lemba, pa tsiku la kutsekera kwa phwando, Yesu anaimirira pakati pawo ndipo anafuula kuti, "Ngati wina amva ludzu, muloleni iye adze kwa Ine!" Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti izo zibwereze kachiwiri usikuuno, kuti ife tikhoze kumva Liwu la Ambuye wathu likutiyitana ife, ndi kutiyitanira ife kukalowa mu utumiki wa Iye, kukayenda chifupi. Ife tikumverera kuti talimva kale Liwu Lake, mu kutsegula kwa Zisindikizo izi, likuyankhula kuti ndi tsiku lotsiriza, ndipo nthawi yayandikira. Perekani madalitso awa omwe ife tikuwapempha, Atate, mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kwa ulemelero Wake. Ameni.

Mukhale pansi.

3 Ine ndikufuna kuwonjezera ichi, kuti, mwa misonkhano yonse yomwe ine ndinakhalapo nayo mmoyo wanga, Ine ndikukhulupirira kuti sabata ino yakhala nthawi yaulemelero kwambiri ya moyo wanga wonse wa utumiki. Ziribe kanthu zomwe ine nda . . . Ine ndawonapo zozizwitsa zazikulu zikuchitidwa, ndithudi, mmbuyomu, ndi misonkhano ya machiritso, koma izi ndi zoposa zimenezo. Yakhala imodzi ya nthawi zazikulu, zopambana za moyo wanga, ndizo kudzakhala pano. Ndi kuwona kachisi wamng'onoyu akutenga mawonekedwe osinthika awa; osati chokhacho, koma mkatimu mukutenga mawonekedwe osinthika!

4 Ndipo, tsopano, ine ndinali kumufunsa Billy; iye anachedwa kwambiri, kubwera kudzanditenga ine. Iye anati panali gulu lina limabatizidwa. Chimene, apitirira handiredi, sabata ino, a anthu omwe abatizidwa mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Chotero, ife tiri—tiri othokoza. Ndipo Mulungu akudalitseni inu!

5 Ndipo, tsopano, ngati inu mulibe tchalitchi kwanu, ife tikukuitanani inu kuno, kuti muzibwera ndi kudzayanjana ndi

ife. Ingokumbukirani kuti tchalitchi ichi ndi chotsegula. Ife sitiri chipembedzo, ndipo ine ndikuyembekeza ndi kudalira kuti icho sichidzakhala konse chipembedzo. Chiyanjano basi kumene amuna ndi akazi, ndi anyamata ndi atsikana, amakumana pozungulira gome la Mulungu, ndi kumayanjana pozungulira Mawu, ndipo ife tiri nazo zinthu zonse mofanana.

6 Tsopano, ndipo ife tiri naye m'busa wodabwitsa, mwamuna weniweni wa Mulungu, ndipo ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha chimenecho. Ngati mungakumbukire, masomphenya, chaka chapitacho, Chakudya chimenecho chimasungidwa kumaloko. Ndipo ndizo ndendende kulondola. Ndipo ife tiri . . .

7 Ife tiri nawo malowo tsopano, okwanira, a makalasi a Sande sukulu, a misinkhu yonse, ndipo ndife oyamikira basi chifukwa cha mwayi uwu. Ena ankanenapo, nthawi ina, ngati iwo akanangokhala ndi makalasi a Sande sukulu kumene iwo akanakhoza kumatumizako ana awo. Tsopano, inu, iwo ali nawo iwo tsopano. Kotero, tsopano, kotero inu muzingobwerabe ndi kudzakhala ndi ife ngati inu mulibe tchalitchi kwanu.

8 Chifukwa, ngati inu muli ndi tchalitchi chabwino kumene inu mumapitako, ndipo amalalikira Uthenga, zina zotero, bwanji, ndiro—ndiro basi gulu lina la ife, mukuona, kwinakwakenso. Koma ngati mulibe kwanu, ndipo inu muli . . .

9 Ine ndamva kuti ambiri anali, asamukira kuno kuchokera ku mbali zina za dziko, kudzachipanga chino kukhala tchalitchi chawo. Ndipo ife ndithudi tikukulandirani inu kuno ku Mawu a Ambuye. Ndipo ndikukumbukira, ine ndikuganiza, pamene ine ndinkachoka, ine ndinakuuzani inu kuti—kuti misonkhano, monga momwe ine zikundikhudzira, izikhalira kuno ku kachisi.

10 Ine sindikudziwabe zonse zomwe Ambuye ali nazo kwa ine mtsogolo. Ine ndikudalira izo ku dzanja Lake, osati matsenga ena kapena chirichonse. Ine ndikungodikirira basi, tsiku ndi tsiku, kuti Iye azinditsogolera ine kupita ku malo komwe ine ndingakakhoze kukakhala wotumikira wabwinoko kwa Iye. Ndipo pamene Iye adzathana nane ine, ndiye ine ndikudalira kuti Iye adzandilandira ine Kwathu, mu mtendere.

11 Ndipo, tsopano, ndine woyamikira kwambiri chifukwa cha mgwirizano wa anthu a pa kachisi. Monga Billy anali kundiuzira ine sabata ino, kuti, ine ndikuganiza, khomo lirilonse lomwe laimiriridwa pano pozungulira kachisi uyu liri ndi winawake ndi iwo. Iwo anatsegula, makomo anu ndi malo, ndipo munatengeramo anthu omwe sakanakhala nawo malo aliwonse oti apiteko. Tsopano, ndiwo machitidwe enieni a Chikhristu. Ndipo makomo ena angodzazitsamo aliyense mu ngodya yaing'ono iliyonse yomwe iwo akanakhoza, kuwapezera anthu malo oti akhalemo.

12 Chifukwa, iyi yakhala ili nthawi yovuta kwambiri, pa chifukwa cha ichi, chochitika cha mtundu winawake chomwe chakhala chikuchitika, chokhudza masewera a mdziko, mtundu wina wa basketball kapena chinachake, ndipo—ndipo kusungitsa malo kunali kutapangidwa. Kuwonjezera gulu lalikulu lochokera . . .

13 Ine ndikuganiza kuti, ayimiridwa pano mu mpingo wawung'ono uno, pafupifupi, kuzungulira maiko twente-eyiti kapena sarte akuimiridwa pomwe pano mu tchalitchi, pambali pa mafuko awiri akunja, kotero, ndi kachitsitsimutso kakang'ono aka. Kotero, izo zatenga malo okulirapo pang'ono, pazokha. Ndikudziwa za . . .

14 Ine ndimafunsa lero, ndiri ndi anthu ena. Ine ndinati, "Ine ndinamva kuti munalibe anthu ambiri a ku Jeffersonville pozungulira, mu msonkhano."

15 Winawake anayankhula, anati, "Ife tikulephera kulowa mkati." Chabwino, izo, izo zinali zimenezo. Icho chinali chifukwa chake. Ena a apolisi, ndi ena otero, amafuna kubwera ku msonkhano, koma anati, anali akuyankhula pozungulira, anati, koma iwo anabwera ndipo iwo sanakhoze kulowa mkati, kuti munali mutadzaza kale isanakwane ngakhale nthawi yomwe iwo akanalowa mkati. Kotero iwo anali nayo nthawi yawo, mwinamwake, kanthawi kena, ndipo iwo sanabwere. Kotero tsopano anthu akubwera kuchokera ku malo ena, kotero ife tiri oyamikira kwambiri.

16 Tsopano, ine sindikudziwa. Chinthu chotsatira chimene chidzatsatire izi, chidzakhala Malipenga Asanu Ndi Awiri, mu uthenga wina. Koma, mu Zisindikizo, mwakuchitika chirichonse chaphatikizidwamo. Mibadwo ya mpingo kumabwera mmusi, ndipo ife tinaiyika iyo poyamba, chomwe chinali kwambiri—chomwe chinali chofunikira kwambiri, koma . . . cha nthawi imeneyo. Tsopano, kutsegula kwa Zisindikizo kukuwonetsa kumene Mpingo ukupita, ndi momwe Iwo ukudzathera. Ndipo tsopano, ine ndikuganiza, Atate Akumwamba akhala ndithudi achisomo kwa ife, pakutilola ife kuti tiwone zomwe ife tiri nazo.

17 Ndipo ine ndikunena ichi, poyang'ana pa zolemba zakale zomwe ine ndinalalikirapo, zaka zambiri zapitazo, Ine ndinali kumangobwera mkati ndi kumanena zomwe ine ndimaganiza kuti zinali zolondola, ndi kumapitirira. Izo zimakhala kunja kwa mzere. Ndipo tsopano, zonse zinayi za Zisindikizo zimenezo, ine ndinali nazo izo mwa pafupifupi ulaliki wa maminiti-twente, zonse za izo. Okwera pa kavalo anayi, a Chivumbulutso, ine ndinaziponyera izo zonse pamodzi ndipo ndinati, "Kavalo mmodzi anapita woyera," Ine ndinati, "mwinamwake ndiwo—a—m'badwo woyambirira. Ndipo kavalo wotsatira anapita nthawi ya njala," ndiyeno nkumapitirira monga chomwecho. Koma,

mai, pamene Mawu anatsegulidwa kwenikweni, Izo zinali mailosi handiredi kutalikirana ndi izi.

18 Chotero, icho chikutikakamiza ife kuti tiyang'anire ndi kumadikirira. Ndipo mwinamwake inali yoti idzakhale nthawi iyi kuti tidzachite zimenezo. Apo pakhoza kukhala zinthu zambiri zomwe zanenedwa, zomwe zikhoza kukhala zosagwirizanika ndi anthu ena. Koma ine ndikukhulupirira kuti, pamene nthawi yaikulu yotsiriza idzabwera, ndipo tikadzakumana naye Ambuye wathu, inu mudzapeza kuti Izo zinali zolondola. Inde, bwana. Izo—Izo—Izo ndi zimenezo kwenikweni.

19 Tsopano, anthu amene ali ochokera kunja kwa mzinda, kuchokera kozungulira ku malo osiyanasiyana, abwera kuchokera ku maiko ndi mafuko osiyanasiyana, momwe ine ndikuyamikirira kudzipereka kwanu kuyendetsa mtunda wonse, ndikutenga matchuthi anu. Ndipo ena a iwo ngakhale opanda malo odzakhala! Ine—ine ndikudziwa, chifukwa ine ndakwanitsa kuthandizira ena a iwo kupeza malo oti azikhalako. Opanda ngakhale ndalama zoti azidyera, kapena china chirichonse, ndipo chotero . . . ndipo ngakhale kubwera, mulimonse, akuyembekezera kuti chinachake chichitika, kuti chidzasamalira za zimenezo. Ndipo ndi chikhulupiriro chachikulu choterocho mu zimenezo, kuti ziribe kanthu ngati iwo atamakhala opanda chakudya, kapena ngakhale malo oti azikhalapo, iwo akufuna kubwera kudzamva izo, zinthu zimenezo zikuchitika, mulimonse. Ndiko kudzipereka kwenikweni, inu mukudziwa. Ndipo aliyense wangokhala ali basi wani handiredi-peresenti!

20 Ine ndinakumana ndi mlamu wanga kumbuyo uko, yemwe anali—a . . . ankamanga tchalitchi ichi ndi njerwa, ndi zina zotero. Ndipo ndinali kumuuza iye za mmene ndimayamikirira nchito yake. Ine sindine—womanga ndi njerwa, kapena kudziwa kanthu za izo. Koma ndimadziwa momwe ngodya yowongoka imakhalira, ndipo ngati iyo yamangidwa mwa mtundu wabwino.

21 Ndipo iye anati, "ine ndikuuzani inu." Iye anati, "Sipanakhalepo nthawi yoteroyo, nkomwe, yomwe iwe unawonapo umodzi wotero pakati pa anthu, pamene iwo onse amagwirira ntchito limodzi."

22 M'bale Wood, M'bale Roberson, ndi aliyense amangoziyika mmalo awo, chirichonse. Ndipo m'bale yemwe—yemwe amayika zoyankhulira, a . . . Ine ndikutanthauza zowulutsira mawu ndi chirichonse, mu tchalitchi. Iwo anati, "Chirichonse chinangogwira ntchito mwabwinobwino." Pamene iwo asowa chinachake, pamakhala munthu atayima pamenepo kuti achite chimenecho. Kotero ndizo . . . Mulungu ali mu dongosolo lonselo. Ife ndife othokoza kwambiri chifukwa cha zimenezi.

23 Opereka mochuluka ambiri mu mpingo, kuti athandizire kuchita izi, monga M'bale wathu Dauch ndi Mlongo Dauch akhala apa, ndi ena ambiri omwe anapereka mochuluka ku ntchito iyi. Ndipo ine ndikuganiza kuti, panthawi yake yomwe, iwo sanasowe mpang'ono pomwe ndipo izo zonse zimalipiridwa. Kotero ndife oyamikira kwambiri chifukwa cha zimenezo.

24 Kumbukirani, ndi tchalitchi chanu, pakuti ndinu wantchito wa Khristu. Ndipo ndicho chimene chinamangidwira pano, khomo lotseguka kuti lidzapange antchito, ndi kwa antchito omwe ali kale antchito a Khristu, kuti azibwera ndi kumadzasangalala iwoeni pozungulira chiyanjano cha Yesu Khristu. Ndipo ife tikufuna kuti inu mudziwe kuti aliyense ndi wolandiridwa.

25 Ndipo tsopano pamene inu mundimva ine nthawizina, pansi pa nthawi ya kudzoza, ndikukhala ngati ndikung'ambira pansi katani ya bungwe, Ine—ine sindimatanthauza izo motsutsa abusa anu, kapena motsutsa m'bale aliyense, mlongo, mu mpingo. Chifukwa, kuwonjezera apo, Mulungu ali nawo anthu mu bungwe lirilonse lomwe liripo. Koma Iye samavomereza bungwelo; Iye amavomereza munthu payekha wa m'bungwelo. Ndipo a . . . Izo sizimatengera bungwe.

26 Chotero, pamene anthu akhala omangidwa kwambiri pozungulira bungwe, ndiye iwo samakhoza kuwona chinthu china chirichonse koma chokhacho basi chimene mpingo umenewo ukunena, mwaona. Ndipo icho chimapangitsa kusayanjana ndi enawo, ndipo ndi kachitidwe komwe Mulungu samakondweretsedwa nako, ndipo iko ndi kachitidwe ka dziko kosadzozedwa konse ndi Mulungu.

27 Kotero, tsopano, ine sindikutanthauza munthu aliyense payekha. Katolika, Chiyuda, chirichonse chomwe chingakhale, kapena—kapena Methodisti, Baptisti, Presbateria, bungwe lirilonse, wopanda mabungwe, ndi—ndi wopanda zipembedzo, ndi onse, Mulungu ali nawo ana Ake akukhala uko mmenemo. Mukuona? Ndipo nthawi zambiri ine ndimakhulupirira kuti iwo ali kunja uko kwa cholinga, kuti akapereke Kuwala, kukawasololamo okonzedweratu amenewo kuchokera konse kozungulirako konsekonse. Ndipo—ndipo pa tsiku lalikulu limenelo, ife tidzawona ndiye kuti, Mpingo wa Ambuye Yesu Khristu udzayitanidwira ku—ku nthawi ya kukumana kwakukulu mu mlengalenga, ndipo ife tonse tidzapita mmwamba kukakumana naye Iye. Ndipo ine ndi—ndikuyembekezera ora limenelo.

Tsopano, pali zambiri zomwe zikanakhoza kunenedwa!

28 Ndipo usikuuno, pa kutsiriza, usiku wotsekera, monga kawirikawiri, aliyense amakhalira . . . Mu msonkhano wa machiritso, ine ndimapeza, pansi pa kuyembekezera zinthu zazikulu zoti zichitidwe mu msonkhano wa machiritso, zomwe

zimawapangitsa iwo kukhala omangika, amanjenje. Ndiyeno ine ndikupeza, chinthu chomwecho usikuuno, kuti aliyense ali pansi pa kuyembekezera kuti awone momwe. . . Ndipo usiku uliwonse, wakhala uli mwanjira imeneyo, pa kutsegula kwa Zisindikizo zimenezo.

29 Tsopano ine ndikufuna kupanga ichi momveka kwenikweni. Nthawi iliyonse, nthawi iliyonse yomwe Zisindikizo izi zimabwera pa malo; chirichonse chomwe ndinkakhulupirira pa Izo, ndi zomwe ndinawerenga za anthu ena, zakhala ziri zosiyana ndi zomwe zimabwera kwa ine mchipindamo.

30 Ndipo malingaliro anga, pa nthawi ino. . . Chifukwa chomwe ine ndinakhalira ndi msonkhano wa machiritso mmawa uja, ndi chifukwa chakuti malingaliro anga aumunthu akukhala kutali kwambiri ndi momwe ndimaganizira. Ine ndayesetsa kukhala mu—mchipinda muli makatani otsitsidwira pansi, ndipo magetsi atayatsidwa. Ili ndi tsiku lachieyiti. Ndipo sindinakwere nkomwe mgalimoto yanga, ku—kuti ndipite kulikonse.

31 Ine ndinachita kupita ndi abale ena, kumusi ku mabanki, kuti ndikasainire zolemba zina ndi zinthu, za ndalama ndi zinthu zomwe zinali zitabwerekedwera tchalitchi chino. Koma ine—koma ndinabwerera molunjika kubweranso, ndipo ndinangobwereranso kumakawerenga.

32 Ndipo chinthu chachirendo, sipanakhalepo munthu mmodzi yemwe ananena chirichonse. Kapena, kawirikawiri, iwo amakhala akugogoda, ndi kumakoka, ndi kumazungulira. Sipanakhale nkomwe chinthu chimodzi. Icho chakhala chopambana kwambiri.

33 Kumene ine ndakhala ndikukadya, kwa M'bale Wood. Kawirikawiri malo amenewo amakhala atadzaza paliponse ndi magalimoto. Ndipo iwo anali oti akhala ndi anthu eyiti kapena teni osiyanasiyana amene anali oti abwera kudzakhala nawo iwo pa nthawi ino, ndipo palibe mmodzi wa iwo anabwera.

34 Ndiyeno, mmawa uno, ine sindidzauyiwala konse mmawa uno, chisomo cha Mpulumutsi wathu kwa wantchito Wake wotopa, wofooka. Pamene, ine ndinali nditayankha funso la munthu wosauka, ndipo, mwakukhoza kwa kulingalira kwanga, kumaganiza kuti ndachita cholondola. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, ngati kuti ine ndinali—ine ndinali nditalanda chinachake kuchokera kwa mwana, ine ndinali wotsutsika kwambiri, ndipo sindinadziwe chimene icho chinali. Ndipo ndinaganiza, mwinamwake pokhala kuti ine ndinali kuthamangira kukafika ku utumiki wa machiritso uja, mwinamwake winawake akudwala mosimidwa kwambiri, amene anali woti apemphereredwe pomwepo. Ndipo ine ndinafunsa osonkhana. Mu maminiti pang'ono, icho chinawululidwa. Ndipo winawake anati, "Kodi inu simuwerenga lanu—simuwerenganso phunziro lanulo?" kapena

chinachake. Ndipo nthawi imeneyo, ine ndinatenga kachidutswa kakang'ono ka pepala ndi kukawerenganso iko kachiwiri, kuwona zomwe iko kananena. Ndinayang'ana pansi pa Mabuku, ndipo izo zinali palimodzi zosiyana, funso lomwe ine ndinali kuliyankha. Mukuona?

35 Mulole ndingopereka ichi kwa inu. Pamene Chauzimu chibweramo, chimenecho ndi maganizo a Khristu. Iwe umadzakhala kutali kwambiri ndi kuganiza kwako komwe, mpaka, mmalingaliro ako omwe, ine...Ichi, inu...ine sinditi...Musati mundirole ine kuti ndiyesetse kufotokoza zimenezo, chifukwa ine sindingathe. Mukuona? Ine sindingakhoze kuchita chimenecho. Palibe aliyense angakhoze kuchita chimenecho.

36 Zinatheka bwanji kuti munthu uja, ameneyo ndi Eliya, atayima pamenepo pa phiri, pansi pa Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo anatsitsa Moto kuchokera kumwamba, ndipo kenako mvula nkugwa pambuyo pomwe pa Motowo? Ndipo kenako nkutseka miyamba, ndipo iyo siyinavumbe kwa zaka zitatu ndi miyezi sikisi, ndi kudzabwereranso ndi kukaiyitanitsa mvulayo, pa tsiku lomwelo! Ndipo pansi pa kudzoza kumeneko, momwe...Ndipo anawatengera ansembe foro handiredi kumeneko ndi kukawapha iwo; ndipo kenako nkuthawira ku chipululu, akufuula chifukwa cha moyo wake, atawopsyezedwa ndi mkazi mmodzi. Mukuona? Yezebeli, iye analumbirira kuti awuchotsa moyo wake. Pamene, Ahabu ndi onse a iwo anali kumeneko, kuti akawone Kukhalapo kwa Mulungu ndi chozizwitsa chachikulu chikuchitidwa. Mwaona, wake... Mzimu unali utamuchokera iye. Mu njira yake yachibadwa ya kaganizidwe, iye sanadziwe momwe angaganizire, mwaona. Iye sakanakhoza kuganiza mwa iyeyekha.

37 Ndipo, kumbukirani, Mngeloyo amamugonetsa iye tulo, ndi kumamupumitsa iye. Anamudzutsa iye, namupatsa iye mikate ina; kenako nkumugonetsa iye tulo, ndi kudzamupumitsa iye; ndi kumudzutsa iye, ndikudzamupatsanso iye mikate ina. Ndipo ife sitikudziwa chomwe chimachitika ndi munthuyo, kwa masiku forte. Kenako iye anakokedwera kubwerera mu mphanga, kwinakwake, ndipo Mulungu anamuitana iye.

38 Musamayesere kufotokoza icho Chauzimu. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Mukuona? Chinthu chokha choti muchite, ndicho basi kumapita chitsogolo pomwepo. Ndipo ine ndimayesetsa kudzipanga ndekha kumveka momwe ine ndingathere, koma kuchokera pano ine ndidza...ine ndikuganiza kuti sindidzayeseranso izo kachiwiri. Inu muzingokhulupirira mwamtheradi, kapena ayi. Ndipo ndiri... Inu mudzawona, patsogolo pang'ono, chifukwa chake.

Tsopano, ine ndayesetsa kukhala woona mtima. Mulungu akudziwa zimenezo.

39 Ndipo funso lija mmawa uno. Ine ndimayesetsa kuliyankha
ilo moona basi momwe ine ndimadziwira. Ine ndinangowerenga
gawo loyamba la ndimeyo, ndipo ilo linali . . . sizikanakhala
zolondola. Koma Mzimu Woyera, kumvetsa kuti ine . . .
malingaliro anga . . . Mwaona, penyani, masiku awiri kapena
atatu apitawa, chomwe chakhala chikuchitika. Mwaona,
ine—ine ndinati seveni handiredi . . . "seveni sauzande,"
seveni handiredi. Mmawa uno, ndinali kuyesetsa, ndipo icho
chinawonedwa ndi anthu, mwaona, ndipo izo zinawonetsa
kuti inu munali tcheru. Tsopano, limodzi linanso, pamene
ndimayesera kunena kuti "nkhunda," ndipo ine ndinadzaitcha
iyo mwanawankhosa; koma ine ndinachigwira icho pomwepo.
Ndipo kenako, apa, lomwe ine sindinaligwire pa chimenecho,
Mzimu Woyera unadzapotolokera mmbuyo momwe ndi
kudzandiyitanira ine kwa ilo.

40 Ndiko kutsimikizira kwapawiri kuti zinthu izi nzoona. Izo
ziri . . . Mulungu akupenyerera, kuwonetsetsa kuti Izo zikukhala
zolondola. Uko nkulondola. Iye akufuna kutero. Iye akufuna kuti
inu mudziwe kuti Icho ndi Choonadi.

41 Iye ndi Yemwe akuzitumiza Izo, chifukwa izo ndithudi
sizinali . . . Izo zinali basi kwa ine monga, kuphunzira, monga izo
zikukhalira kwa inu. Ndipo kotero ife tiri . . . ndine woyamikira
kwambiri chifukwa cha—chi—chidziwitso, kudziwa tsopano za
Ambuye, ora limene ife tikukhalamoli; mwaona, tikukhala mu
nthawi yotsiriza kumene, Mpingo usanapite. Tsopano basi . . .

42 Ife takhala tikuyankhula, kotero tiyeni tingopempha
madalitso Ake pa Mawu kachiwiri.

43 Atate athu Akumwamba, apa pakubwera usiku wopambana
uja, ora lopambana lomwe chinthu chopambana chachitika.
Icho chakhala chiri ponse pozungulira anthu. Ndipo, Atate,
ine ndikupemphera kuti usikuuno chidziwike, kupyola mthunzi
wa kukaikira, kwa mitima ya anthu ndi malingaliro, kuti iwo
akhoze kudziwa kuti Mulungu akadali pa Mpandowachifumu,
ndikuti Iye akuwakondabe anthu Ake.

44 Ndipo ndi oralo, ora lomwe dziko lakhala likuyembekezera
kuliwona, tsopano ilo likuyandikira, pakuti ilo likulirira
chiwombolo. Ife tikukhoza kuwona zipangizo zakonzeka
kulibweretsanso ilo. Ife tikukhoza kuziwona zipangizo
zakonzeka kuwubweretsa Mpingo mu Kukhalapo kwa Khristu.
Ife tikukhoza kuwona a—Mkwatibwi akutenga mawonekedwe,
akuvala chovala cha ukwati, akukonzekera. Ife tikukhoza
kuwona magetsi akuthwanima. Ife tikudziwa kuti tiri kumapeto.

45 Tsopano, Atate Akumwamba, pamene ichi chikupita
patsogolo tsopano kukalalikira, kapena kukaphunzitsa
pa chochitika chachikulu ichi, champhamvu chimene
chinachitika mu Ulemelero, zaka thuu sauzande zapitazo,
ndipo chinaperekedwa kwa mtumwi wokondedwa wamkulu,

Yohane. Ndipo usikuuno ife tiri oti tiyankhule pa Icho. Mulole Mzimu Woyera ubwere patsogolo tsopano mu Mphamvu Yake yaikulu ya vumbulutso, kuti Iye akhoze kuwulula kwa ife chinthu icho chimene Iye akufuna kuti ife tichidziwe, monga Iye wachitira mu mausiku angapo apitawa. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu, limodzi ndi Mawu, mu Dzina la Yesu. Ameni.

46 Tsopano, pamene mukufuna kuti mutsegule, mwinamwake, mu Mabaibulo anu. Ndipo iyi ndi ndime yaifupi chabe, ndime imodzi ya Lemba. Koma, iyo ndi ndime yotsiriza, iyo ikupezeka . . . Chisindikizo chotsiriza, kani.

Tsopano, usiku wathawu ife tinali kuyankhula pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi.

47 Chisindikizo Choyamba, kukhala wotsutsakhristu akuyamba. Nthawi yake inapita nidutsa, ndipo ife tinawona momwe iye anatulukira.

48 Momwe Chamoyo chimene chinawonetseredwa, pa Mphamvu ya Mulungu chimene chinapita ndi mphamvu ya wotsutsakhristu, kukamenyana nayo iyo! Ine sindikukhulupirira kuti pangakhale funso mmalingaliro a aliyense pa zimenezo.

49 Kenako ife tinadzapeza kuti, zinali mwamsanga utatha iwo, m'badwo wa mpingo umenewo, Zamoyo izo zinapita.

50 Tinadutsamo, ife tinapeza kuti, ife tinasintha, chithunzi chonsecho pamenepo, palibenso Zamoyo zomwe zinatulukira. Mukuona? Koma, uko kunali kuyambitsa, kubwera patsogolo, uko mu nthawi ya Chisautso, Mpingo utatha kutuluka.

51 Zinagwirizana mwangwiro bwanji ndi mibadwo ya mpingo! Ine sindikuwona dontho limodzi, chinthu chimodzi chimene sichinagwirizane mwangwiro, ngakhale ku mibadwo ndi chirichonse, ndi nthawi. Taganizani za zimenezo. Izo zikuwonetsa kuti, uyo anayenera kukhala Mulungu amene anachita zimenezo. Malingaliro a munthu sakanakhoza kukwanitsa zimenezo. Ndipo tsopano ife tikupeza kuti izo, nazonso, ife . . .

52 Ambuye anatilola ife kuti titenge Lemba, Lemba Loyera, chimene Yesu anati chikanadzachitika. Ndipo ife tikanachipeza bwanji icho konse? Ndipo apa, akubwerapo ndi kudzawulula, ndi kudzachibweretsa icho ndendende basi. Ulaliki Wake pamenepo, poyankha izo, akubweretsa ndendende pa nsonga, zisanu ndi chimodzi za Zisindikizozo, koma Iye analumpha Chachisanu Ndi Chiwiri. Mukuona?

53 Ndiye pamene Zisindikizo zinadzatsegulidwa, Mulungu, zindikirani apa, Iye analumpha kuwulula ngakhale chiphiphiritso chirichonse cha Chachisanu Ndi Chiwiri Icho. Mukuona? Ndicho chinsinsi changwiro ndi Mulungu. Zindikirani. Tsopano ife tiwerenga mu Baibulo, mu—

Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri. Chimene chikupezeka mu Chivumbulutso, mutu wa 8.

> *Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu ndi chiwiri, kunali chete kumwamba pafupifupi kadanga* ka theka *la ora.*

54 Ndipo ndizo zonse zomwe ife tiri nazo pa icho. Tsopano ife tizindikira.

55 Ndipo ndiyesetsa kuti ndisakusungeni nthawi yotalika kwambiri, chifukwa ambiri a inu mukhala muli pa msewu, komabe, usikuuno, mukupita kwanu. Ndipo ine ndinaganiza kenanso, zokhala ndi msonkhano wa machiritso mmawa uno, zimene zikanakulolani inu kudzapita mmawa, simukusowa kuti muzidikiriranso. Ndipo tsopano ife. . .

56 Ndipo ine, nanenso, ndiyenera kupita ku—ku Tucson, Arizona, kumene ine ndimakhala. Ndipo ndiko kwathu tsopano. Ndipo kenako ine—ine ndikufuna kuti ndidzabwererenso kuno, Ambuye akalola, cha. . .Banja likufuna lidzabwererenso kwa masiku angapo mu Juni. Ndipo, tsopano, mwinamwake ine ndidzakumana nanu inu nonse kuno, mu msonkhano pa nthawi imeneyo.

57 Utumiki wanga wotsatira wokhazikika ndi ku Albuquerque, New Mexico. Ine ndikuganiza kuti ndi pa naini, teni, ndi leveni. Ine ndidzakakhala kumeneko Lachinayi ndi Lachisanu la Isitara. Kotero, ine ndimati ndidzakhale ndi chinthu chonsecho, ndipo ine ndinali nawo malonjezo ena omwe ine sindikanakhoza kuwakwaniritsa mpaka nthawi imeneyo, kotero ine ndidzakhala ndi Lachinayi usiku ndi Lachisanu usiku, ku Albuquerque, New Mexico.

58 Ndiyeno—ndiyeno a—wotsatira, wodziwika, woyandikira, ndizo mwakungoyankhula. Ife sitikudziwa motsimikiza. Zimenezo ndi kukakhala ndi azimzanga abwino, a—a gulu la *The Midnight Cry,* ku. . .kumtunda ku Southern Pines, North Carolina.

59 Ndipo iwo ali pa foni kumeneko tsopano, chomwe, iwo atumiza matelegramu, mauthenga, ndi chirichonse, ndipo akubwera pafupi chomwechi, kwa gulu lina, ku Little Rock; la anthu a Dzina la Yesu omwe ine ndinakhala nawo pa misonkhano, cha ku Cow Palace chirimwe chathachi. Iwo akukhala ndi msonkhano wawo waukulu ku Little Rock, Arkansas. Ndipo iwo akhala, kuyambira chaka chatha, akufuna pafupifupi usiku umodzi. Kapena, akufuna wonse wa iwo, koma iwo akhoza kukhala okonzeka ngakhale kwa usiku umodzi. Ndipo kotero ine ndinawauza iwo, posadziwa basi choti ndichite, ine ndinati iwo akhoza kulengeza iwo, "mwakungoyankhula." Ndiye iwo adzawudziwitsa iwo mtsogolo pang'ono.

60 Kodi iye wangoyimba kumene? Uh-huh. Chabwino. Mukuti chiyani? [M'baleyo akuti, "Hot Springs."—Mkonzi]. Hot Springs,

ndi choncho? Ine ndimalakwitsa. ["Twente-foro."] Twente-foro wa . . . ["Meyi."] Meyi? [Winawake akuti, "Twente-foro mpaka twente-eyiti wa Juni."] Twente-foro mpaka twente-eyiti wa Juni. Tsopano izo zalengezedwa, "Mwakungoyankhula," izo ziri, "ngati chiri chifuniro cha Ambuye." Mukuona? Ndidzatero . . .

61 Apa pali chifukwa chimene ine ndimakondera kuchita zinthu zimenezo. Inu mudzaphunzira mtsogolo pang'ono, tsopano, mwaona. Pamene ine ndipita ku malo, ine ndimakonda kukapondetsa phazi langa pansi pamenepo, ndikudziwa kuti Mulungu anati, "Pita kumeneko." Ndiye ngati mdaniyo adzuka paliponsepo, ine ndimati, "Ine ndiri pano mu Dzina la Ambuye Yesu. Ingosunthira mmbuyo!" Mukuona? Mukuona? Mukuona? Ndipo ndiwe—iwe umakhala wotsimikiza, za malo ako, mwaona. Pamene Iye akutumiza iwe kulikonse, Iye adzakusamalira iwe. Mukuona? Koma ngati iwe upita, mopenekera, ndiye ine sindikudziwa; Iye akhoza kusakakhalako kumeneko. Kotero ine—ine ndimafuna kukhala wotsimikiza momwe ine ndingakhalire. Ine ndayendapo maulendo ambiri amene Iye sanandiwuze kuti ndiyende, koma ine—ine ndimakonda kukhala wotsimikiza momwe ndingathere. Ambuye akudalitseni inu nonse tsopano.

62 Tsopano, tsopano ife tikuzindikira, iyi pokhala ndime imodzi yokha apa, ife tikufuna kuchita chinachake pang'ono chabe—pang'ono pokha tisanafike apa. Inu mukuzindikira kuti, ife tinalumpha mutu wa 7. Mutu wa 6 ukutsirizitsa Chachisanu Ndi Chimodzi, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. Koma, pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, pali chinachake chimene chikuchitika. Mukuona? Ndipo momwe—momwe izo zayikidwira mokondeka basi pa malo ake oyenera, pakati pa, mutu wa 6 ndi wa 7. Tsopano inu muzindikira mu mutu wa 7, ife tikuzindikira, pakati pa Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri, pali kadanga. Kadanga, pakati, pa mutu wa 6 ndi wa 7 wa Bukhu la Chivumbulutso, ndipo ndi pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri danga ili likuperekedwapo. Tsopano ife tikufuna kuti tizindikire ichi. Ndi chofunikira kwambiri kuti ife tizindikire kanthawi kapang'ono aka.

63 Tsopano kumbukirani, utatha mutu wa 4 wa Chivumbulutso, Mpingo wapita. Pambuyo pa—okwera pakavalo anayi atatha kutulukira, Mpingo wapita. Mukuona? Chirichonse chimene chinachitika kwa Mpingo, chinachitika kufikira mutu wa 4 wa Bukhu la Chivumbulutso. Chirichonse chimene chinachitika mu kusuntha kwa wotsutsakhristu, chinapita mpaka ku mutu wa 4. Ndipo Chisindikizo Chachinayi cha Chivumbulutso, ziwiri zonse kwa wotsutsakhristu ndi Khristu, zinatha. Ndipo wotsutsakhristu akubwera ku chiwonongeko chake, ndi ankhondo ake; ndipo Khristu akubwera ndi ankhondo Ake.

64 Iyo ndi nkhondo yakale imene inayamba kale mmbuyo, kuseri kwa nthawi. Ndiyeno iwo anali . . . Satana ndi angelo ake anakankhidwira kunja, ndipo zitatero iwo anabwera pa dziko lapansi. Ndipo nkhondoyo inayambika kachiwiri, chifukwa Eva anaswa chotchingacho kuchoka kumene iye anali atabisidwa, kuseri kwa Mawu a Mulungu. Ndipo kuchokera pa ora lomwelo, Satana anapambana nkhondoyo pa Mawu a Mulungu, chifukwa mmodzi wa omumvera Ake, wofookayo, analekerera zigwiriro. Ndipo ndimo ndendende momwe iye wakhala akupambanira nkhondoyo nthawi iliyonse, zakhala ziri chifukwa mmodzi wa omumvera Ake analekerera chigwiriro kuchoka ku Mawu.

65 Ndipo izo zinachitika mu m'badwo wa mpingo wotsiriza uno, kupyolera mu kachitidwe kabungwe. Chimene, mpingo weniweni, wapachiyambi, woyera wa Mulungu wamoyo, wokhala ndi wokwera wabodza, sunakhoze kulandira Mawu, ndipo zinatembenuza mpingo kuchoka ku Mawu kupita ku mbalume.

66 Tsopano, ndi angati akudziwa kuti ndi mbalume zomwe mpingo wa Roma Katolika wamangidwirapo? Kodi iwo amavomereza zimenezo? Mwamtheradi. Zedi. Ndithudi, iwo amavomereza izo. Sindizo zonse. Akatolika, ndithudi, icho sichingapweteke kumverera kwawo nkomwe, chifukwa iwo amadziwa zimenezo. Iwo angowonjezera imodzi yatsopano, kuno osati kale kwambiri, yakuti Maria anawuka. Inu mukuikumbukira iyo, kuno zaka zingapo zapitazo, pafupifupi zaka teni. Ndi angati akukumbukira zimenezo? Pepala, kumeneko. Ndithudi. Mukuona? Chirichonse, "mbalume" yatsopano. Mwaona, zonsezo ndi mbalume, osati Mawu. Mukuona?

67 Wansembe, pa kuyankhulana posachedwapa, iye anati, "Bambo Branham," iye anati, "Mulungu ali mu mpingo Wake."

Ine ndinati, "Mulungu ali mu Mawu Ake."

Iye anati, "Ife sitiyenera kumakangana."

68 Ine ndinati, "Ine sindikukangana nanu. Ine ndikungoyankhulapo neno. Mulungu ali mu Mawu Ake. Uko nkulondola. 'Aliyense amene ati adzachotse chirichonse kwa Iwo, kapena kuwonjezera chirichonse kwa Iwo,' anatero Mawu."

69 Iye anati, "Chabwino, Mulungu anapereka . . . Khristu anawupatsa Mpingo Wake mphamvu, ndipo anawauza iwo kuti: chirichonse chimene iwo akanati adzamange pa dziko lapansi, chikanadzakhala chomangidwa Kumwamba; ndipo chiyani . . . "

Ine ndinati, "Izo ndizo ndendende Choonadi."

70 Iye anati, "Ife tiri nazo, pa . . . pa mfundo iyi, kuti ife tiri ndi mphamvu yakumasula tchimo."

71 Ndipo ine ndinati, "Ngati inu mungachite zimenezo mwanjira yomwe zinaperekedwera kwa Mpingo, ndi momwe iwo ankachitira izo, ine ndivomereza izo. Ngati inu mukutero, pali madzi apa, kuti 'mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu,' mwaona, osati winawake kukuuzani inu kuti machimo anu akhululukidwa." Mukuona? Mukuona? Ndizo ndendende.

72 Tamuwonani Petro ali ndi makiyi, pa Tsiku la Pentekoste. Kumbukirani, iye ali nawo makiyi omwe iwo amawakamba. Ndipo a—anthuwo anati, "Amuna ndi abale, tingakhoze kuchita chiyani kuti tipulumutsidwe?"

73 Petro anati, "Lapani, mmodzi aliyense wa inu, mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu" (kwa chiyani?) "kwa chikhululukiro cha machimo, ndiyeno inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezoli liri kwa inu, ndi kwa ana anu, iwo omwe ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana." Uko nkulondola. Kotero izo zikukhazikitsa zimenezo kwa nthawizonse. Izo zonse zatha. Icho chinachita izo.

74 Tsopano, koma, mukuona, wotsutsakhristu anadzabwera mmenemo, monga momwe ife tachijambulira icho ndi kuchiwonetsa icho. Ndi vumbulutso lotani! Mai, mai! Ndipo kuganiza, zaka zonse izi, ife tachiwona icho chikusunthira mmwamba. Ndipo apa chiri mwamtheradi, molunjika, PAKUTI ATERO AMBUYE.

75 Tsopano, ndipo ife tikuzindikira kadanga aka tsopano, pakati pa, mutu wa 6 ndi wa 7. Tsopano, mutu wa 7 wa Chivumbulutso, apa pali a—a...ukuwulula chochitika. Izo siziri apa kwachabe. Izo sizinayikidwemo, pakati pa izi, kwachabe. Mukuona? Izo ziri apa kwa cholinga, ndipo ndiro vumbulutso lomwe likuwulula chinachake. Zindikirani mwachinsinsi mwake ndi mwamasamu momwe zikukwanira mu Lemba kumene! Mukuona? Ndendende.

76 Kodi mumakhulupirira mu masamu a Mulungu? Ngati inu simumatero, motsimikizadi inu mwatayika mu...Inu motsimikiza mudzataika mu Mawu, ngati muyamba kumayika foro kapena sikisi, kapena—kapena chinachake, pambali pa mawu a masamu okha akuyenda mwa dongosolo. Inu ndithudi mudzakhala nazo mu chochitika chanu, ng'ombe ikudya udzu pa nsonga ya mtengo, penapake. Inu ndithudi mudzasochera. Chifukwa, Mulungu samatero...Mawu Ake onse amayenda kwathunthu mu—mu—mu masamu. Inde, bwana. Mwangwiro, mwangwiro zedi! Palibe bukhu lina lolembedwa monga Ilo, monga Ilo, langwiro chomwecho mu masamu.

77 Tsopano, a—mutu wa 8 ukuwulula kokha chochitika cha—chochitika cha Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, pamene palibe chinthu chirichonse chomwe chikuwululidwa, tsopano, chirichonsecho. Icho sichikuwululidwa mu Chisindikizo

Chachisanu Ndi Chiwiri . . . tsopano, chiribe chochita ndi mutu wa 7 wa—wa Chivumbulutso. Kuwululidwa kwake, kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, kuli chete mwangwiro. Ndipo ngati ndikanangokhala ndi nthawi . . . Ine ndiyesetsa malo angapo, kuti ndikuwonetseni inu.

78 Njira yonse mmbuyo, kuchokera ku Genesis, mutu uwu Wachisanu ndi chiwiri- . . . kapena Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi—ndi—chikunenedwachi. Kuchokera kuchiyambi komwe, mu Genesis, Chisindikizo ichi Chachisanu Ndi Chiwiri- . . .

79 Zisindikizo izi zimasunthira mmwamba kumene. Kodi simukukhoza kukumbukira, mmawawu, tikuzibweretsa zinthu izi? Ndipo penyani, usikuuno, tikuzibweretsa izo. Ndipo inu mupeza kuti, pamene izo zidzafike ku Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri icho, iye akudukiza. [M'bale Branham anakhwatchitsa zala zake—Mkonzi]. Inde.

80 Yesu Khristu, mu kuyankhula, Iyemwini, ananena za mapeto a nthawi. Ndipo pamene Iye anafika . . . Anayankhula za Zisindikizo zonse zisanu ndi chimodzi. Pamene Iye anadzafika ku Chachisanu Ndi Chiwiri, Iye anayima. Ndi zimenezotu, mwaona. Ndi chinthu chachikulu.

81 Tsopano, tsopano, ife tiyankhula apa tsopano pa mutu uwu wa 7, miniti yokha, ku—kukhala ngati kuchilumikiza icho mkati, pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri. Chifukwa, ndicho chipangizo chokhacho chomwe ife tiri nacho kuti tipitirire nacho, pakali pano, ndi Chachisanu Ndi Chimodzi . . . pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri, pali kuyitana kuti Israeli atuluke.

82 Tsopano, ndiri nawo azimzanga abwino ambiri a Mboni za Yehova amene akhala pano, ndizo zonse . . . kapena akhala ali. Mwinamwake ena a iwo akadali a Mboni za Yehova. Koma iwo nthawizonse akhala akuwayika, Bambo Russell anatero, handiredi ndi forte foro sauzande awa, kukhala Mkwatibwi wauzimu wa Khristu. Mukuona? Iwo . . . Sindiwo.

83 Izo ziribe chochita mu m'badwo wa mpingo, nkomwe. Iwo mwamtheradi ndi Israeli. Tsopano, ife tiwerenga mu maminiti pang'ono. Tsopano, kadanga aka, pakati pa Chachisanu Ndi Chimodzi . . . Zisindikizo, pali kuyitana ndi kusindikiza kwa Ayuda handiredi ndi forte-foro sauzande, oyitanidwa mu nthawi ya Chisautso, Mpingo utapita kale. Mukuona? Izo ziribe kanthu kochita ndi m'badwo wa mpingo, nkomwe. Oh, akuyitanidwa, ndipo mwangwiro mogwirizana ndi Lemba. Zaka zitatu ndi theka zotsiriza za Daniele, zoperekedwa kwa "anthu" a Daniele, mwaona, osati Amitundu. Kwa "anthu" a Daniele ndipo Daniele anali Myuda!

84 Tsopano zindikirani, Israeli, Israeli amakhulupirira aneneri ake okha, ndipo, iwo atatha kutsimikiziridwa.

85 Ndipo palibe paliponse kudutsa mu m'badwo wa mpingo, kuyambira mu Mpingo woyambirira wa atumwi, pamene mpingo wa Chiprotestanti unayamba wakhalapo naye mneneri. Ndiwuzeni ine yemwe iye anali, ndipo mundiwonetse ine zimenezo. Palibepo! Iwo anali naye, mu m'badwo woyambirira wa utumwi, mmodzi wotchedwa Agabasi, amene anali mneneri wotsimikiziridwa. Koma mu. . .Pamene Amitundu anadzabweramo, mu cholowa cha Mulungu, ndipo Paulo natembenukira kwa Amitundu. Pambuyo pa Petro, monga ife tinawerengera usiku wathawu, anali atalandira kuchokera kwa Ambuye, kuti, "Iye anali kuwatenga a—anthu kuchokera kwa Amitundu, kwa Dzina Lake, Mkwatibwi Wake," ndiye apo sipanayambe pakhalapo konse, pa masamba a mbiriyakale, mneneri wa Amitundu. Tsopano mungobwerera kudutsa mu mbiriyakale ndipo mukafufuze. Bwanji? Ndendende, izo zingakhale zotsutsana ndi Mawu. Ndendende.

86 Pamene woyamba unatulukira, unali mkango, amenewo *anali* aneneri: Mawu.

Wotsatira womwe unapita apo, unali ntchito, nsembe.

Wotsatira unabwera pamenepo, unali kuchenjera kwa—kwa munthu.

87 Koma tinalonjezedwa, mu tsiku lotsiriza, kuti izo zidzabwerera kwa Mpingo kachiwiri, kwa cholinga chodzawongola zonse zimene zinasocheretsedwa, zinaphonyedwa, zosakonzedwa, zosiyidwa osakonzedwa. Pakuti, zinanenedweratu apa kuti Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri ukanadzatsirizitsa zinsinsi za Mulungu. Ndipo, ndiye, ife tadutsa kudutsa mu zonsezo Izo. Ife tikuwona kuti Izo ziri mwangwiro mu mgwirizano ndi Lemba. Ndicho chifukwa chake.

88 Tsopano, kodi inu mungakhoze kulingalira, pamene munthu uyu akubwera powonekera? Pamene iye adzatero, kumbukirani, izo zidzakhala zonyozeka kwambiri ndi zinthuzo, mpaka mipingo idzaziphonya izo kwambiri. Ndipo kodi inu mungakhoze kulingalira, kuti mipingo, yomwe ikadali pansi pa mwambo wa okonzanso, ingamulandire nkomwe mneneri wochokera kwa Mulungu, yemwe angadzakhale wotsutsa mwamphamvu ziphunzitso zawo ndi mabungwe?

89 Tsopano, alipo munthu mmodzi yekha yemwe angakhoze kukwaniritsa chimenecho, Mzimu umodzi wokha umene unakhalapo konse pa dziko lapansi, umene ine ndikuwudziwa. Ukhoza mwina kudzakhala. . .Iye ayenera kudzakhala Eliya, mu nthawi yake. Ndipo izo zinanenedweratu kuti zikanadzachitika, womwe sikanthu koma Mzimu wa Khristu.

90 Pamene Khristu anabwera, Iye anali chidzalo. Iye anali Mneneri. Iye anali a—Mulungu wa aneneri. Mukuona? Mukuona?

91 Khristu, penyani momwe iwo anamudera Iye. Koma Iye anabwera ndendende momwe Mawu ananenera kuti Iye akanadzabwerera. Koma pokhala kuti Iye anali Mneneri, iwo anadzichitira okha mwano pochoka ku Ufumu wa Mulungu, powutcha Mzimu wa Mulungu, umene unali kuzindikira za mu mtima ndi zina zotero kuti, "mzimu woyipa." Anati, "Iye anali i—iye anali wam'bwebwe, kapena mdierekezi," chomwe chiri.

92 Wam'bwebwe ndi mdierekezi, mwaona, mzimu wa mdierekezi. Ndithudi. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Mwamtheradi. Zam'bwebwe ndi zokopera za mneneri, zomwe ziri mwamtheradi kuchitira mwano pamaso pa Mulungu.

93 Tsopano zindikirani. Kuyitanidwa, mogwirizana mwangwiro ndi Malemba, mu zaka zitatu ndi theka zotsiriza za Daniele.

94 Zindikirani, wokhulupirira wa Israeli—okhulupirira ankangowuzidwa, mu Chipangano Chakale, kuti azikhulupirira aneneri awo mneneriyo atatha kutsimikiziridwa. "Ngati patakhala mmodzi pakati panu, yemwe ali wauzimu kapena mneneri, Ine Ambuye Wa-. . . Mulungu wanu ndidzazidziwitsa Ndekha kwa iye, ndi kuyankhula kwa iye mmasomphenya, kupyolera mmaloto, kumasulira maloto." Winawake akakhala ndi loto, mneneri adzakhala wokhoza kumasulira ilo. Ndipo ngati—ngati iye ali ndi masomphenya, iye amawayankhula iwo. "Ine ndidzadzizindikiritsa Ndekha kwa iye kupyolera mu masomphenya ndi maloto, kudzizindikiritsa Ndekha. Ndipo ngati chimene iye anena chifika podzachitika, ndiye mvereni mneneri ameneyo, chifukwa Ine ndiri ndi iye. Ngati sizichitika, ndiye musamuwope iye nkomwe." Eya. Uko nkulondola. "Chokanipo, ingomusiyani iye yekha, mwaona." Tsopano ndizo. . .

95 Tsopano, Israeli nthawizonse adzakhulupirira zimenezo. Ndipo kodi inu simukuwona? Chifukwa chiyani?

Tsopano ine ndikufuna kuti inu mumvetse bwino phunziro ili, usikuuno, tsopano.

96 Chifukwa chiyani? Chifukwa, ndiro lamulo lochokera kwa Mulungu, kwa iwo. Ine sindikusamala kaya ndi timabuku tingati tomwe Amitundu angapititse kumeneko ndi kukagawa. Ine sindikusamala kaya inu mupita mochuluka chotani kudutsa mu Israeli muli ndi Baibulo pansi pa nkono wanu, mukutsimikizira *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*; iwo sadzalandira konse kalikonse koma mneneri. Ndiko kulondola ndendende. Pakuti, mneneri ndi yekhayo yemwe angakhoze kutenga Mawu Auzimu ndi kuwaika Iwo pamalo Ake, ndipo nkukhala mneneri wotsimikiziridwa. Iwo adzakhulupirira zimenezo. Uko nkulondola.

97 Pamene ine ndinali kuyankhula kwa Myuda cha kuno ku Benton Harbor, pamene John Rhyn uja, pokhala wakhungu moyo wake wonse, pafupifupi, analandira kupenya kwake. Iwo ananditengera ine kumeneko, nyumba ija ya Davide. Ndipo rabbi uyu anatulukira ali ndi ndevu zake zazitali. Iye anati, "Ndi mwa ulamuliro wanji womwe inu munamupatsira John Rhyn kupenya kwake?"

Ine ndinati, "Mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu."

98 Iye anati, "Zoti Mulungu ali ndi Mwana zikhale kutali!" Mukuona? Ndipo iye anati, "Inu anthu simungakhoze kumudula Mulungu mu zidutswa zitatu ndi kumupereka Iye kwa Myuda. Kupanga Amulungu atatu kuchokera mwa Iye; ndinu gulu la achikunja!"

99 Ine ndinati, "Ine sindimamudula Iye mu zidutswa zitatu." Ine ndinati, "Rabbi, kodi icho chingakhale chinthu chachirendo kwa inu kuti mukhulupirire kuti mmodzi wa aneneri anu ananena zimenezo . . . chinachake cholakwika?"

Iye anati, "Aneneri athu samanena kanthu kolakwika."

Ine ndinati, "Ndi ndani yemwe Yesaya 9:6 ankamukamba?"

Iye anati, "Mesiya."

100 Ine ndinati, "Ndiye, Mesiya adzakhala Mneneri-Munthu. Ndi kulondola uko?"

Anati, "Inde, bwana. Uko nkulondola."

101 Ine ndinati, "Ndiwonetseni ine pamene Yesu anaphonya izo." Iye anati . . . Ine ndinati, "Ndi ubale wanji womwe Mesiya-Mneneri ati adzakhale nawo kwa Mulungu?"

Iye anati, "Iye adzakhala Mulungu."

Ine ndinati, "Uko nkulondola. Tsopano inu mukuzimvetsa izo pamutu."

102 Kotero ndithandizeni ine, Myuda ameneyo atayima pamenepo ndipo misonzi yake ikutsikira mmasaya mwake, anati, "Ine ndidzakumvani inu nthawi ina mtsogolo."

Ine ndinati, "Rabbi, inu mumakhulupirira zimenezo?"

103 Ndipo iye anati, "Penyani," iye anati, "'Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kuwukitsa ana kwa Abrahamu.'" Ine ndinadziwa kuti iye anali mu Chipangano Chatsopano.

Ine ndinati, "Kulondola, Rabbi! Tsopano nanga bwanji zimenezo?"

104 Iye anati, "Ngati ine nditalalikira zimenezo, ine ndingakakhale kumusi uko," inu mukudziwa kumene malo awo ali pa phiri kumeneko, "kumusi uko mu msewu, ndikupemphetsa chakudya changa."

105 Ine ndinati, “Ine kuli bwino ndikakhale ndiri kumusi uko ndikupemphetsa chakudya changa.” Myuda akadali ndi manja ake pa ndalama, inu mukudziwa. Mukuona? Mukuona? “Ine kulibwino . . . ” Ndi dzina lake mu golide, pa . . . ine ndinati, “Ine kulibwino ndikakhale ndiri kumusi uko, ndikudya zitumbuwa zamchere ndi kumamwa madzi a mngalande, ndikumadziwa kuti ine ndiri mu chiyanjano ndi Mulungu, ndi woona; kuposa kuti ine ndikhale ndiri kuno ndi dzina langa pa nyumba imeneyo, mu zolemba za golide monga choncho, ndi kumadziwa kuti ine ndiri kutali ndi Mulungu. Ine nkumadziwa zimenezo.” Iye sanamvetserenso kwa ine, kotero iye analowa mkati.

106 Koma ndi zimenezo. Inu simungakhoze kumudula Mulungu pawiri kapena mzidutswa zitatu, zotchedwa “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ndi kupanga Amulungu atatu ndi kuzipereka izo kwa Myuda. Lamulo lake lomwe ndilakuti, “Iwe sudzakhala nayo milungu ina patsogolo pa Ine. Ine ndine Yehova Mulungu wako.” Kodi Yesu ananena chiyani? Yesu anati, “‘Mverani inu, O Israeli, Ine ndine Ambuye Mulungu wanu, Mulungu mmodzi.’” Osati atatu; inu simungapereke konse zimenezo kwa iwo. Ayi. Palibe mneneri yemwe angayankhule konse za Amulungu atatu. Ayi. Palibe. Inu simudzamva konse za izo. Ayi, bwana. Izo ndi zachikunja monga komwe izo zinachokera. Inde, bwana.

107 Zindikirani. Koma aneneri awa adzabwera. Osati icho chokha . . . A—aneneriwo, tsopano, ndi Chivumbulutso 11. Ife tawerenga zina za izo. Ndipo ine ndikufuna kuti muziwerenge izo pamene inu mukuphunzira, pa matepi ndi zina zotero. Iwo mwamtheradi ndi aneneri otsimikiziridwa, mwa chizindikiro cha aneneri. Zikatero Israeli adzawamvera iwo.

108 Tsopano, kwa inu, amzanga a Mboni za Yehova, mvetsani tsopano kuti awa, handiredi ndi forte-foro sauzande, alibe chochita ndi Mkwatibwi. Palibe chidutswa chimodzi cha Lemba choti chigwirizane ndi zimenezo. Ayi, bwana. Iwo siali. Iwo ndi Ayuda. Osankhidwa omwe akuyitanidwa mu nthawi ya zaka zitatu ndi theka zotsiriza za masabata sevente a Daniele. Tsopano ndizo . . .

109 Ine—ine ndikumabwerezabe izi. Osati mochuluka kwambiri kwa inu nonse muli pano, koma, mukuona, anthu, matepi awa akupita konsekonse, mukuona. Ndipo inu mumvetse zimenezo. Inu mukandimva ine ndikubwereza. Ndi chifukwa cha cholinga chimenecho.

110 Zindikirani. Tsopano mukuona momwe iwo ankayenera, kuchititsidwa khungu, inu mukuona momwe iwo ankayenera . . . ? Yesu, kapena, Mulungu anachita kuwachititsa khungu Ayuda, kuwaletsa iwo kuti asamuzindikire Yesu. Ngati iwo akanadziwa, ngati iwo akanadziwa kokha kuti izo . . . Powona chizindikiro chimene Iye anachita, ngati iwo akanakhala pamalo awo olondola, monga iwo

ankachitira kumbuyo uko pansi pa lamulo pamene Mulungu ankawalamulira iwo za mneneri, ndipo anali atamuwona Yesu akuchita zimenezo, iwo akanati, "Uyu ndi Mesiya." Chifukwa chiyani zinali chomwecho?

111 Iwo a mu m'badwo umenewo, omwe maina awo anali atalembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, atumwi Ake ndi ena otero, iwo anachiwona icho ndipo anachizindikira icho.

112 Ndi chifukwa chiyani ena onse a iwo sanatero? Mwaona, iwo anachititsidwa khungu. Iwo sakanakhoza kuchiwona icho. Iwo sakuchiwona icho, panobe. Ndipo iwo sadzachiwona icho mpaka iye atabadwa monga fuko, pa nthawi imodzi. Izo sizingakhoze . . .

113 Mawu sangakhoze kulephera. Kumbukirani, Mawu sangakhoze kulephera. Sindikusamala kaya inu muli nazo zogirigisha zingati, ndi zonse zomwe zingachitike, komabe Mawu amenewo sangakhoze kulephera. Izo zidzakhala ndendende mwanjira yomwe Mulungu anati izo zinakhalira. Mukuona? Tsopano, ife tikuzindikira kuti zinthu izi ziyenera kuchitika.

114 Ndipo ndicho chifukwa chake iwo sanamuzindikire Yesu pamene Iye anadzizindikiritsa Yekha mwangwiro kuti anali Mneneri.

115 Ngakhale wamng'ono—mkazi wamng'ono uja wa Chisamariya atayima pamenepo pa chitsime. Iye anali asanafikepo mu Samariya; Iye anangopita kumeneko, anati Iye anali nako kusowa koti adzere njira imeneyo, ndipo Iye anapita kumeneko. Ndipo kumeneko kunali mkazi wamng'ono uja. Ndipo iye, mu chikhalidwe chake, iye anali mu chikhalidwe chabwinoko kuti alandire Uthenga kuposa ansembe achipembedzo amenewo ndi zinthu za tsiku limenelo. Iye anachita zimenezo. Ndithudi. Tsopano, mukuona?

116 Koma, pamaso pa kukana kwawo konse, komabe mmodzi wa anthu olemekezeka awo anavomereza kuti iwo ankadziwa kuti Iye anali Mphunzitsi wotumidwa kuchokera kwa Mulungu.

117 Ine ndinali kuyankhula kwa mmodzi wa madokotala abwino kwambiri amene alipo ku maiko a kummwera, mu ofesi yake, osati kale kwambiri. Katswiri wabwino kwambiri mu Louisville, mwamuna wochirimika kwenikweni. Ndipo ine ndinati kwa iye, ine ndinati, "Adokotala, ine ndikufuna ndikufunseni inu funso."

Iye anati, "Chabwino."

118 Ine ndinati, "Ine ndinawona chizindikiro chanu chachipatala, wogwira ntchito. Inu muli ndi njoka yokulungidwa pa mtengo. Kodi chimenecho chikuyimira chiyani?"

Iye anati, "Ine sindikudziwa."

119 Ndipo ndinati, “Icho chimaimira ichi: icho chinali choyimira cha machiritso Auzimu, pamene Mose ankakwezera mmwamba njoka yamkuwa mchipululu, mwaona, chomwe chinali chiphiphiritso chabe, chiphiphiritso chabe cha Khristu woona.”

120 Tsopano, lero, mankhwala ndi chiphiphiritso cha machiritso Auzimu. Ndipo ngakhale ambiri a iwo samakhulupirira zimenezo, madokotala abwino enieni amakhulupirira zimenezo. Koma ena a iwo samakhulupirira zimenezo. Koma choyimira chawo chomwe chimene iwo ali nacho chimachitira umboni ku Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse, kaya iwo akufuna kukhulupirira izo kapena ayi. Mukuona? Uko nkulondola. Apo pali njoka ya mkuwa itapachikika pa mtengo, pa chizindikiro cha zachipatala.

121 Tsopano zindikirani Ayuda awa. Tsopano, mamba a khungu anali pa maso a anthu awa. Iwo, iwo sakanakhoza kuchitira mwina; iwo anali pamenepo, ndipo Mulungu anawayika iwo pamenepo. Ndipo iwo ali pamenepo mpaka m’badwo umene iwo analonjezedwa, aneneri akudza awa. Inu mukhoza kutumiza mamishonare, inu mukhoza kuchita chirichonse chomwe inu mukufuna kuchita; Israeli sadzatembenuka konse mpaka aneneri awa atadzabwera powonekera, ndipo izo zidzachitika ukadzachitika Mkwatulo wa Mpingo wa Amitundu.

122 Chimodzimodzinso m’badwo wa ng’ombe sukanakhoza kulandira kuyitana kwa mkango, pakuti Mulungu wanena mu Mawu Ake kuti Mzimu wa ng’ombe unatulukira. Ndipo mu m’badwo wa okonzanso, munthu anatulukira. Mukuona? Inu basi . . .

123 Ndicho chinthu chokhacho chimene inu . . . iwo akhoza kulandira. Ndicho . . . Ndipo, mmenemo tsopano, iwo anachititsidwa akhungu. Ndizo basi zonse zomwe ziripo kwa izo. Tsopano zindikirani.

124 Koma m’badwo ukubwera pamene nthawi idzakhala itatha kwa Amitundu. Pali mtengo, ndi mizu yake unali Wachiyuda, ndipo iwo unadulidwapo; ndipo Amitundu anamezanitsidwa mmenemo, “wakuthengo, mtengo wa azitona,” ndipo iwo ukubereka chipatso chake. Tsopano, pamene Mkwatibwi wa Amitundu ameneyo adzadulidwapo, mtengo wa Mkwatibwi uja umene ine ndinawukamba, ndipo nkudzatengedwera mmwamba mu Kukhalapo kwa Mulungu; Mulungu adzawasesera Amitundu osakhulupirira amenewo, cha kuno kumbali (anamwali ogona), ndi kuwamezanitsanso kachiwiri. Iye analonjeza kudzachita zimenezo.

125 Ndipo kufikira nthawi imeneyo, iwe ukungoyenera kudziwa komwe uli . . . Ngati ukudziwa kumene ukupita, chabwino, zabwino. Ngati sukudziwa, bwanji, iwe ukupunthwa mu mdima.

126 Tsopano, apo ndi pamene Ayuda ati adzatembenuzidwe, mu m’badwo umenewo. Tsopano, monga m’badwo wa mpingo,

pansi pa mphamvu ya lonjezo lodzozedwa, iwo adzalandira Khristu; koma, tsopano, osati pamene Amitundu akadalipobe. Tsopano ife tikhoza kuwona mtundu wa uthenga womwe aneneri awiri awa, a Chivumbulutso mutu wa 11, ati adzalalikire. Tsopano inu momveka mukhoza kuwona ndendende chomwe iwo ati adzachite. Pakuti, otsalirawo, kapena handiredi ndi forte-foro sauzande, okonzedweratu, adzalandira Chisindikizo cha Mulungu.

127 Tiyeni tingowerenga. Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano. Tsopano ine ndikufuna kuti inu muwerenge ndi ine, ngati mungakwanitse, chifukwa ine ndilozera mmbuyo kwa izi mwa pang'ono pokha, Mutu wa 7, tsopano, izi ndi pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri.

> . . . *zitachitika zinthu izi—zitachitika zinthu izi* (Zisindikizo izi) . . .

128 Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chinamasulidwa, ndipo ndiyo nthawi ya Chisautso. Aliyense akumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chinamasulidwa, ndipo Chisautso chinali chitayambika. Zitatha izi, chiyani?

> . . . *zitachitika zinthu izi ine ndinawona angelo anayi atayima pa ngodya zinayi za dziko lapansi, akugwira mphepo zinayi za dziko lapansi, kuti* iyo *isawombe* pa *dziko lapansi, kapena pa nyanja, kapena pamtengo uliwonse*. (Angelo anayi!)
>
> *Ndipo ndinawona mngelo wina akutsika kuchokera kummawa, ali nacho chisindikizo cha Mulungu wamoyo: ndipo iye anafuula ndi liwu lalikulu kwa angelo anayiwo, kwa omwe kunapatsidwa kuti awononge* nyanja, *dziko lapansi . . . nyanja,*
>
> *Akuti, Musawononge dziko lapansi, ngakhale nyanja, kapena mitengo,* mpaka *ife titasindikiza antchito* . . .

129 Osati Mkwatibwi. "Antchito." Osati ana. "Antchito." Israeli nthawizonse wakhala ali antchito a Mulungu. Mpingo ndi ana, mwaona, mwa kubadwa. Israeli ndi wantchito Wake. Penyani, malo aliwonse, zimakhala chomwecho nthawizonse. Abrahamu anali wantchito Wake. Ife si antchito. Ndife ana, ana aamuna ndi aakazi. Eya.

> . . . cha . . . *cha Mulungu wathu mu* mphumi *zawo*.

130 Tsopano penyani.

> . . . *Mulungu wathu pa* mphumi *zawo*.
>
> *Ndipo ndinamva chiwerengero cha iwo* omwe *anasindikizidwa:* . . .

131 Tsopano ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwatcheru ku kuwerenga kwa iwo.

. . . ndipo apo anasindikizidwa handiredi ndi forte foro sauzande a mafuko onse a ana a Israeli.

132 Iye akuwatchula iwo mwangwiro. Tsopano, ngati pangapezeke Muisraeli-Wachibritish wozindikira zamumtima wa wakhala pano, mvetserani momwe izi zikuchotsera mphepo kuchokera mwa izo, mwaona.

A fuko la Yuda anasindikizidwa thwelovu sauzande. (Analitchula, "fukolo.") *A fuko la Rubeni anasindikizidwa thwelovu sauzande. A fuko la Gadi . . . thwelovu sauzande.*

133 Penyani anu—penyani mafuko anu tsopano.

Ndipo *a fuko la Asa anasindikizidwa thwelovu sauzande. . . . fuko la Nefitali anasindikizidwa thwelovu sauzande. . . . fuko la—la Manase . . . thwelovu sauzande.*

Ndipo *fuko la Simeoni . . . anasindikizidwa thwelovu sauzande. A fuko la—la Levi anasindikizidwa thwelovu sauzande. A fuko la Isakara . . . thwelovu sauzande.* (Isakara, ine ndikuganiza kuti inu mumatchula chomwecho.) *. . . thwelovu sauzande.*

. . . fuko la Zabuloni . . . thwelovu sauzande. Ndipo *fuko la Yosefe anasindikizidwa thwelovu sauzande. Onse* a . . . *A fuko la Benjamini anasindikizidwa thwelovu sauzande.*

134 Tsopano, alipo mafuko thwelovu, thwelovu sauzande kuchokera mu fuko. Thwelovu kuchulukitsa ndi thwelovu . . . ndi chiyani? [Osonkhana akuti, "Handiredi ndi forte-foro sauzande."—Mkonzi]. Handiredi ndi forte-foro sauzande. Tsopano penyani. Awo anali, onsewo, a mafuko a Israeli.

135 Tsopano penyani, "Zitatha izi . . . " Tsopano apa pakubwera gulu lina. Tsopano, Mkwatibwi wapita, ife tikudziwa zimenezo. Koma liyang'aneni gulu ili lomwe likubwerapo.

Zitachitika izi ine ndinawona, ndipo, taonani, unyinji wawukulu, womwe palibe munthu akanawuwerenga, wa mafuko onse, . . . mitundu, ndi anthu, ndi lirime, *anayima pamaso pa mpandowachifumu, ndi pamaso pa Mwanawankhosa, atavekedwa* mu *mikanjo yoyera, ali ndi kanjedza* mdzanja *lawo;*

Ndipo anafuula ndi liwu lokweza, akuti, Chipulumutso kwa Mulungu wathu yemwe wakhala pa mpandowachifumu, ndi kwa *Mwanawankhosa.*

Ndipo mafuko *onse . . . anaimirira* pozungulira *mpandowachifumuwo, ndi pozinga* akuluwo *ndi zamoyo zinayizo, ndipo anagwa pa nkhope zawo*

pamaso pa mpandowachifumu, ndipo anapembedza Mulungu,

Akuti, Ameni: Madalitso,. . . *ulemelero,. . . nzeru,. . . mathokozo,. . . ulemu,. . . mphamvu,. . . mphamvu, zikhale* kwa *Mulungu wathu kwa nthawi za nthawi. Ameni.*

Ndipo mmodzi wa akuluwo. . .

136 Tsopano iye ali pamaso pa akuluwo apa. Monga, ife tamuwonera iye, monse kupyola mu Zisindikizo.

Ndipo mmodzi wa akuluwo anayankha, kunena kwa ine, Awa ndi ndani. . .

137 Tsopano, Yohane, pokhala Myuda, anawazindikira anthu ake omwe. Iye anawawona iwo mmawonekedwe a fuko. Nkulondola uko? Iye anawazindikira ndipo anatchula lirilonse la mafukowo.

138 Koma tsopano, pamene iye akuwawona awa, iye akukhala ngati akudabwa. Ndipo mkuluyo akudziwa zimenezo, kotero iye akuti:

. . . Kodi *awa ndi ndani omwe avekedwa mu mikanjo yoyera? ndipo iwo* akuchokera *kuti?*

139 Yohane, akuyankha tsopano:

Ndipo ine ndinanena kwa iye, Bwana, inu mukudziwa.

140 Yohane sankawadziwa iwo, mwaona; mitundu yonse, malirime, ndi mafuko.

. . . *Ndipo iye ananena* kwa *ine, Awa ali—iye anati* kwa *ine, Awa ndi iwo omwe* atuluka *kuchokera mu chisautso chachikulu*, (mwa kuyankhula kwina, Chisautso chachikulu), *ndipo atsuka mikanjo yawo,. . . ayipanga iyo kuyera mu magazi a Mwanawankhosa.*

Chotero iwo ali *pamaso pa mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo akumutumikira iye usana ndi usiku mu kachisi wake: ndipo* iwo. . . *iye yemwe* anakhala pa *mpandowachifumu adzakhala pakati pa iwo.*

Iwo sadzamvanso njala, ngakhalenso kuti iwo *sadzamva ludzu nkomwe; ngakhale dzuwa silidzawalira pa iwo—dzuwa silidzawala pa iwo, kapena kutentha kulikonse.*

Pakuti Mwanawankhosa yemwe ali pakati pa mpandowachifumu adzawadyetsa iwo, ndipo adzawatsogolera iwo ku akasupe amoyo a madzi: *ndipo Mulungu adzapukuta. . . misozi yonse mmaso mwawo.*

141 Tsopano ife tikutsegula. . . tikufika ku Chisindikizo.

Kodi inu munazindikira, iwo anali . . . Poyamba, ife tikuyamba tsopano, ndi Israeli.

142 Ndipo kenako ife tikuwona mpingo woyeretsedwa, osati Mkwatibwi; mpingo woyeretsedwa, ndi Chisautso, mwaona, mwaona, ukubwera apa, chiwerengero chachikulu cha mitima yodzipereka kwenikweni yomwe ikubwera kuchokera ku—ku Chisautso chachikulu. Osati Mpingo; Iwo wapita, Mkwatibwi. Ndi uwo mpingowo.

143 Tsopano ife tikupeza kuti, uko patsogolo pang'ono, Yesu ananena kuti Mpandowachifumu udzakhazikitsidwa, ndipo womwe . . . iwo adzayima mu chiweruzo, aliyense.

144 Tsopano, ife tikupeza tsopano kuti anthu awa anasindikizidwa ndi Chisindikizo cha Mulungu wamoyo (nkulondola uko?), Ayuda awa. Kodi Chisindikizo cha Mulungu wamoyo ndi chiyani?

145 Tsopano, ine sindikumutcha aliyense, kupweteka kumverera kulikonse. Ine ndikungonena, mwaona. Kodi inu mukudziwa, kuti, nditawerenga zambiri za ophunzira omwe analemba pa izi, amanena kuti gulu ili apa, lotsukidwa-mmagazi, ndiro kwenikweni Mkwatibwi?

146 Kodi inu mumadziwa kuti ophunzira ambiri amanenanso kuti handiredi ndi forte-foro sauzande ndi Mkwatibwi? Chiyani a . . . Pali chinachake chimene chikuyenera kukwanira apa, cholakwika . . . apa molondola, chifukwa apo pali chinachake cholakwika tsopano.

147 Zindikirani, abale athu a Adventisti amanena, kuti, "Chisindikizo cha Mulungu, ndi kusunga tsiku la sabata." Inu mukudziwa zimenezo. Koma ine ndikufuna chidutswa chimodzi cha Lemba cha zimenezo, kuti chiwonetse kuti sabata, kapena kusunga tsiku la sabata, ndi Chisindikizo cha Mulungu. Mukuona? Ndi winawake chabe anangojambula lingaliro limenelo.

148 Koma ngati mungawerenge Aefeso 4:30, iyo imati, "Musawukhumudwitse Mzimu Woyera wa Mulungu, womwe inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku lomwe inu . . . la chiwombolo chanu," inde, bwana, pamene ntchito ya umkhalapakati yatha, ndipo inu mwabwera; Khristu akubwera kudzawombola Ake Omwe. Inu mwasindikizidwa; osati kufikira chitsitsimutso chotsatira. Pamene munasindikizidwa kamodzi ndi Mzimu Woyera, ndi ntchito yotsirizidwa, kuti Mulungu wakulandirani inu, ndipo palibe kuchoka kwa icho.

149 Inu mukuti, "Chabwino, ine ndinali nawo Iwo, ndipo ine ndinatayika." Ayi, inu—inu munalibe Iwo.

150 Mulungu anati Iwo umapitirira mpaka ku Tsiku la Chiwombolo. Tsopano, uh-huh, inu mukungotsutsana naye

Iye, ndipo inu mukuwona chomwe chikutanthauza. "Mpaka Tsiku la Chiwombolo chanu."

151 Zindikirani. Monga panali . . . Monga panali otsalira malingana ndi kusankha, Ayuda awa tsopano ndi otsalira malingana ndi kusankha. Mmasiku a utumiki woyamba wa Eliya kwa Ayuda, pamene okhulupirira seveni sauzande anayikidwa pambali ndi dzanja la Mulungu, tsopano alipo mu nthawi ya otsalira iyi, akubwera ku nthawi yawo, adzakhalapo handiredi ndi forte-foro sauzande malingana ndi kusankha. Iwo, Uthenga pa nthawi imeneyo, oti adzakhulupirire Uthenga, adzakhalapo handiredi ndi forte-foro sauzande.

152 Tsopano, inu mukuti, "Oh, tsopano miniti yokha, m'bale, ine sindikudziwa za chinthu cha 'kusankha' ichi. Chabwino, ine sindinaziwerenge izo pamenepo."

153 Chabwino, tsopano tiyeni tiwone ngati ziri zolondola, kapena ayi. Tiyeni titsegulenso ku Mateyu, ndipo tifike pamusi apa ndi kukapeza ngati ife sitingakhoze kupeza kakang'ono kenakake pa izi penapake. Ine ndikukhulupirira tsopano kuti ine ndikulondola. Ine sindinalembe izo apa, koma changobwera chabe ku malingaliro anga. Tiyeni titenge, pa mapeto, ndime ya 30; pamene ife tinapitapo usiku watha, pamapeto pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, pa ndime ya 30. Tsopano tiyeni tiwerenge zimenezo ndipo tiwone tsopano pamene ife tikufika, ndime ya 31. Mukuona? "Iwo adzamuwona Mwana wa munthu akubwera mu ulemelero." Tsopano ndime ya 31.

> *Ndipo iye adzatuma angelo ake ndi kuwomba kwakukulu kwa lipenga, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi osankhidwa ake kuchokera ku mphepo zinayi, kuchokera ku mathero amodzi a kumwamba mpaka kwa enawo.*

154 "Osankhidwa" adzatulukira. Ndi chiyani chimenecho? Ndipo nthawi ya Chisautso. Mulungu adzaitana osankhidwa Ake, ndipo amenewo ndi Ayuda pa nthawi imeneyo, osankhidwawo. Baibulo likuyankhula za zimenezo. Paulo akuyankhula za zimenezo, "Molingana ndi kusankha." Padzakhala handiredi ndi forte-foro sauzande molingana ndi kusankha, omwe ati adzakhulupirire Uthenga, kuchokera mwa kwenikweni mamillioni omwe ati adzakakhale kumeneko.

155 Analipo mamillioni mu Palestina, mmasiku a uneneri wa Eliya, ndipo seveni sauzande anapulumutsidwa kuchokera mwa mamillioni.

156 Tsopano, "molingana ndi kusankha." Kumene, mamillioni a Ayuda akusonkhana ku dziko la kwawo. Ilo ladzakhala fuko. Kudzakhala mamillioni kumeneko, koma handiredi ndi forte-foro sauzande okha "osankhidwawo" adzatengedwa. Iwo adzamva Uthenga.

157 Chinthu chomwecho chiri mu Mpingo wa Amitundu. Muli Mkwatibwi, ndipo Iye ndi wosankhidwa. “Ndipo iye adzayitanidwa malingana ndi kusankha.” Zindikirani, izi zonse zikuimira Mpingo, mwangwiro, okhulupirira osankhidwa.

158 Enawo sakukhulupirira. Iwe ukhoza kungodziwa izo. Iwe ukamuwuza munthu Choonadi, ndi kulola kuti icho chitsimikiziridwe mwa Mawu, ndipo kenako nkuwonetseredwa; iye nkuti, “Ine sindikukhulupirira Icho.” Iwe ukhoza basi . . .

159 Usalimbane nazonso izo konse. Yesu ananena kuti musamatero. Anati, “Ziri ngati basi kuponyera ngale pamaso pa nkhumba.” Mukuona? Anati, “Ingowasiyani iwo okha. Iwo adzatembenuka ndi kukuponderani inu pansi pa mapazi awo. Iwo adzakusekani inu. Ingochokanipo ndi kuwasiya iwo. ‘Ngati wakhungu atsogolera wakhungu . . .’”

160 Ine ndinapita kwa munthu, osati kale kwambiri, kapena, iye anabwera kwa ine, kani. Iye anakhala akutsutsa, kuzungulira konseko, konsekonse, akutsutsa machiritso Auzimu. Ndipo anadzabwera, ndipo iye anati, “Ine sindimakhulupirira machiritso ako Auzimu.”

161 Ine ndinati, “Anga, ine ndikuganiza, sangakhale ndi ubwino uliwonse, chifukwa ine ndiribe aliwonse.” Ndipo iye . . .ine ndinati, “Koma a Mulungu ndi angwiro.”

Iye anati, “Kulibe chinthu choterocho.”

162 Ine ndinati, “Iwe wachedwa kwambiri kunena zimenezo, mzanga. Eya, iwe wachita—iwe wazidikirira zimenezo nthawi yaitali kwambiri. Iwe ukanayenera kutsutsa, zaka zingapo zapitazo, koma pabwera m’badwo wina tsopano. Alipo mamillioni oti achitire umboni, mwaona.” Ine ndinati, “Ndiwe—iwe wachedwa kwambiri tsopano, mzanga, kuti unene zimenezo.”

163 Iye anati, iye anati, “Chabwino, ine sindikukhulupirira zimenezo; ine sindikusamala zomwe iwe ungachite.”

Ine ndinati, “Ndithudi ayi. Iwe sungakhoze kutero.” Mukuona?

164 Iye anati, “Undikanthe ine ndi khungu!” Anati, “Ngati iwe uli nawo kwenikweni Mzimu Woyera, monga Paulo,” anati, “undikanthe ine ndi khungu.”

165 Ine ndinati, “Ine ndingachite bwanji izo pamene iwe uli kale wakhungu?” Ine ndinati, “Atate ako akuchititsa iwe khungu kwa Choonadi.” Ine ndinati, “Iwe, ndiwe wakhungu kale.”

166 Ndipo iye anati, “Ine sindingakhulupirire; ine sindikusamala chomwe iwe ungakhoze kuchita, umboni wochuluka motani umene iwe ungakhoze kutsimikizira, kapena chirichonse chonga icho. Ine sindikukhulupirirabe zimenezo.”

167 Ine ndinati, "Ndithudi. Izo sizinali za kwa osakhulupirira. Izo zinali za kwa okhulupirira okha. Ndi zimenezotu." Mukuona?

168 Chinali chiyani chimenecho? Mwaona, iwe umadziwa pomwepo, kuti kusankhidwako palibepo. Basi osapusisika nazo izo, nkomwe. Yesu anachita chinthu chomwecho, Iye anati, "Asiyeni iwo okha. Ngati wakhungu atsogolera wakhungu, kodi onsewo sagwera mu dzenje?"

169 Koma pamene Iye anabwera kwa hule wamng'ono, [M'bale Branham akukhwatchitsa zala zake—Mkonzi]. chimenecho chinayatsa moto! Chinali chiyani chimenecho? Iyo inali mbewu yosankhidwa itagona mmenemo, mwaona, yomwe inachiwona Icho pompano. Pamene Icho chinabwera kwa Petro, umo munali mbewu yosankhidwa ikugona mmenemo, mwaona, ndipo iwo anachiwona Icho. "Ndipo onse omwe Atate anandipatsa, anatero" (zochitika kale) "anandipatsa Ine, iwo adzabwera. Iwo adzabwera kwa Ine." Oh, mai! Ine ndimazikonda zimenezo! Inde, bwana. Zindikirani, okhulupirira amakhulupirira Zimenezo.

170 Osakhulupirira sangakhoze kukhulupirira Zimenezo. Chotero, tsopano, ngati aliyense afuna kutsutsa za mbewu ya serpenti ndi zinthu, ndipo iwe nkuyesetsa kuti uwawonetse iwo, iwo nkusamvetsera kwa Izo; ungochokapo. Ungowasiya iwo okha. Mwaona, Mulungu samatsutsana, ngakhalenso ana Ake.

171 Zindikirani, Ayuda wani handiredi ndi forte-foro sauzande osankhidwa a Mulungu sadzagwadira kwa chirombo, zachipembedzo zake, kapena mafano, kapena chirichonse, ngakhale fuko lawo liti lidzapange pangano ndi iwo pa nthawiyo. Israeli ali mu pangano, koma apa pali handiredi ndi forte-foro sauzande omwe sadzachita zimenezo. Ndiwo osankhidwawo.

172 Chinthu chomwecho chiri komwe kuno mu Mpingo wa Amitundu tsopano, ndiro gulu losankhidwa. Inu simungawakokere iwo mu zinthu za mtundu umenewo. Iwo sangakhulupirire zimenezo. Ayi, bwana. Pamene Kuwala kuwakhudza iwo kamodzi, izo zimakhazikitsa izo pomwepo. Iwo amawona . . . amaziwona izo zikuchitika, kenako nkuziwona izo zikuwonetseredwa ndi kutsimikiziridwa monga chomwecho. Ndipo iwo amayang'ana pansi apa mu Baibulo, kuwaona Mawu amenewo akumangopita. Chabwino, inu basi—inu basi mukhoza kungosiya kumapusisidwa ndi iwo, chifukwa iwo amakhulupirira Zimenezo. Ndizo zonse. Ndizo zonse. Ngakhale iwo sangakhoze kuzifotokoza Izo, koma iwo amadziwa kuti ali nazo Izo. Chotero, monga ine ndimati, pali zinthu zambiri zomwe ine sindingakhoze kuzifotokoza, koma ine—ine ndimadziwa kuti ndi zenizeni mulimonse. Uh-huh. Chabwino.

173 Nthawi iyi inali pakati pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi ndi Chachisanu Ndi Chiwiri, yomwe Iye akuwaitana

anthu awa, zoyankhulidwa ndi Yesu mu Mateyu mutu wa 24 ndi ndime ya 31, zimene tangowerenga kumene, mwaona. Malipenga apa, mboni ziwirizo za. . . Pamene lipenga likuwomba, ndiro lipenga la mboni ziwiri za m'badwo wa chisomo kwa Ayuda. Kuwomba kwa lipenga limodzi, inu mukuzindikira, kuwomba kwa lipenga limodzi. Iye anati Iye adzawomba lipenga. Tsopano zindikirani cha apa, ya 31.

> *Ndipo iye adzatumiza angelo ake* (osati mmodzi, mwaona; alipo awiri a iwo) *ndi kuwomba kwakukulu kwa lipenga,. . .*

174 Ndi chiyani chimenecho? Pamene Mulungu akukonzekera kuti ayankhule, pamakhala kuwomba kwa lipenga. Limenelo nthawizonse limakhala Liwu Lake. Ndiko kuyitanira ku nkhondo, mwaona. Mulungu akuyankhula. Angelo awa adzatulukira ndi kuwomba kwa lipenga.

175 Ndipo kodi inu munazindikira, pa Uthenga wa mngelo wotsiriza, lipenga likuwomba. Uthenga wa mngelo woyamba, lipenga linawomba; wa mngelo wachiwiri, lipenga linawomba, pamene Iye anawutumiza iwo. Zindikirani, koma pamene Zisindikizo zinalengezedwa, izo zonse zinali mu chinthu chimodzi, Chauzimu, kuti chikaitanire lituluke gulu la anthu; panali lipenga limodzi lomwe linawomba, ndipo Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zinamatulidwa.

176 Zindikirani, "Kusonkhanitsa Ayuda Ake osankhidwa kuchokera kumadera anayi a miyamba."

177 Iye anatchula Zisindikizo zisanu ndi chimodzi, monga ife tawonera, koma osati Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri. Iye sananene konse kanthu umu kokhudza Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, paliponse.

178 Mwaona, pomwepo, pa ndime ya 32, akutembenukira ku mafanizo, a nthawi ya kuyitana kwa Ayuda osankhidwa. Tsopano penyani apa, mwaona.

179 "Ndipo Iye adzatuma angelo ndi lipenga, ndi kukasonkhanitsa Osankhidwa kuchokera ku ngodya zinai za kumwamba." Tsopano Iye akuyamba. . .

180 Mwaona, Iye sakunena kanthu kokhudza Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri apa. Mukuona? Iye anayankhula za Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi; Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, Chachinayi, Chachisanu, ndi Chachisanu Ndi Chimodzi.

181 Koma zindikirani:

> *Tsopano phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu; Pamene* nthambi zake *zidakali zanthete, ndipo zikuphukira masamba*, inu *mumadziwa kuti dzinja liri pafupi:*

*Chotero momwemonso inu, pamene inu mudzawona zinthu zonse izi, mudzadziwe kuti iyo ili pafupi, ngakhale pa*khomo.

182 Lotsiriza lija, funso lija lomwe iwo anamufunsa Iye, "Ndipo chidzakhala chiyani chizindikiro cha mapeto a dziko lapansi?"

183 "Pamene inu mudzawona Ayuda awa . . . Pamene inu mudzawona zinthu zina izi zikuchitika, inu mudzadziwa chomwe chikuchitika. Tsopano, pamene inu mudzawawona Ayuda awa . . . " Akuyankhula kwa Ayuda! Tsopano penyani. Ndi gulu lanji lomwe Iye akuyankhula nalo, Amitundu? Ayuda! Ayuda! Mukuona?

184 Tsopano Iye anati, "Inu mudzadedwa ndi mafuko onse chifukwa cha Dzina Langa," ndi zina zotero, monga chomwecho.

185 Tsopano, "Pamene," Iye anati, "inu mukadzawawona Ayuda awa akuyamba kuphukira masamba awo kutsidya uko," pamene Israeli uyo akuyamba kubwerera kwawo, kubwera ku dziko lake. Pamene iye adzakafika kumeneko, (Mpingo udzakhala utakonzeka kuti Ukwatulidwe), pali zaka zitatu ndi theka zokha zomwe zatsalira kufikira kutha kwa dziko lakale, ndipo ilo likupita mu chisokonezo, ndipo umo mudzabwera Zakachikwi, kwa latsopano—dziko latsopano. Anati, "Ngakhale pakhomo!" Tsopano, zaka wani sauzande pa dziko lapansi ndi tsiku limodzi chabe kwa Mulungu. Ndipo zaka zitatu ndi theka, zingakafike kuti izo? Mphindi zochuluka kwambiri, mu nthawi ya Mulungu. Ndi chifukwa chake Iye anati, "Iyo ili pakhomo."

Indetu Ine ndinena kwa inu, kuti, *M'badwo uwu* sudzatsirizika, kuthana nawo, anthu awa, mpaka *zinthu zonse izi* zitatero . . .

186 Chiyani, ndi chiyani chomwe sichidzathetsedwa? Iwo ayesetsa kuti amuphe Myuda, kumuchotsa pa dziko lapansi, nthawi zonse. Iwo sadzakhoza konse kuti achite zimenezo.

187 Koma zindikirani. M'badwo kumene wa Ayuda umene unawona kubwererako, kubwerera ku Palestina, m'badwo umenewo udzawona zinthu izi zikuchitika. Ndipo zaka ziwiri chabe zapitazo, iye anali mwathunthu atakhala fuko, ali ndi ndalama zake zake ndi chirichonse. Iye ali kumeneko.

188 Tsopano ife tiri pati, mzanga? Zisindikizo ndi chirichonse zikutseguka; tsopano ife tikuzipeza izi pakati apa. Ndi izo kumeneko. Mwaona pamene ife takhala?

189 Ine ndikuyembekeza kuti inu mukumvetsa Zimenezo. Ine ndiribe maphunziro. Ine ndikudziwa chomwe ine ndikuchikamba, koma mwinamwake ine sindingathe kufotokoza—kuchifotokoza Icho, kuti chimveke bwino kwa inu. Koma ine ndikuyembekeza kuti Mulungu awatenga Mawu amene asakanizidwa, ndi kuwagawa iwo molondola, mwaona, ndi kukulolani inu kudziwa chomwe Icho chiri. Chifukwa,

ndizo, ife tiri pakhomo. Ife tiri apa pa nthawiyo. Tsopano zindikirani.

190 Mwaona, nthawi yomweyo tsopano, Iye akutembenukira kwa Ayuda awa, ndi pa—nthawi yotsiriza. Iye akunena zomwe ziti zidzachitike. Ife tikudziwa ngakhale zimenezo tsopano. . . Ife tikudziwa, tikuzindikira bwino, kuti mafukowo ndi omwazikana. Iwo akhala ali, kwa zaka twente-faivi handiredi. Iwo analoseredwa kuti adzamwazikana ku mphepo zinayi. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Ife tikudziwa zimenezo.

191 Chifukwa, ife sitichita kubwerera mmbuyo ndi kukatenga, kukatenga zimenezo, chifukwa ine ndiri nacho chinachake apa chofunika kwenikweni chomwe ine ndikufuna kuti inu muchiwone, musanafike potopa kwambiri, ndipo ine ndisanafooke.

192 Zindikirani. Ife tikudziwa, kuti ngakhale fuko lirilonse, uwo ndi mndandanda wa mafuko, kapena chirichonse chomwe inu mukufuna kuchitchula icho, kapena mibadwo, kapena malo a mafuko, salinso nkomwe pamodzi. Iwo amwazikana, konsekonse.

193 Ayuda, akusonkhana ku Yerusalemu, sikuti. . . Iwo sakudziwa nkomwe mafuko awo. Iwo alibe nkomwe mbendera za mafuko kapena chirichonse. Zonse zomwe iwo akudziwa, ndiye, nzakuti iwo ndi Ayuda. Iwo analoseredwa kuti akanadzakhala mwanjira imeneyo, padziko lonse. Tsopano, mabuku awo anawononged wa. Iwo sakudziwa.

Iwe ukati, "Ndiwe wa fuko liti?"

"Ine sindikudziwa."

"Fuko liti?"

"Ine sindikudziwa."

194 Wina wochokera kwa Benjamini, wina wochokera kwa *ili*, ndipo wina wochokera kwa *ilo*. Iwo sakudziwa kumene iwo akuchokera. Mabuku awo anawononged wa, mu nthawi ya nkhondo, ndipo kwa zaka twente-faivi handiredi. Chinthu chokhacho chimene iwo akuchidziwa ndi chakuti, iwo ndi Ayuda. Ndizo zonse. Kotero, iwo akudziwa kuti abwerera ku dziko la kwawo. Iwo komabe. . . Zindikirani, ngakhale iwo sakudziwa mafuko awo, koma Mulungu akudziwa.

195 Ine ndikungozikonda zimenezo! Inu mukudziwa, Iye mpaka anati pali. . . "Tsitsi lirilonse la pamutu panu linawerengedwa." Hum! Zindikirani, Iye samataya kanthu. "Ine ndidzaliwukitsa ilo kachiwiri pa tsiku lotsiriza."

196 Ngakhale iwo ataya zawo—zawo—mbendera zawo za fuko, ndi *yemwe* ali, ndipo kaya iwo ali a *ili* kapena *ilo*; iwo sakudziwa kaya iwo ndi ochokera kwa Benjamini, kapena kaya iwo ndi ochokera kwa Rubeni, kapena—kapena Isaka, kapena kumene

iwo akuchokera. Koma, mulimonse, Mulungu akuwatchula iwo apa.

197 Tsopano zindikirani, mu Chivumbulutso 7, ife tikuwerenga izi. "Thwelovu sauzande" a fuko lirilonse, mwa osankhidwa, kuchokera mwa onse a iwo. Alipo thwelovu sauzande kuchokera mu fuko lirilonse, omwe ali osankhidwa, ndipo ayikidwa pomwe apa mu dongosolo. Oh, mai! Kodi iwo ndi chiyani? Iwo ali mu dongosolo la fuko. Komabe, iwo siali tsopano, koma iwo adzakhala ali. Iwo ali mu dongosolo la fuko. Nchiyani chiti chidzakhale mu dongosolo la fuko? Osati Myuda wamba, ayi. Koma iwo omwe ali osankhidwa, handiredi ndi forte-foro sauzande, adzayikidwa mu dongosolo la fuko. Oh, mai!

198 Momwe ine ndikanakondera kukuwonetsani inu! Ife sitipita mu zimenezo. Koma ndicho ndendende chimene Mpingo uyenera kukhala, uh-huh, mu dongosolo kumene.

199 Tsopano ine ndikufuna kuti inu mupenyetsetse mwatcheru kwenikweni ndipo muwerenge nane, kwa miniti. Tsopano apa pali chinachake chomwe mwinamwake inu simunachizindikire konse mu a—kutchula kwa fuko. Ine ndinakuuzani inu, kanthawi kapitako, kuti muwerenge Chivumbulutso 7. Muwerenge ndi ine, ndipo mupenye mafuko amenewo. Mu Chivumbulutso 7, Dani ndi Efraimu akusowa ndipo sanawerengedwe limodzi ndi iwo. Kodi inu munazindikira zimenezo? Yosefe ndi Levi analowetsedwa m'malo mwawo. Kodi inu munazindikira zimenezo? Dani ndi Efraimu sali pamenepo. Ayi, bwana. Koma, Yosefe ndi Levi analowezedwa mmalo mwa—mwa—mwa Dani ndi Efraimu.

200 Chifukwa chiyani? Iwo . . . Mulungu wokumbukira nthawizonse amakumbukira lonjezo lirilonse la Mawu Ake. Oh, ndikufuna ndidzalalikire pa zimenezo. Mukuona? Mulungu samaiwala kanthu, ngakhale zimawoneka ngati.

201 Monga Iye anamuuzira Mose. Israeli anali ali kumusi uko, "zaka foro handiredi." Koma iwo ankayenera kupita uko nthawi imeneyo. Iye anamuuza Abrahamu, "Ndipo mbewu yake ikanadzakhala ikuyenda mdziko lachirendo kwa zaka foro handiredi, kenako Iye akanadzawatulutsa iwo ndi dzanja lamphamvu." Koma ndiye Iye anati kwa Mose, "Ine ndakumbukira lonjezo Langa, ndipo Ine ndabwera pansi kuti ndidzapange zomwe Ine ndinanena."

202 Mulungu samaiwala. Iye samaiwala matemberero Ake, komanso Iye samaiwala madalitso Ake. Koma, lonjezo lirilonse limene Iye analipanga, Iye amakhala nalo ilo.

203 Apa pali chifukwa chomwe iwo akusowera, tsopano, ngati inu mungayang'ane. Tsopano werengani. Ine ndikufuna inu muwerenge ndi ine tsopano. Mupite ku Deuteronome, wa twente- . . . mu ndime ya 29 mmenemo, kapena mutu wa 29, kani. Apo pali chifukwa chomwe mafuko awa

sakupezekera pamenepo. Chirichonse chiri nacho chifukwa chake. Deuteronome ife tikufuna kuti titenge a—mutu wa 29 wa Deuteronome. Tsopano, Ambuye chotero atithandize ife, kuti ife tikhoze kumvetsa tsopano. Tsopano ife tikufuna kuti tiyambire mu Deuteronome, mutu wa 29, pa ndime ya 16. Tsopano mvetserani. Mose akuyankhula.

> *(Pakuti* inu *mukudziwa momwe ife takhalira mdziko la Igupto; ndi momwe ife tinabwerera kudutsa mmafuko amene* ife *tinawadutsa;*
>
> *Ndipo inu mwawona zoyipa, ndi mafano awo, mitengo . . . miyala, siliva . . . golide, zomwe zinali pakati pawo:)*

204 Aliyense ankanyamula kenakake kakang'ono kapena china, fano laling'ono la Cecilia Woyera. Inu mukudziwa, chinachake chonga icho, mwaona. "Kuti chotero . . . " Mvetserani.

> *Kuti pasakhale munthu pakati panu mwamuna, . . . mkazi, kapena banja, kapena fuko, yemwe mtima wake utembenukire kutali tsiku ili kuchoka kwa* Ambuye *Mulungu wathu, nkupita ndi kukatumikira milungu ya mafuko awa; kuti pasakhale pakati panu muzu wakubala ndulu ndi mwavi;*
>
> *Ndi kuchitika kuti, pamene iye amva mawu a themberero ili, kuti iye—kuti iye azidzidalitsa iyemwini mu mtima wake,* ndi kunena, *ine . . . ndiri nawo mtendere, ngakhale ndingayende mu kulingalira kwa mtima* wanga womwe, . . .

205 Mwaona, anthu amati, "Oh, iye amadzidalitsa yekha." Inu mukudziwa, kupanga kamtanda kakang'ono kapena chinachake, monga iwo amachitira tsopano, mukuona; chinthu chomwecho, mwaona. Ndipo inu mukuwona ndiko kachitidwe kachikunja, mwaona, ziri ngati achikunja.

> . . . *iye* amadzidalitsa *yekha mu mtima mwake* momwe, . . . *kulingalira* kwake komwe mmalingaliro mwake momwe, *kuti awonjezere kuledzera kwa ludzu:*

206 "Zimwani basi, izo sizimapanga kusiyana kulikonse; bola ngati mukumapita ku tchalitchi, inu muli bwino bwino."

> Ndiye *Ambuye sadzamulekerera iye, komano mkwiyo wa Ambuye . . . nsanje yake idzafuka momutsutsa munthu ameneyo, ndi* a *matemberero onse omwe alembedwa m'buku ili* ("Musachotse Mawu amodzi kwa Ilo, kapena kuwonjezera amodzi kwa Ilo," mwaona.) *adzagona pa iye, ndipo Ambuye adzafufuta* lake . . . *adzafufuta dzina lake pansi pa kumwamba.*

207 Ndizo pamene iye ali pano pa dziko lapansi, mwaona, "pansi pa kumwamba."

Ndipo Ambuye adzalekanitsa kwa iye *choipa kuchokera ku mafuko onse a Israeli, malingana ndi* themberero *lonse la pangano* lomwe *lalembedwa mu bukhu ili la chilamulo:*

208 Chotero, "Ngati munthu aliyense adzatumikira fano, kapena kusunga fano pa iye, kapena kudzidalitsa yekha mwa kulingalira kwake komwe kwa malingaliro ake, ndi kutumikira mafano," Mulungu anati, "mwamuna, mkazi, banja, kapena fuko, dzina lake lidzafutidwa kwathunthu, kuchotsedwa pakati pa anthu." Tsopano, nkulondola uko? Nzoona bwanji!

209 Kupembedza mafano kunachita chinthu chomwecho mu mpingo, zaka zapitazo, ndipo kukuchita lero. Ndipo ine ndikuzindikira...Penyani momwe wotsutsakhristu anayesetsera kupanga kusuntha-kotsutsa. Ndi angati akudziwa kuti mdierekezi amafanizidwa ndi kufanana ndi—ndi oyera a Mulungu?

210 Ndi chiyani—tchimo ndi chiyani? Ndiro chinthu cholondola chopotozedwa. Kodi bodza ndi chiyani? Ndiro choonadi chonenedwa mokhota. Chigololo ndi chiyani? Ndi kachitidwe kolondola, kachitidwe kovomerezedwa, katachitidwa molakwika. Mukuona?

211 Tsopano, poyesera kuchita izi, "akufufuta dzina," kodi inu munazindikira mu m'badwo wa mpingo, chirombo chomwecho chomwe chimatumikira mafano a anthu akufa, ndi zina zotero, chinayesetsa kufufuta Dzina la Ambuye Yesu Khristu, ndi kupereka maudindo monga Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Chinthu chomwecho, ndi themberero ilo kuseri kwa icho, monga chomwecho.

212 Dani ndi Efraimu anachita kumene zimenezo, pansi pa chinyengo cha mfumu mu Israeli, wonamizira, Yeroboamu. Tsopano, zindikirani, mu Mafumu Woyamba mutu wa 12. Ine ndikudziwa kuti ife tiri...Izi, kwa ine, izi—izi—izi zikuyika maziko pa chomwe ife tikhoza kudalirapo, chomwe ife tikuchiwona. Mafumu Woyamba, ine ndikufuna kuti ndipite ku mutu wa 12, ndime ya 25 mpaka kukafika ya 30.

Ndiye Yeroboamu...Sekemu mu phiri la *Efraimu, ndipo anakakhala* kumeneko; *ndipo anapita* mu... *ndipo anakamanga Penueli.*

Ndipo tsopano *Yeroboamu anati* kwa...*mu—mu mtima mwake,* (mukuona, zolingalira za mu mtima mwake), *Tsopano ufumuwu* udzabwerera *ku nyumba ya Davide:*

213 Iye ankayamba kuchita mantha, mukuona, chifukwa anthuwo akanakhoza kuchokako.

Ngati anthu awa adzapita uko kuti...akapereke nsembe mnyumba ya Ambuye ku Yerusalemu, pamenepo

mtima wa anthu awa udzatembenukira *kachiwiri* kwa *ambuye, ngakhale* kwa *Rehoboamu mfumu ya Yuda, ndipo iwo adzandipha ine, ndi kupita*. . . kwa *Rehoboamu—Rehoboamu mfumu ya Yuda.*

Potero mfumu inapanga lingaliro, ndipo anapanga ng'ombe ziwiri za golide, ndipo ananena kwa iwo, Ndi zolemetsa kwa inu kuti muzipita ku Yerusalemu: taonani, milungu yanu*, O Israeli, yomwe inakutulutsani inu*. . . *kuchokera ku dziko la Igupto.*

Ndipo iye anayika mmodzi mu Beteli, ndipo winayo anamuyika mu Dani.

Ndipo chinthu ichi chinadzakhala *tchimo: pakuti anthu ankapita kukapembedza pamaso pa ameneyo, ngakhale* ku *Dani.*

214 Mwaona, Efraimu ku Beteli, ndi Dani, ndipo iwo anayikako mafano. Ndipo awa ankapita kukapembedza izi.

215 Ndipo apa ife tiri, mmusi momwe mpaka mu m'badwo wa Zakachikwi, pafupifupi, ndipo Mulungu akulikumbukirabe tchimo limenelo. Iwo sakuwerengedwa nkomwe mmenemo. Hey! Ulemelero! Motsimikiza basi monga Iye amakumbukirira lonjezo lirilonse labwino, Iye amakumbukira choyipa chirichonse, nachonso. Tangokumbukirani, pamene. . .

216 Ndi chifukwa chake ine ndimakhulupirira, amzanga, ine nthawizonse ndayesetsa kukhala ndi Mawu amenewo, ziribe kanthu kaya Iwo awoneka achirendo chotani.

217 Mwaona, tsopano, iwo sankaganiza za icho nthawi imeneyo kumeneko. Iwo sankaganizira za icho nthawi imeneyo. Iwo ankaganiza, "Chabwino, iwo zawathera bwino zimenezo." Chabwino.

218 Koma apa iwo ali cha apa mu m'badwo wa Zakachikwi uwu akudzalowamo, pamene maina awo ndi mafuko "zinafutidwamo" kuchoka pamenepo, chifukwa iwo anatumikira mafano, omwe Mulungu anawatemberera.

219 Kodi Iye sananene kuti Iye "ankadana" nacho Chinikolai ndi Yezebeli uja? Muzikhala kutali ndi zimenezo. Kodi Iye sananene kuti Iye akanadzapha ana aakazi a Yezebeli ndi kupha kwa "imfa," komwe kuli kulekana Kwamuyaya kuchoka ku Kukukhalapo Kwake? Musamadalire mwa zimenezo, nkomwe. Chokaniko kwa izo. Kotero, Mulungu amakumbukira. Zindikirani.

220 Koma kodi inu munazindikira pamenepo, ilo linali loti "lidzafutidwe"? Chifukwa chiyani? Pansi pa Kumwamba panalibe Nsembe ya nthawi yomweyo imene ikanakhoza kumupatsa iye Mzimu Woyera, kuti imulole iye kuti awone zinthu izi. Koma iye anachita icho, mulimonse, mmalingaliro ake omwe odzikonda.

221 Koma, Ezekieli, mmasomphenya ake, mu Zakachikwi, iye akudzawawonanso iwo kachiwiri mu dongosolo langwiro. Ezekieli, ngati inu mukufuna kuwerenga izo. Ingolembani izo, ndipo inu mukhoza kukawerenga izo, posunga nthawi. Ezekieli 48:1 mpaka 7, ndiponso mukawerenge 23 mpaka 29. Ezekieli anawona fuko lirilonse liri ndendende basi mu dongosolo. Chabwino.

222 Ndipo, penanso, mu Chivumbulutso 14, Yohane anadzawawona iwo kachiwiri ali mu dongosolo la mafuko, uko nkulondola, fuko lirilonse pamalo ake. Chinachitika ndi chiyani?

223 Inu mukukumbukira, Iye anati, "Pansi pa miyamba, kuti dzina lake likanadzafutidwa pa chochitika cha fuko." Bola ngati iye anali pansi pa miyamba, sakanadzapezekanso pamenepo. Ndipo handiredi ndi forte-foro sauzande awa ali pansi apa mu gawo la fuko, apobe. Kulondola. Koma, inu mukuona, iwo anali atachititsidwa khungu. Iwo anangokhala ndi nsembe za ng'ombe ndi mbuzi zokha. Mukuona? Tsopano zindikirani, Iye anawafufuta iwo, "pansi pa kumwamba."

224 Koma Amitundu, mmasiku a Mzimu Woyera, kudzawutsutsa Iwo; dzina lako limachotsedwa kwathunthu kuchoka mu Bukhu la Moyo, "ndipo sukanadzakhoza konse kudzakhala ndi chikhululukiro, mdziko lino kapena mdziko liri nkudza." Nkulondola uko? Kotero apo ndi pamene ife tikuyima.

225 Israeli, pansi pa mbuzi, nkhosa, iwo—iwo anali nawo malo. Bola ngati iwo anali pa dziko lapansi pano, mafuko awo anali kusowa. Iwo sakanakhoza konse kuphatikizidwapo. Tsopano, onse. . . Pamene Iye ankawatchula iwo, cha uko, handiredi ndi forte-foro sauzande, iwo anali akusowa. Uko nkulondola. Iwo sakuwerengedwa nkomwe mmenemo. Ndipo Yosefe ndi Levi ayikidwa mmalo a Dani ndi Efraimu. Tsopano inu mukhoza kuyang'ana pa zimenezo. Pomwe apo izo ziri, patsogolo panu, mwaona. Ndipo apa pali lonjezo la Mulungu, kumbuyo uko, mahandiredi ndi mahandiredi a zaka izo zisanachitike.

226 Tsopano, chinachitika ndi chiyani? Iwo anayeretsedwa mu nthawi ya Chisautso chowopsya.

227 Tsopano, ngati Mulungu ati adzamuyeretse uyo—namwali uyo, yemwe anali mkazi wabwino, koma iye anangolephera kupeza mafuta mu nyali yake, ndipo Iye adzamuyeretsa iye kupyolera mu kuzunzidwa kumeneko. Iye akuwayika mafuko amenewo mkati uko, chifukwa cha chinthu chomwecho, ndipo akuwayeretsa iwo mu nthawi ya Chisautso. Chifukwa, uko ndi a—kuyeretsa. Ndi chiweruzo. Koma, inu mukuona, iwo, zitachitika. . . Ndipo, tayang'anani apa, apa pakubwera handiredi ndi forte-foro sauzande, kutachitika kuyeretsa kwa Israeli. Ndipo apa pakubweranso namwali wogona,

akubwerapo, atayeretsedwa, ndipo wavala mikanjo yoyera. Mukuona? Zangwiro bwanji! Ndizokongola bwanji izo!

228 Chimodzimodzi monga Yakobo, mu nthawi ya vuto, mwaona. Iwo . . . Yakobo, mu nthawi ya vuto. Iye anali atachita cholakwika. Koma iye anadutsa kupyola mu nthawi ya kuyeretsa chifukwa iye anali atamulakwira m'bale wake, Esau. Mukuona? Iye anamunyenga, kuti atenge ufulu wake woyamba kubadwa. Koma iye anadutsa kupyola mu kuyeretsa asanakhale nako kusinthidwa kwa dzina lake kuchoka kokhala Yakobo nkudzakhala Israeli, chomwe chiri choyimira cha dongosolo la Mulungu, kuyimira lero.

229 Tsopano, ife titsegula tsopano ku ndime ya 8 ya, kapena, ndime ya 1, ine ndikutanthauza, ya mutu wa 8; wa Chivumbulutso 8:1.

230 Ine ndikudziwa kuti inu mwatopa. Koma, tsopano, tangoyesetsani kuti mumvetsere kwa maminiti pang'ono okha tsopano. Ndipo, Mulungu wa Kumwamba atithandize ife, ndiro pemphero langa.

231 Ife tiyenera kukumbukira kuti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi ndicho mapeto a nthawi, ya zinthu zonse. Uko nkulondola. Zinthu zomwe zinalembedwa mu Bukhu Losindikizidwa Kasanu Ndi Kawiri, losindikizidwa, la dongosolo la chiwombolo kuchokera pamene maziko a dziko lapansi anali asanakhazikitsidwe, chidutswa chirichonse chikutsirizika. Icho ndi mathero; icho ndi mathero a dziko lovutikira. Icho ndi mathero a chirengedwe chovutikira. Icho ndi mathero a chirichonse. Mmenemo, muli mathero a Malipenga. Ndi mathero a Mbale. Ndi mathero a dziko lapansi. Ndi . . . Ndipo mpaka mathero a nthawi.

232 Nthawi ikutha. Baibulo linanena chomwecho. Mateyu, mutu wa 7 . . . ine ndikutanthauza, Chivumbulutso, mutu wa 7- . . . mutu wa 10 ndi a . . . ndipo ndime ya 1 mpaka ya 7. Nthawi ikutha. Mngeloyo anati, "Sipadzakhalanso nthawi," pamene icho, mmasiku akuchitika kwa chinthu chachikulu ichi.

233 Chirichonse chikutha, mu nthawi iyi, mathero a—a . . . pamathero a Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi. Zindikirani. Ndi mathero a m'badwo wa mpingo. Ndi a—mathero a Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri. Ndi mathero a Malipenga. Ndi mathero a Mbale, ndipo ngakhale mathero a kulowetsamo kwa Zakachikwi. Zimenezo ziri pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri.

234 Izo ziri ngati kuponyera chombo mu mlengalenga. Ndipo chombo chimenecho chimaphulika *apa*, ndipo chimapita mmwamba ndipo kenako chimadzaphulikanso. Icho chimatulutsa nyenyezi zisanu. Imodzi ya nyenyezi zimenezo imaphulika ndi kuphulitsira kunja nyenyezi zisanu kuchokera mwa iyo; ndiyeno imodzi mwa nyenyezi zimenezo imaphulika

ndi kukankhira kunja nyenyezi zisanu kuchokera mwa iyo. Mwaona, izo zimangozimiririrabe nkutha.

235 Ndicho, chimene, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri chiri. Icho chikungotsirizitsa nthawi ya dziko lapansi. Icho chikutsirizitsa nthawi ya *ichi*. Icho chikutsirizitsa nthawi ya *icho*. Icho chikutsirizitsa nthawi ya *ichi*. Icho chikutsirizitsa nthawi. Chirichonse chinangotsirizira pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri chimenecho.

236 Tsopano, Iye achita motani izo? Ndicho chimene ife sitikuchidziwa. Sichoncho? Ife sitikudziwa.

237 Mpaka kuti iyo ndi nthawi ya zinthu zonse izi, ndi kulowetsedwamo kwa Zakachikwi.

238 Zindikirani, kumatulidwa kwa Chisindikizo ichi kunali kwakukulu kwambiri, mwakuti, Kumwamba kunachititsidwa bata ndi Icho, "kukhala chete, kwa danga la theka la ora." Tsopano, Icho nchachikulu! Ndi chiyani Icho? Munachititsidwa bata, Miyamba. Uko kunalibe kanthu komwe kanasuntha, kwa theka la ora.

239 Tsopano, theka la ora mwinamwake silingakhale lalitali ngati inu mukukhala ndi nthawi yabwino. Koma, mu chikhalidwe cha pakati pa imfa ndi Moyo, zinawoneka ngati kuti ndi Zakachikwi. Icho chinali chachikulu kwambiri!

Yesu sanachitchule konse Icho. Palibe aliyense wa enawo.

240 Yohane sakanakhoza ngakhale kulemba za Icho. Ayi, iye analetsedwa kuti alembe *apa*. Mwaona, pangokhala chabe . . . chabe . . . Iye sanachilembe Icho, koma ili ndi bata.

241 Ndipo akulu twente foro amene anayima pamaso pa Mulungu, Pamenepo, akuyimba ndi azeze awo; iwo anasiya kuyimba azeze awo.

Angelo anasiya kuyimba kwawo, Kumwamba.

242 Taganizani! Akerubi oyera ndi Aserafi, amene Yesaya anawawona mu kachisi, ali nawo asanu ndi limodzi . . . kapena maseti atatu a mapiko. Atatu . . . Awiri pa nkhope yake, ndipo awiri pa mapazi ake, ndi kumawuluka. Ndipo iye ali usana ndi usiku, pamenepo, pamaso pa Mulungu, akuyimba, "Woyera, woyera, woyera, ndi Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse!" Ndipo ngakhale pamene iwo akulowa mkati, kapena kulowa mu kachisi, nsanamira za kachisi zinkasuntha, ndi kwawo—kukhalapo kwawo.

243 Ndipo Aserafi oyera awa anakhala chete. Angelo anasiya kuyimba. Uh-huh. Psyii! Akuwuluka mu Kukhalapo kwa Mulungu, akuyimba, "Woyera, woyera, woyera," Iwo anatseka pakamwa. Kunalibe Angelo oyimba. Kunalibe matamando. Kunalibe—kunalibe utumiki wa paguwa. Kunalibe, kalikonse. Uko kunali chete; bata, bata la imfa Kumwamba, kwa theka la ora.

244 Khamu lonse la Kumwamba linali chete kwa theka la ora ili, pamene chinsinsi cha Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi mu Bukhu la Chiwombolo chinatsegulidwa. Taganizani za zimenezo. Koma, Icho chamatulidwa. Mwanawankhosa akuchimatula Icho. Inu mukudziwa chiyani? Iwo anadabwa nacho Icho, ine ndikukhulupirira. Iwo samadziwa; apo Icho chinali! Iwo anangoyima.

245 Bwanji? Ndi chiyani Icho? Tsopano, palibe aliyense wa ife akudziwa. Koma, ine ndiri—ine ndikuuzani inu, mwa langa—mwa vumbulutso langa la Icho.

246 Ndipo, tsopano, ine si wotentheka. Ngati ine ndiri, ine sindikudziwa za icho, mwaona. Ine ndiri. . . ine sindimatengeka ndi kwa zoterozo monga zotengeka ndi zinthu zongolingalira.

247 Ine ndanenapo zinthu zina, zomwe mwina zakhala ziri zonga ngati zachirendo kwa anthu ena. Koma pamene Mulungu abwera pozungulira, kuseri kwa Icho, ndi kudzachitsimikizira Icho ndi kunena kuti Icho ndi Choonadi, ndiye awo ndi Mawu a Mulungu. Mukuona? Icho chikhoza kuwoneka mwachirendo, mwanjira imeneyo. Mukuona?

248 Ndipo tsopano, motsimikiza monga ine ndaimirira pa nsanja usikuuno, ine ndinali nalo vumbulutso lomwe linawululula. Icho chiri mu kufutukuka patatu. Izo ine ndiyankhula kwa inu, mwa thandizo la Mulungu, za kufutukuka kwa Icho. Ndiyeno inu. . . Tiyeni tidutse pa izo, poyamba. Apa pali vumbulutsolo, kuti ndiyambe zomwe ine ndikufuna kukuwuzani inu, chomwe Icho chiri. Chimene chikuchitika, ndi chakuti. . . Mabingu Asanu Ndi Awiri amenewo omwe iye anawamva akugunda, ndipo analetsedwa kuti alembe; ndiwo chimene chinsinsicho chiri, chikugona kuseri kwa Mabingu Asanu Ndi Awiri otsatizana amenewo akulengeza.

249 Tsopano, chifukwa chiyani? Tiyeni titsimikizire zimenezo. Chifukwa chiyani? Icho ndi chinsinsi chimene palibe aliyense akudziwa za icho. Yohane analetsedwa kuti alembe za Icho, nkomwe—ngakhale kulemba chiphiphiritso cha Icho. Chifukwa chiyani? Ichi ndi chifukwa chake kunalibe chochitika mu—chochitika Kumwamba: icho chikanakhoza kuwululula chinsinsicho. Kodi inu mukuziwona zimenezo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

250 Ngati Icho chiri chachikulu kwambiri, Icho chiyenera kuphatikizidwa, chifukwa Icho chiyenera kuchitika. Koma pamene Mabingu Asanu Ndi Awiri. . .

251 Tsopano zindikirani. Pamene Angelo asanu ndi awiri anabwera kudzawomba Malipenga awo, panali bingu limodzi. [M'bale Branham akugogoda pa guwa kamodzi—Mkonzi]. Pamene Israeli anasonkhanitsidwa, panali lipenga. "Pamene sipadzakhalanso nthawi," lipenga lotsiriza, bingu limodzi.

252 Koma apa pali Mabingu Asanu Ndi Awiri olunjika, kumene mu mzere: wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, nambala yangwiro imeneyo. Mabingu Asanu Ndi Awiri ali mu mzere, anabangula, osati . . . kungopanga—basi wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, molunjika. [M'bale Branham anagogoda pa guwa kaseveni—Mkonzi]. Ndiye, Miyamba simukanakhoza kulemba Zimenezo. Miyamba simungakhoze kudziwa za Zimenezo, palibe china chirichonse, chifukwa apo palibe kanthu koti kazipitirira. Iyo inali nthawi yosatangwanika. Icho chinali chachikulu kwambiri, mpaka, Icho chinasungidwa chachinsinsi kwa Angelo.

253 Tsopano, chifukwa chiyani? Ngati Satana angachigwire Icho, iye akhoza kuwononga kwakukulu. Apo pali chinthu chimodzi chomwe iye sakuchidziwa. Tsopano, iye akhoza kumasulira chirichonse chimene iye akufuna kutero, ndi kukopera mphatso ya mtundu uliwonse, (ine ndikuyembekeza kuti inu mukuphunzira), koma iye sangakhoze kuchidziwa Ichi. Icho sichinalembedwe nkomwe mu Mawu. Icho ndi chinsinsi kwathunthu.

254 Angelo, chirichonse, chinakhala chete. Ngati iwo akanapanga kusuntha kumodzi, iko mwina kukanapereka chinachake, kotero iwo anangotseka pakamwa, anasiya kuyimba azeze. Chirichonse chinayima.

255 Seveni, nambala yangwiro ya Mulungu. Seveni, [M'bale Branham akugogoda pa guwa kaseveni—Mkonzi]. basi mpaka mmusi mwa mzere. Mabingu Asanu Ndi Awiri anabangula motsatizana limodzi, ngati kuti iwo anali kutchula chinachake. Zindikirani, pa nthawi imeneyo, Yohane anayamba kuti azilemba Icho. Iye anati, "Usalembe Icho."

256 Yesu sanayankhulepo konse za Icho. Yohane sakanakhoza kulemba za Icho. Angelo sakudziwa kanthu za Icho. Ndi chiyani Icho? Ndi chinthu chimene, Yesu anati, "Ngakhale Angelo a Kumwamba sankadziwa" kanthu za Icho. Mukuona? Mukuona? Iye sankachidziwa Icho, Iyemwini. Anati, "Mulungu yekha" akuchidziwa Icho.

257 Koma Iye anatiuza ife, kuti pamene ife "tidzayamba kuwona zizindikiro izi zikubwera." Tsopano kodi inu mukufika kwinakwake? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Zindikirani, ife "tikadzayamba kuwona zizindikiro izi zikubwera." Mukuona?

Ngati Satana akanachigwira Icho . . .

258 Ngati iwe utafuna kuti chinachake chichitike . . . Tsopano inu muyenera kutenga mawu anga pa izi. Ngati ine ndikukonzekera kuchita chinachake, ine ndimadziwa bwinoko kuposa kumuuza aliyense za icho. Osati kuti munthu ameneyo angachinene icho, koma kuti Satana achimva icho. Mukuona? Iye sangakhoze kuchipeza icho, mu mtima mwanga umo, bola

ngati Mulungu wachitsekera icho ndi Mzimu Woyera, kotero icho chimakhala pakati pa ine ndi Mulungu. Mukuona? Iye samadziwa kanthu za icho mpaka inu mutachiyankhula icho, mukatero iye amachimva icho. Ndipo ine ndimayesetsa . . . ine ndikawauza anthu kuti ndichita chinthu *chakuti-chakuti*, ndipo umamuwona mdierekezi akudula gudumu lirilonse lomwe iye angakhoze, kuti akafike kumeneko, mwaona, kuti andichinye ine pa icho. Koma ngati ine ndipeza vumbulutso kuchokera kwa Mulungu, ndipo nkusangonena kanthu za ilo, ndiye izo zimakhala zosiyana.

259 Kumbukirani, Satana adzayesetsa kukopera. Iye adzayesetsa kukopera chirichonse chimene Mpingo uti udzachite. Iye wayesetsa kuchita zimenezo. Ife tazizindikira izo, kupyolera mwa wotsutsakhristu.

260 Koma ichi ndi chinthu chimodzi chimene iye sangakhoze kuchikopera. Sipadzakhala kutsanzira kwa ichi, mwaona, chifukwa iye sakuchidziwa Icho. Palibe njira yoti iye achidziwire Icho. Icho ndi Chikoka Chachitatu. Iye basi sakudziwa kanthu za Icho. Mukuona? Iye samachimvetsetsa Icho.

261 Koma pali chinsinsi chomwe chagona pansi pa Icho! Ulemelero kwa Mulungu wa Mmwambamwamba! Ine sindingakhoze konse kuganiza chimodzimodzi, moyo wanga wonse, pamene ine ndinawona. Tsopano, ine sindikudziwa chomwe . . . Ine ndikudziwa sitepe yotsatira pamenepo, koma sindikudziwa chomwe, momwe ndingamasulire izo. Izo sizitenga nthawi yaitali. Ine ndalemba pansi apa, pamene izo zimachitika, ngati inu mungakhoze kuwona apa, "Ima. Usapitirire kudutsa pomwe apa." Ine sindiri wotentheka. Ine ndikungonena Choonadi.

262 Koma kodi inu mukukumbukira nsapato yaing'ono ija, yomwe ine nthawizonse ndakhala ndikuyesetsa kufotokoza momwe kuti solo inkagona pafupi ndi *chakuti-ndi-chakuti*, ndi chikumbumtima chamkati, ndi zinthu zonse za mtundu umenewo? Chomwe, chinangopangitsa gulu lalikulu la zokopera kuyambika pa icho. Momwe iwo amayenera kutenga dzanja, ndi kuwagwira anthu, ndi kukhala ndi kututuma? Aliyense anali nako kututuma mmanja mwawo.

263 Koma inu kumbukirani, pamene Iye ananditengera ine pamwamba uko, ndipo anati, "Ichi ndi Chikoka Chachitatu chija, ndipo palibe aliyense ati adzachidziwe Icho." Inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Masomphenya samalephera nkomwe. Iwo ali Choonadi mwangwiro.

264 Tsopano zindikirani. Mukukumbukira masomphenya a kuwundana aja? Charlie, ine . . . Ndi iwe apa.

265 Chinachake chikuchitika, ine ndinakuuza iwe, sabata ino, kuti iwe . . . Icho chakhala chiri paliponse pokuzungulira iwe, koma ine ndikudabwa ngati iwe unachizindikira icho.

266 Mukukumbukira kuwundana, kwa masomphenya a Angelo, pamene ine ndinachoka kuno kuti ndikupita ku Arizona? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Inu mukukumbukira *Ndi Nthawi Yanji Ino, Mabwana?* ["Ameni."] Inu mukukumbukira zimenezo? Zindikirani, apo panali kuphulika kumodzi kokha kwa bingu, ndipo Angelo asanu ndi awiri anawonekera. Nkulondola uko? ["Ameni."] Kuphulika kumodzi kwa bingu, Angelo asanu ndi awiri anawonekera.

Ndipo ndinawona Mwanawankhosa pamene iye ana*tsegula* chisindikizo choyamba, *ndipo ine ndinamva, ngati kuti ilo* linali liwu *la bingu,* ndipo *chimodzi cha zamoyo zinayi* chinati, *Bwera ndipo udzawone.*

267 Zindikirani, bingu limodzi, Mauthenga Asanu Ndi Awiri omwe anasindikizidwa ndipo sangakhoze kuwululidwa kufikira tsiku lotsiriza, la m'badwo uno. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

268 Tsopano, kodi inu mwalizindikira gawo lachinsinsi la sabata ino? Ndicho chomwe Icho chiri. Ndicho chomwe Icho chakhala chiri. Wakhala asali munthu, a—munthu, akhala ali Angelo a Ambuye.

269 Zindikirani, pali mboni, zitatu, zakhala mkati muno, kuti sabata yapitayo, kupitirira pang'ono sabata yapitayo, ine ndinali pamwamba, kutali uko mmapiri, koyandikira ku Mexico, ndinali ndi abale awiri omwe akhala pano. Ndikuchotsa chisoso, kapena zomamatira, pa mwendo wa thalauza langa; ndipo kuphulika kunachitika, komwe pafupifupi, kunawoneka ngati, kunagwedezera mapiri pansi. Tsopano, uko nkulondola. Ine sindinawauze konse abale anga, koma iwo anazindikira kusinthikako.

270 Ndipo Iye ananena kwa ine, "Tsopano ukonzekere. Uzipita kummawa. Ndi uku kumasulira kwa masomphenya aja." Mukuona? Tsopano, kuti ndikudziwitseni inu, M'bale Sothmann sanaphe nyama yomwe iye amafuna. Ife tinali kuyesetsa kuti timupezere iye. Ndipo Iye anati, "Tsopano, usikuuno, kuti chikhale chizindikiro kwa iwe, iye sachita zimenezo. Iwe uyenera udzipatule wekha pa nthawi ino chifukwa cha kudzacheza kwa Angelo awa." Ndipo ine ndinamverera ngati ndasokonezeka, inu mukukumbukira.

271 Ndipo ine ndinali kumadzulo. Angelowo anali akubwera kummawa. Ndipo pamene iwo anali akubwera pamenepo, ine ndinanyamulidwa nawo iwo, (inu mukukumbukira zimenezo?) akubwera kummawa.

272 Ndipo M'bale Fred, muno usikuuno, ndi mboni, ndi M'bale Norman. Pamene ife tinali kupita kumeneko, ine

ndinatsala pang'ono kuti ndimunyengerere mwamuna ameneyo kuti atsalire ndi kupeza nyama yake. Nkulondola uko, M'bale Sothmann? [M'bale Fred Sothmann akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Eya, apo, wayima pomwe apo. Ine ndinamukakamiza; koma, apobe, Iye anati, "Iye sachita zimenezo." Ine sindinayankhule kalikonse; ndinapitirirabe.

273 Chinachake, nditakhala cha pambali pa chihema, tsiku limene . . . Iwe ukukumbukira, M'bale Sothmann. Ndipo ine, mwamsanga pamene zinthu zina zinali kunenedwa, kuti Ine ndinakuyika iwe ndi M'bale Norman . . . Kodi M'bale Norman ali kuti? Kumbuyo uko. Ndinawayika iwo pansi pa lumbiriro, kuti iwo asadzanene zomwe zinali kuchitika. Nkulondola uko? [Abalewo akuti, "Ameni. Izo nzoona."—Mkonzi]. Kodi ine ndinatembenuka ndi kudzachokapo ku chihema chija, monga *choncho*? Nkulondola uko? ["Uko nkulondola."]

274 Chifukwa, ichi ndi chimene chinali, ndendende chomwe icho chinali, ndipo podziwa kuti ine sindikanakhoza kunena icho mpaka icho chitachitika, kuwona ngati anthu angachimvetse icho.

275 Ndipo kodi inu munazindikira? "Mngelo mmodzi uja," ine ndinati, "mkati umo, munali Mngelo wachirendo." Iye ankawoneka wodziwika kwa ine kuposa aliyense wa Iwo. Inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Iwo anali mu kuwundana; atatu mmbali, ndipo mmodzi anali pamwamba. Ndipo mmodzi yemwe anali pafupi ndi ine apa, kuwerenga kuchokera kumanzere kupita kumanja, akanakhala Mngelo wachisanu ndi chiwiri. Iye anali wowala, anatanthauza mochuluka kwa ine kuposa ena onse a Iwo. Inu mukukumbukira? Ine ndinati, "Iye anali atatulutsa chidali chake kunja, monga *choncho*, ndipo anali kuwulukira chakummawa" (inu mukukumbukira) "monga chomwecho." Ine ndinati, "Iye anandinyamulira ine mmwamba; kundikwezera ine mmwamba." Inu mukukumbukira zimenezo? ["Ameni."]

276 Ndi Uyu apa, yemwe ali ndi Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, chinthu chimene ine ndakhala ndikuchidabwa moyo wanga wonse. Ameni! Zisindikizo zinazo zinatanthauza zochuluka kwa ine, ndithudi, koma, oh, inu simukudziwa chomwe Ichi chatanthawuza, kwa nthawi imodzi m'moyo!

277 Ine ndinapemphera, ine ndinalirira kwa Mulungu. Ine—ine—ine . . . Utatha msonkhano uja wa ku Phoenix . . . Aliyense wa anthuwo, kumeneko ndi ine, tikudziwa. Ine ndinagona mmapiri.

278 Mmawa wina, ine ndinadzuka ndipo ndinapita ku Sabino Canyon, mapiri aakulu, okumbika, aatali amenewo. Ndipo ndinapita pamwamba kumeneko. Ndipo uko kuli kanjira-kamapazi kakang'ono, iwe utha kukhota, kupita pamwamba ku Phiri la Lemmon, komwe kuli kuyenda kwa mailosi sarte, pafupifupi chisanu cha mapazi sarte pamwamba

kumeneko. Kotero, pamwamba m'phiri, mmawa kwenikweni kusanache, ndikupita pamwamba kudutsa mu kanjira kamapazi kakang'ono aka, ndikugudubuza miyala pokwera. Ine ndinamverera kutsogozedwa kuti nditembenukire ku mbali *iyi*. Ndipo ine ndinatembenuka, ndipo ndinapita mmwamba mu miyala ina yayikulu, yosongoka, oh, mai, yotalika mahandiredi a mapazi mmwamba.

279 Ndipo ine ndinagwada pansi pakati pa miyala imeneyo. Ine ndinagoneka pansi Baibulo *ili*, ndi kugoneka pansi bukhu ili . . . tabuleti yaing'ono *iyi*. Ine ndinati, "Ambuye Mulungu, kodi masomphenya awa akutanthauza chiyani? Ine—ndine—ndine . . . " Ine ndinati, "Ambuye, iwo . . . Kodi iwo akutanthauza kufa kwanga?"

280 Inu mukukumbukira, ine ndinakuuzani inu, "Ine ndinkaganiza kuti iwo akhoza kutanthauza imfa yanga, chifukwa chinachake chinaphulika mpaka icho chinangondigwedezera ine mzidutswa." Inu mukukumbukira zimenezo. Ndi angati akudziwa zimenezo, anazimvapo izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Bwanji, zedi, mwaona, nonse a inu. Ndipo ndinkaganiza kuti izo zikanakhoza kutanthauza imfa yanga.

281 Ndiyeno mchipindamo, ine ndinati, "Chinali . . . Chiyani—chiyani—chinali chiyani icho, Ambuye? Chiyani—kodi izo zikutanthauza chiyani? Kodi izo zikutanthauza kuti ine ndimwalira? Ngati izo ziri chomwecho, chabwino, ine sindinena kwa banja langa. Ingondirolani ine ndizipitirira, mwaona, ngati ntchito yanga yatha." Ndipo ine ndinati . . .

282 Tsopano, chinali chiyani icho? Koma Iye anatumizanso umboni, inu mukukumbukira ine ndikukuuzani inu, kuti izo sizinali zimenezo. Uko kunali kupitiriza kwa ntchito yanga. Oh, oh, oh! Inu mukumvetsa zimenezo?

283 Mwaona, ndipo nditakhala pamwamba mu Sabino Canyon, Atate Akumwamba akudziwa izi, moona basi monga inu mukuwona izo zikufika pochitika, Angelo amenewo anabwera mpaka mmusi ndipo anadzatsimikizira Uthenga uliwonse kuti unali chimodzimodzi. Ndiye, inu mukudziwa ngati Iwo ukuchokera kwa Mulungu, kapena ayi. Izo zinaloseredwa, inu, mwa masomphenya. Ine sindikanakhoza kukuwuzani inu mpaka misonkhano itatha, chifukwa ine ndinaletsedwa kutero.

284 Mu Sabino Canyon, nditakhala pamwamba apo mmawa uja, ine ndinali nditakweza manja anga mmwamba. Ndipo changa . . . Mphepo inali itakupizira pansi chipewa changa chakuda chakale. Pamene . . . Ine ndinali nditayima pamenepo, ndi manja anga mmwamba, ndikupemphera. Ine ndinati, "Ambuye Mulungu, kodi ichi chikutanthauza chiyani? Ine sindikutha kuchimvetsa icho, Ambuye. Kodi ine ndichite chiyani? Ngati ili nthawi yanga yopita Kwathu, mundirole ine

ndizipita pamwamba pano, ndi pamene iwo sangadzandipeze konse ine. Ine sindikufuna kuti aliyense azidzabuula pozungulira, ngati ine ndikupita. Ine—ine ndikungofuna kuti banja lidzaganize kuti ine ndinangoyenda ulendo. Ndipo iwo sadzandipeza ine. Mukandibise ine kutali kwinakwake. Ngati nditi ndizipita, bwanji, mundirole ine ndizipita. Mwinamwake Joseph adzalipeza Baibulo langa litagona apa, tsiku lina, ndipo mumulole iye adzaligwiritse Ilo ntchito. Mwaona, ngati ine ndikuchokapo, ndiroleni ine ndizipita, Ambuye." Ndipo ine ndinali ndi manja anga mmwamba. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, chinachake chinagunda dzanja langa.

285 Ine sindikudziwa. Ine sindingakhoze kunena. Kodi ine ndinali nditagona? Ine sindikudziwa. Kapena kodi ine ndinalowa mu chizimbwizimbwi? Ine sindikudziwa. Kodi anali masomphenya? Ine sindingakhoze kukuwuzani inu. Chinthu chokhacho chimene ine ndingakhoze kunena ndi chomwe ine. . . Chinthu chomwecho basi monga momwe Angelo awo anakhalira!

286 Ndipo icho chinakhudza dzanja langa. Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo ilo linali lupanga. Ndipo ilo linali ndi chigwiriro cha ngale, chokongola kwenikweni; ndipo linali ndi chotetezera pa ilo, cha golide. Ndipo mpeniwo unkawoneka ngati chinachake chonga koromu, monga siliva, kokha kuti unali wonyezimira kwenikweni. Ndipo iwo unali wooneka ngati nthenga m'mbali mwake ndipo wakuthwa kwambiri, oh, mai! Ndipo ine ndinaganiza, "Kodi icho si chinthu chokongola kwambiri!" Langokwanira mdzanja langa! Ine ndinaganiza, "Ndiro lokongola kwenikweni. Koma," ine ndinati, "hey, ine nthawizonse ndimawopa zinthu zimenezo, lupanga." Ine ndinaganiza, "Ine ndichita nalo chiyani ilo?"

287 Ndipo basi pomwepo Liwu linagwedeza pansi kudutsa pamenepo, lomwe linagudubuza miyala. Linati, "Ilo ndi Lupanga la Amfumu!" Ndipo kenako ine ndinatuluka mu zimenezo.

288 "Lupanga la Amfumu." Tsopano, ngati Ilo likanati, "Lupanga la mfumu. . ." Koma Ilo linati, "Lupanga la Amfumu." Ndipo pali mmodzi yekha "Amfumu," ndipo ndiye Mulungu. Ndipo Iye ali nalo Lupanga limodzi, ndiro Mawu Ake, womwe ine ndakhalira nawo moyo. Ilo, kotero ndithandizeni ine, Mulungu; nditayima pa gome Lake loyera apa, ndi Mawu oyera awa ali apa! Ilo ndi Mawu! Ameni! Oh, ndi tsiku lanji lomwe ife tikukhalamo! Ndi chinthu chachikulu bwanji! Mukuwona chinsinsicho ndi chobisika? Chachitatu. . .

289 Nditayima pamenepo pamene izi zinandichokera ine, Chinachake chinangobwera kwa ine ndipo chinati, "Usawope ayi." Tsopano, ine sindinamve liwu lirilonse. Zinali ngati mkati mwa ine, munayankhula. Ine ndikungoyenera kuti ndikuwuzeni

inu zoona, ndendende basi chomwe chinachitika. Chinachake chinagunda, ndipo chinati, "Usawope ayi. Ichi ndi Chikoka Chachitatu chija."

290 Chikoka Chachitatu! Inu mukuchikumbukira Icho? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Iye anati, "Iwe wakhala nazo zokopera zambiri pa izi, zomwe iwe umayesetsa kuti uzifotokoze. Koma," anati, "usati uyesere nkomwe, Ichi." Inu mukukumbukira zimenezo? Ndi angati akukumbukira masomphenya aja? ["Ameni."] Bwanji, izo ziri paliponse. Izo zinajambulidwa, ndipo ziri konsekonse. Izo zakhala ziri pafupifupi zaka sikisi zapitazo, zaka seveni zapitazo. Zakhala ziri zaka seveni zapitazo. Anati, "Usayesere kuchifotokoza Icho." Anati, "Ichi ndi Chikoka Chachitatu, koma ine ndikakumana nawe iwe mkati umo." Nkulondola uko? ["Ameni."] Iye anati, "Usati uyesere . . . "

291 Ine ndinali nditayima ndiri ndi a—kansapato kakang'ono ka mwana, pamene Iye ankandiuza ine. Anati, "Tsopano upange Chikoka chako Choyamba. Ndipo pamene utatero, nsomba zithamangira nyamboyo." Anati, "Kenako udzawone Chikoka chako Chachiwiri," anati, "chifukwa Icho chidzangokhala nsomba yaying'ono." Iye anati, "Kenako Chikoka Chachitatu chidzagwira izo."

292 Ndipo azitumiki onse awo anandizungulira ine, anati, "M'bale Branham, ife tikudziwa kuti inu mukhoza kuchita zimenezo! Aleluya! M'bale Branham!" Apo ndi pamene ine nthawizonse ndimazimangirizapo, ndi gulu la azitumiki. Mukuona? Ine ndimawakonda anthu. Iwo amafuna kuti iwe uzifotokoza chirichonse, *ichi*, *icho*.

293 Ndipo ine ndinati, "Chabwino, uh, uh, uh," Ine ndinati, "Ine sindikudziwa." Ine ndinati, "Ine ndimamvetsetsa zowedza. Tsopano," ine ndinati, "tsopano, chinthu choyamba chomwe inu mungachite . . . Umu ndi momwe zimachitidwira. Inu mukawona nsomba zonse pozungulira; inu muyenera kumagwedeza nyamboyo." Chabwino, ndizo ndendende njira zowedzera nsomba. Kotero ine ndinati, "Mudzagwedeze nyamboyo. Tsopano, inu mukuona, pamene ine ndinagwedeza nyamboyo, nthawi yoyamba, tsopano nsombazo zinatsatira iyo." Koma izo zinali zazing'ono. Ndipo izo zinali basi zofanana ndi zomwe iwo anali kupha.

294 Kotero ndiye ine—ine ndinati, "Kenako inu mudza—mudzayike . . . " Ndipo ine ndinaikokera iyo pa mtunda, pa gombe. Ndipo ine ndinali ndi nsomba, koma iyo inkawoneka ngati kakhungu pa nyambo, iyo inali chabe . . . iyo inali yaing'ono kwambiri.

295 Ndiyeno ine ndinali kuyima pamenepo, ndipo Chinachake chinati, "Ine ndinakuwuza iwe kuti usachite zimenezo!"

296 Ine ndinayamba kulira. Chingwe chonse chinali chitamangana mondizungulira ine, monga *chonchi*. Ndipo ine ndinali . . . ndinali nditayima pamenepo, ndikulira, mutu wanga utazyolika pansi monga *choncho*. Ine ndinati, "Mulungu! Oh, ine . . . Ndikhululukireni ine! Ine—ndine munthu wopusa. Ambuye, musati . . . Mundikhululukire ine." Ndipo ine—ine ndinali nacho chingwe ichi.

297 Ndipo icho, chimene ine ndinali nacho mdzanja langa, inali nsapato ya mwana wamng'ono, pafupifupi yotalika *chonchi*. Ndipo ndinali ndi chingwe chimenecho, chinali chonenepa pafupifupi monga ngati chala changa, pafupifupi theka la inchi, chomwecho. Ndipo kabowo mu nsapato iyi kanali basi kukula kwa . . . kocheperapo kuposa wa—wani pa sikisitini, mwinamwake, ya inchi, mu kabowoko. Ndipo ine ndinali kuyesetsa kumanga nsapato yaing'ono iyi, ndi chingwe cha inchesi yayikulu ichi. Huh!

298 Liwu linabwera, linati, "Iwe sungakhoze kuwaphunzitsa makanda Achipentekoste zinthu zauzimu." Anati, "Tsopano, asiye iwo okha!"

299 Ndipo basi nthawi yomweyo Iye anandinyamulira ine mmwamba. Iye ananditengera ine mmwamba, ndi kudzandikhazika ine pamwamba kwambiri, kumene msonkhano unali kuchitikira. Chinkawoneka ngati chihema kapena kachisi, wa mtundu wina. Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo apo panali kabokosi kakang'ono, monga, malo aang'ono cha kumbali. Ndipo ndinawona kuti Kuwala kuja kunali kukuyankhula ndi winawake, pamwamba pa ine, Kuwala kuja kumene inu mumakuwona pa chithunzi apo. Iko kunadzazungulira kuchoka kwa ine, monga *choncho*, ndipo kunadzapita pamwamba pa chihema icho. Ndipo kunati, "ine ndikakumana nawe iwe kumeneko." Ndipo kunati, "Ichi chidzakhala Chikoka Chachitatu, ndipo iwe sudzachinena Icho kwa aliyense."

Ndipo mu Sabino Canyon, Iye anati, "Ichi ndi Chikoka Chachitatu."

300 Ndipo pali zinthu zitatu zazikulu zomwe zikupita nacho Icho. Ndipo chimodzi chafutukuka lero, kapena, dzulo; chinacho chafutukuka lero; ndipo pali chinthu chimodzi chimene ine sindingakhoze kuchimasulira, chifukwa icho chiri mu chinenero chosadziwika. Koma ndinayima pomwepo ndi kuyang'ana molunjika kumene pa Icho. Ndipo ichi ndi Chikoka Chachitatu chikubwerapo. Ndipo Mzimu Woyera wa Mulungu . . . Oh, mai!

Ndi chifukwa chake Kumwamba konse kunali chete.

301 Tsopano, ine—ine kulibwino ndiyimire pomwepa apa, mwaona. Ine basi—ine ndikungomverera kuyimikidwa, kuti ndisanenenso zochuluka za Icho. Mukuona?

302 Kotero, ingokumbukirani, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, chifukwa chimene Icho sichinatsegulidwe. Mwaona,

chifukwa chimene Icho sichinawululе Icho, palibe aliyense akuyenera kudziwa za Icho.

303 Ndipo ine ndikufuna kuti inu mudziwe, ine ndisanadziwe ngakhale Mawu aliwonse a Icho, masomphenya aja anabwera zaka zapitazo. Inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndipo apa Icho chiri, basi monga momwe china ichi chakhalira, kugwera molunjika kumene kukalowa mu Mawu ndendende kumene Icho chinali. Ndipo Mulungu akudziwa mtima wanga, ine sindinaganizepo nthawi imodzi za chinthu choterocho chonga Icho, ndipo apa Icho chinali. Nthawi yatha kuposa momwe ife tikuganizira. Uh-huh. Oh, mai!

304 Izo zikuwonetsa kuti Icho ndi chochokera kwa Mulungu, pakuti, onani, Icho chikukwanira ndendende mu malonjezo a Mulungu, kuchokera ku mapeto a—a Uthenga. Inu muzindikira. Zindikirani tsopano, kwa Uthenga-wa-nthawi-yotsiriza, Chisindikizo ichi. Kuwonjezera apo, Iye—Iye wawululа Zisindikizo zisanu ndi chimodzi zonsezo, koma Iye sakunena kanthu kokhudza Chachisanu Ndi Chiwiri. Ndipo Chisindikizo cha nthawi yotsiriza, pamene Icho chidzayambe, chidzakhala mwamtheradi chinsinsi kwathunthu, molingana ndi Baibulo, ife tisanachidziwe Icho. Ndipo kumbukirani, Chivumbulutso 10:1-7, 1 mpaka 7, mutu wa 10:1 mpaka 7, "Pa mathero a Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, zinsinsi zonse za Mulungu zidzadziwika." Ife tiri pa nthawi yotsiriza, kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri.

305 Tsopano, ine ndinadziwa bwanji? Tsiku lina, Lamlungu lathali, sabata yapitayo lero, pamene ine ndinali kulalikira pa "Khalani odzichepetsa! Khalani odzichepetsa! Kumbukirani, Mulungu amachita mu zinthu zazing'ono." Ine sindinazindikire chomwe kwenikweni chinali kuyankhulidwa. Ndipo tsopano ine ndikuchiwona icho. Izo ziri mwanjira yophweka chomwecho! Inu mukuganiza kuti chinachake chonga chimenecho chikanakawululidwa ku Vatican kapena. . . Koma Icho chikubwera monga ngati Yohane M'batizi. Icho chikubwera monga kubadwa kwa Ambuye wathu, mu khola. Ulemelero kwa Mulungu! Kotero ndithandizeni ine, ora layandikira! Ameni! Ife tiri pano. Oh, mai!

306 Tsopano kodi inu mukuchiwona icho, Choonadi cha masomphenya a Mulungu, Angelo seveni akundibweretsa ine kuchokera kumadzulo? Iwo anali kubwera kuchokera kumadzulo, kubwerera kummawa, kundibweretsa kuno chifukwa cha Uthenga uwu usikuuno. Oh, mai!

307 Tsopano, Liwu la bingu lalikulu lija, ndi cholinga chomwe linabweretsedwera kuno, chawululidwa, kuti Ilo. . . ndipo zatsimikiziridwa kuti Ilo linali la Mulungu. Tangoganizani tsopano. Ine sindinkazidziwa Zisindikizo izi, ndipo izo

zawululidwa sabata ino. Kodi aliyense anaganizapo za zimenezo, za Angelo asanu ndi awiri amenewo kukhala Ichi, kukhala Uthenga umene unali kubwera, Angelo amenewo kundibweretsa ine kuno kwa cholinga Chimenecho? Mukuona?

308 Kumbukirani, Wamthenga wachisanu ndi chiwiri anali . . . Amithenga asanu ndi awiri anali . . . Mmodzi wodziwikayo kwa ine, Mngelo wachisanu ndi chiwiri, Iye amawoneka mochuluka kwa ine kuposa aliyenseyo. Tsopano, onani, iwo anali atayima monga *chonchi*. Tsopano, ife tikungofuna kuti inu muzindikire. Ndipo ine ndinali nditayima *apa*, ndipo ine ndinali kuwayang'ana ena amenewo . . .

309 Mwaona, limodzi, gulu loyamba, la mbalame zazing'ono, nthenga zonse zitathothokera pansi. Inu mukukumbukira zimenezo? Ndipo izo zonse zinawulukira chakummawa. Ndipo gulu lachiwiri, zinali zowalirapo, mbalame zokulirapo, zimawoneka ngati nkhunda, zamapiko osongoka. Izo zinawulukira chakummawa. Chikoka Choyamba, Chikoka Chachiwiri, kenako lotsatira anali Angelo. Ndipo monga . . .

310 Ine ndinali nditayima pamenepo, ndipo kuphulika uku kunadzachokapo. Ndipo ine ndinali kuyang'ana mbali *iyi*, moloza kumadzulo, ndipo Iwo anabwera ndipo basi anadzandinyamulira ine mmwamba, mkati Umo. Ine ndinapita kutali kwa kudziwa kwanga. Ndipo mmodzi wa Iwo, akubwera, anali Mmodziyo yemwe ankawoneka wachirendo kwambiri kwa ine, anali Iye amene anali kwanga . . . Kukhale kumanzere, kumene ine ndinalowera mu kuwundanako. Koma kuwerenga kuchokera kumanzere kupita kumanja, iye angakhale Mngelo wachisanu ndi chiwiri, mwaona, akubwera chopingasa. Tsopano, kumbukirani, Amthenga asanu ndi awiri.

311 Kodi inu mukukumbukira piramidi ya Mwala woyera, ya loto la Junior Jackson lomwe ine ndinamasulira kwa inu? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mukuona? Zindikirani, usiku umene ine ndinachoka, ndipo ine . . . Panali maloto sikisi omwe anabwera, ndipo limodzi lirilonse la iwo molunjika kupita kwa chinthu chomwecho. Kenako masomphenyawo anayamba, ndipo anandituma ine kumadzulo. Ndipo, Junior, iye anali kuyang'anira pamene . . . Zindikirani. Penyani ungwiro wake!

312 Tsopano, ine ndiri—ine ndikuyembekeza ndi kudalira kuti anthu inu mukuzindikira kuti ine ndikuyesetsa kuyika chisomo ichi pa Yesu Khristu, Yemwe ali Mlembi wa Icho chonse. Ndipo chifukwa chokhacho chomwe inu simunandimve ine konse ndikuyankhula monga chonchi mmbuyomu, mmoyo wanu, koma ora ili likuyandikira. Mukuona? Mukuona? Zindikirani.

313 Tsopano kuti ndizipange izo motsimikizika, kwa inu, kuchitira kuti zikhoze kukhomereredwa pansi. Ine ndikukonzekera kuti ndikusiyeni inu kachiwiri. Ine

sindikudziwa komwe nditi ndipite. Ine ndiyenera kukalalikira Uthenga ku malo ena. Koma tsopano, kuti . . .

314 Inu mukhoza kunena kuti, "Ine ndamva mtundu wonse wa kutentheka kumeneko." Ine sindikudziwa chiyani; ine sindingakhoze kumuweruza munthu wina aliyense.

315 Ine ndiyenera kungoyankhira kwa Mulungu pa zomwe ine . . . kwa—kwa inemwini. Koma kodi panayamba pakhalapo konse nthawi imodzi yomwe ine ndinakuwuzanipo inu chirichonse mu Dzina la Ambuye, chomwe sichinali cholondola, mu zaka zonsezi? [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Palibe aliyense angakhoze kunena chomwecho, chifukwa ine nthawizonse ndakhala ndikuzinena izo basi momwe Iye amanenera izo.

316 Tsopano mundirole ine ndingokuwonetsani inu kuti izi ndizo ndendende zoona, ndi kutsimikizira izo.

317 Tsopano kumbukirani, "Ngati akhalapo wauzimu kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzayankhula kwa iye mmasomphenya, ndi kudzizindikiritsa kwa iye mwa maloto." Kumasulira maloto, kumeneko. Yosefe, iye ankakhoza kumasulira maloto, ndi kuyankhula ndi—ndi kuwona masomphenya. Kodi izo nzoona?

318 Tsopano zindikirani ichi, kuti, tsopano, pamene ichi chinachitika, Junior anali atayima mmunda umene unali ndi a—unali ndi piramidi yaikulu mmenemo, monga chomwecho. Ndipo pamenepo panali chinachake chitalembedwa pa miyala, ndipo ine ndinali kuwulula Icho kwa anthu. Nkulondola uko, Junior? [M'bale Junior Jackson akuti, "Ndi zoona zimenezo."—Mkonzi]. Pafupifupi chaka izo zisanachitike.

319 Ndipo zindikirani chinthu chotsatira tsopano. Ine ndinatenga chinachake chokhala ngati chitsulo ndipo ndinaidula Iyo, ndipo mkatimo munali Mwala woyera umene unalibe kanthu kolembedwa pa Iwo. Ndipo, pa nthawi imeneyo, ine ndinayamba kupita kumadzulo. Ndipo ine ndinawauza iwo onse, ine ndinati, "Musapite kumadzulo. Mukhale pano ndipo muziyang'ana pa Ichi kufikira ine nditabwerera." Ndinapita kumadzulo, kwa kuphulikako; ndinabwereranso kummawa, ndiri ndi Mzimu Woyera ukutanthauzira Mawu osalembedwa awa. Tsopano, ngati izo siziri mwangwiro Mulungu Wamphamvuzonse, ine ndikufuna kuti inu mudziwe chomwe izo ziri.

320 Kodi ine ndikuyesetsa kunena izi chifukwa chiyani, amzanga? Ndi kuti ndikuwonetseni inu kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza. Tsopano, ngati zinazo ziri mwangwiro pa dontho ndi Mawu, chomwechonso Ichi chiri mwangwiro pa dontho ndi Mawu! Ife tiri pano. Ife tiri pa mathero, amzanga.

321 Posachedwapa zidzakhala "nthawi yatha." Mamillioni adzataya miyoyo yawo. Mamillioni adzatero, omwe tsopano akukhulupirira kuti iwo ndi opulumutsidwa, adzawerengedwa

ngati utuchi wa m'badwo wa atomiki. Ife tikukhala pa ora lotsiriza. Mwa chisomo cha Mulungu Wamphamvuzonse, mwa thandizo Lake kwa anthu Ake, kuti iwo akakhoze kuyang'ana patsogolo ku kuwonekera kwaposachedwa kwa Khristu! "Motalika chotani, M'bale Branham?" Mwinamwake zaka twente; mwinamwake mu zaka fifite; mwinamwake mu zaka handiredi. Ine sindikudziwa. Ndipo mwinamwake mmawa; mwinamwake usikuunobe. Ine sindikudziwa. Ndipo aliyense yemwe angati akudziwa, iwo akulakwitsa. Mukuona? Iwo sakudziwa. Mulungu, yekha, akudziwa.

322 Tsopano zindikirani. Kotero ndithandizeni ine, mwa Mulungu, ine ndikunena Choonadi, kuti izi zazindikiridwa mwauzimu kwa ine, kuzindikiridwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo, chirichonse cha Izo, chazindikira malo Ake mu Baibulo.

323 Tsopano, chomwe chinsinsi chachikulu ichi chiri chimene chagona pansi pa Chisindikizo ichi, ine sindikudziwa. Ine sindikuchidziwa icho. Ine sindinakhoze kuzimvetsa izo. Ine ndinalephera kuchidziwa Icho, basi chomwe Icho—basi chomwe Icho chinanena, koma ine ndikudziwa kuti Icho chinali Mabingu Asanu Ndi Awiri amenewo akubangula iwoeni moyandikana kumene pamodzi, basi kumangogunda nthawi zisanu ndi ziwiri zosiyana. Ndipo Iwo anafutukulidwa mu chinachake chimene ine ndinachiwona. Ndiye, pamene ine ndinachiwona Icho, ine ndinafunafuna kutanthauzira. Icho chinadzawuluka kudzadutsa pamenepo, ndipo ine sindinakhoze kuchimvetsa Icho. Uko nkulondola ndendende. Mukuona? Orali silinafikebe la Icho.

324 Koma, Icho chikusunthira mu mkombero umenewo, mwaona. Icho chikubwera moyandikira. Kotero, chinthu choti inu muchite ndicho kukumbukira kuti ine ndikuyankhula kwa inu mu Dzina la Ambuye. Mukhale okonzekera, pakuti inu simukudziwa nthawi yomwe chinachake chingakhoze kuchitika.

325 Tsopano, pamene icho chidzafike pa tepi, chomwe Icho chiri, icho mwinamwake chidzatumiza teni sauzande a abwenzi anga kudzandichokera ine. Chifukwa, iwo adzanena, kuti, "M'bale Branham akuyesetsa kuti adziyike yekha, ndi kudzipanga yekha, a—mtumiki kapena mneneri, kapena chinachake, pamaso pa Mulungu." Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu, abale anga, uko nkulakwitsa.

326 Ine ndikungokuuzani inu zomwe ine ndinawona ndi zomwe ine ndauzidwa. Ndipo tsopano inu—inu muchite chirichonse chimene inu mukufuna kuchita. Ine sindikudziwa yemwe ati. . . chomwe chiti chidzachitike. Ine sindikudziwa. Ine ndikungodziwa kuti Mabingu Asanu Ndi Awiri amenewo agwirizira chinsinsicho. Miyamba inali chete. Aliyense akumvetsa? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Iyo ikhoza kukhala nthawiyo, likhoza kukhala oralo tsopano, lomwe

munthu wamkulu uyu yemwe ife tikumuyembekezera kuti awuke powonekera akhoza kuwuka powonekera.

327 Mwinamwake utumiki uwu, umene ine ndayesetsa kuwatengera anthu kubwerera ku Mawu, wayika maziko; ndipo ngati iwo watero, ine ndidzakhala ndikukusiyani inu, kosabwereranso. Sipangakhale awiri a ife pano pa nthawi imodzi. Mukuona? Ngati ziri chomwecho, iye akula; ine ndichepa. Ine sindikudziwa.

328 Koma ine ndakhala nawo mwayi, mwa Mulungu, woyang'ana ndi kuwona chomwe Icho chinali, mwaona, ndachiwona chikufutukuka mochuluka chomwecho. Tsopano, icho ndi Choonadi.

329 Ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu mwazizindikira zinthu zimenezo zomwe zakhala zikuchitika sabata ino. Ine ndikutsimikiza kuti inu munamuzindikira mnyamata wamng'ono uja wa a Collins atagona pamenepo, akufa, usiku wina; wamng'ono uja, mtsikana wa leukemia.

330 Ufumu wa Mulungu ukubwera. Ndipo Iwo ukubwera moyandikira kwambiri kuchoka ku chithunzi kupita ku chenichenicho, monga izo zakhala zikuchitikira. Tsopano, izo siziyenera kuwatsamwitsa anthu. Kuchoka ku kulungamitsidwa, kupita ku kuyeretsedwa, mpaka ku ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo kenako *apa*, *apa*. Mukuona? Ife tikungoyandikira kwa Mulungu, nthawi zonse.

331 Kodi inu simukukhoza kuwona, atumiki a Methodisti, momwe kuti uthenga wanu wa kuyeretsedwa unali wapamwamba kwa uwo umene Luther analalikira?

332 Inu Achipentekoste, kodi inu simukuwona kuti uthenga wanu wa ubatizo ndi woposa womwe Amethodisti ankalalikira? Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza?

333 Oh, ife takhalapo nazo zinthu zambiri zikuchitika! Ndipo uko nkulondola. Ndipo ngati alipo aliyense amene amatsutsa cholakwika, ndipo anthu nkumanena chinachake chimene chiri makamaka chabodza ndipo osati Choonadi, ine ndimadana nazo zimenezo.

334 Koma ine—ine ndimakonda Choonadi chokhazikika, ziribe kanthu kaya ndi mochuluka bwanji momwe Icho chingasokonezere njira *iyi* kapena njira *iyo*. Ngati Icho chiri Choonadi, Mulungu potsiriza adzachiwonetsera Icho monga Choona. Ndipo ngati Iye sachita zimenezo, limodzi la masiku awa posachedwapa, ndiye kuti masomphenya anga sanali olondola. Tsopano inu mukuona pamene ine ndinangozigonekapo ndekha.

335 "Zidzakhala liti zimenezo, M'bale Branham?" Ine sindingakhoze kukuuzani inu. Ine sindikudziwa.

336 Koma, limodzi la masiku awa, ngati ife sitikumananso pa dziko lapansi lino, ife tidzakakumana kutsidya uko pa—pa Mpando Wachiweruzo wa Khristu. Ndipo inu mudzapeza, kuti, mchipinda chija, vumbulutso likubwera kuchokera kwa Mulungu, basi monga ngati ena onse achitira, kuti Iwo... Chimodzi cha chinsinsi cha Chisindikizo chimenecho, chifukwa chimene Icho sichinawululidwe, Iwo anali Mabingu Asanu Ndi Awiri omwe anayankhula maliwu Awo. Ndipo ndi Icho pamenepo, mwangwiro. Chifukwa, palibe chimene chikudziwa chirichonse cha Icho. Icho sichinalembedwe nkomwe. Chotero, ife tiri pa mapeto a nthawi. Ife tiri pano. Ine ndikumuthokoza Mulungu chifukwa cha Mawu Ake.

337 Ine ndikumuthokoza Iye chifukwa cha Yesu Khristu. Pakuti, popanda kumutumiza Iye kwa chi—chitetezero cha machimo athu, ife tonse tikanakhala tiri mu thope lalikulu la tchimo, opanda chiyembekezo. Koma, mwa chisomo Chake, Ake—Magazi Ake amatsuka tchimo lonse. Basi monga ngati dontho la inki mu chidebe cha Clorox, inu simungayipezenso konse inkiyo. Pamene machimo athu avomerezedwa, amayikidwa mu Magazi a Yesu Khristu; iwo sadzadziwikanso konse kachiwiri. Mulungu amawaiwala iwo; iwo sanachitidwe nkomwe. Ndipo bola ngati Nsembe imeneyo ikugona pamenepo mu chitetezero kwa ife, ndiye ndizo zonse. Ndi zimenezotu, mwaona. Ife—ife sitiri ochimwanso konse. Ndife Akhristu, mwa chisomo cha Mulungu. Kumbukirani, mwa ifeeni tikanakhoza kukhala oyipa basi monga ife tinali kale. Koma, mwaona, chisomo cha Mulungu chawonekera kwa ife, ndipo ndicho chomwe chatipanga ife kukhala chimene ife tiri lero, abale ndi alongo Achikristu.

338 Iyi yakhala sabata yopambana kwa ine. Ine ndatopa. Malingaliro anga atopa. Chifukwa ine—ine ndiri...ndi mopambana momwe ine ndikanakhoza kuchitira. Ndipo chinachake chachirendo chikuchitika, tsiku lirilonse. Ine ndimadabwitsidwa; kuyenda kulowa mchipindamo, ndi kukhala mmenemo kwa maminiti pang'ono, ndi kuwona Chinachake chikungonditembenuza ine mozungulira kwathuthu.

339 Ndipo, apa, ine ndimapita mkati umo ndi kukatenga zolemba. Ine ndimatha kutenga mabuku a Dr. Smith, Uriah Smith, ndi, oh, onse a—olembawo ndi chirichonse, ndi kuwerengamo, kuwerenga mmabuku awo. Ine nkudzati, "Tsopano *apa* pali Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi. *Apa* pali Chisindikizo Chachinayi. Tsopano kodi munthu uyu akunena chiyani? Iye amakhoza kunena kuti, 'Chabwino, Icho chinali *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*.'" Ine ndimatha kuyang'ana cha apa ndi kumutenga munthu winayu. Iye anati Icho chinali *chakuti-ndi-chakuti*. Ndipo izo nkumawoneka ngati ine basi... Izo basi sizimamveka molondola. Mukuona?

340 Ndiye ine nkuganiza, "Chabwino, ndi chiyani Icho, Ambuye?" Ndipo ine ndimatha kuyenda chokwera ndi chotsika

kwa kanthawi. Ine ndimagwada pansi ndi kupemphera. Kubwereranso ndi kukatenga Baibulo; kukhala pansi, kuwerenga. Kubwerera mmbuyo ndi mtsogolo.

341 Kenako, zonse mwadzidzidzi, pamene ine ndikhala chete, apa Icho chimangofutukuka monga chomwecho. Ndiye ine ndimagwira cholembera mwamsanga ndithu, ndi kuyamba kulemba Izo monga chomwecho, chirichonse chimene ine ndinali kuchiwona ndi kuchita. Kuchipenya Icho, monga chomwecho, mpaka ine nditachilemba Icho apo.

342 Ndiye ine ndimatenga, tsiku lonse, ndi kupita kumusi ndi kukachifufuza Ichi, ndi kuwona ngati Icho chinamangiriza njira yonse mmusi kudutsa Mmalemba. Kenako, "Kudzatsimikizira zinthu zonse." Mukuona? Ine ndikudzakhala ndi Ichi apa.

343 Ndipo ine ndikuganiza, "Tsopano, alipo anthu ambiri amene anali nawo masomphenya. Alipo ambiri amene akhala ali mmavumbulutso." Ngati izo zikutsutsana ndi Mawu, zisiyeni izo zokha; uko nkulondola, zisiyeni izo zokha.

344 Tsopano, tsopano, ndiye ine ndimatha kuchiyendetsa Ichi ngakhale mpaka mmusi monga *chonchi*, kuchiyendetsa icho mmusi monga *chonchi*. Ine ndimalemba zinthu zing'ono zing'ono apa. Ine ndikudzaganiza, "Chabwino, tsopano, kalasi ikakhala yokondwa kuzimva izi, chifukwa izo zikumangirira *apa* ndi kudzamangirira *apa*. Tsopano, tiyeni tiwone, kodi ichi chikunena chiyani *apa*? Inde. Ndipo, eya, apa icho chiri, pomwe *apa*." Mukuona?

345 Ndi kuchibweretsa Icho mmbuyo kudutsa mu Baibulo, ndi kudzachimangiriza chinthucho mmusi, kudutsa mu sabatayi. Ndi Ichi pamenepo, pa matepi. Ndinu olandiridwa kwa iwo. Ndipo ine ndazichita izo mwa kupambana kwa chidziwitso changa, pansi pa chiyanjano cha Chikhristu, chisomo cha Mulungu, kwa anthu onse, mwa Yesu Khristu. Ine ndachita mopambana kumene mmene ine ndimadziwira kachitidwe kake.

346 Inu mwakhala muli limodzi mwa magulu a omvetsera abwino kwambiri. Palibe aliyense yemwe akanakhoza kukhala mwabwinoko kuposera apo. Inu nonse mumabwera muno wani koloko masana, mpaka faivi koloko, mpaka pamene iwo akutsegula tchalitchi ndi kubweretsa . . . kuwalola anthu alowemo. Inu mumakhala mukuyima mu kuzizira; inu mumakhala mu chisanu; inu mwachita chirichonse; kuyima mozungulira makoma, mpaka miyendo yanu kumapweteka. Ine ndimatha kuwawona amuna, atakhala pansi. Akuwalola akazi aimirire, ndipo osiyanasiyana amakhoza kuyimirira, ndipo monga choncho, atakhala pozungulira. Ine ndinaganiza, "Ambuye, yonse . . . "

347 Iyi yakhala ili sabata yosamvetsetseka. Chinthu chonse chakhala chonga chachirendo, momwe, pamene anthu amabwera, kuwawona iwo ataimirira kuzungulira panjapo,

mmazenera, mu zitseko, kumbuyo kuzungulira kumbuyo, paliponse, akumvetsera. Ndipo kunena za woyankhula, ine ndiri kutali kuti ndingakhale woyankhula. Ine—ine ndiri nalo luntha lochuluka chomwecho, kudziwa kuti ine sindiri, kuti ine sindine woyankhula. Koma ndi chifukwa chiyani anthu amakhala pansi ndi kumamvetsera monga chomwecho? Ndi chifukwa chiyani iwo amachita zimenezo? Iwo samabwera kudzamvetsera kwa munthu wonga ine. Koma iwo amabwera chifukwa muli Chinachake mu zimenezo, chikuwakoka anthu. Uko nkulondola. Mukuona? Muli Chinachake mmenemo, chimene chikuwakoka iwo.

348 Monga mkazi wanga anayima apa pa nsanja ndi kudzayimba, pamene ine ndinkayamba:

> Iwo amabwera kuchokera Kummawa ndi Kumadzulo,
> Iwo amabwera kuchokera ku dziko lakutali,
> Kudzadya ndi Mfumu, kudzadya monga alendo Ake;
> Ndi odala chotani amwendamnjira awa!
> Kuyang'ana pa nkhope Yake yowala
> Kunyezimira ndi Kuwala Kwauzimu;
> Odala ogawana nawo chisomo Chake,
> Monga ngale mu korona Wake kuti awale.

349 Muzikumbukira zimenezo nthawizonse, "Kuti mukhale ngale mu Korona wa Yesu Khristu." Paulo ananena kwa Mpingo, "Inu muli—inu ndinu miyala yowala, kapena, ngale za Korona Wake." Ife tikufuna kuti tikhale ngale za Korona wa Yesu Khristu.

350 Ife sitikufuna, kumuyika konse munthu mu izo. Inu muyiwale chirichonse cha ine. Ine ndine m'bale wanu, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo, wosayenera kukhala moyo. Ndicho ndendende choonadi. Ine sindikunena zimenezo kuti ndikhale wodzichepetsa; ndizo zoona. Mulibemo kanthu mwa ine, wopanda kanthu kamodzi kabwino, nkomwe.

351 Koma chisomo cha Mulungu chalola maso anga osawuka, a mdima ayang'ane kupyola kuseri kwa katani la nthawi ndi kukawona zinthu zimenezo kutsidyako, ndipo ine ndinabwererako.

352 Pamene ndinali mnyamata wamng'ono, ine ndinkawakonda anthu. Ine nthawizonse ndinkafuna winawake kuti azindikonda ine ndi kumayankhula ndi ine. Palibe aliyense ankachita zimenezo, chifukwa cha dzina la banja. Palibe aliyense ankayankhula ndi ine.

353 Koma pamene ine ndinapanga kugonjera kwanga kwa Mulungu, ndiye. . . Anthu athu, mbiri yawo, pokhala achi Irish, ine ndinaganiza, "Mwinamwake. . . Iwo onse anali Achikatolika, ndipo mwinamwake icho chikanakhala Chimenecho." Ine

ndinkapita *kumeneko*, ndipo Iye anali kumbali ina. Ndipo ine ndinapita kumusi ku mpingo Woyamba wa Chibaptisti, ndipo Iye anali kumbali ina.

Ine ndinati, "Ambuye, payenera kukhala njira ina yomwe ili yowona."

Ndipo Chinachake chinati, "Iyo ndi Mawu."

Ine ndakhala ndikuwagwira Mawu amenewo. Kuyang'ana pa masomphenya aliwonse, kulikonseko.

354 Tsiku limene ine ndinkayika mwalawapangodya uko, ndi kuwuyika iwo mkati umo, ine ndinalemba pamenepo chomwe Iye anandiwonetsa ine mmawa uja mmasomphenya. "Ukhale wachangu mu nyengo, kunja kwa nyengo; dzudzula ndi chipiriro chonse ndi Chiphunzitso. Pakuti nthawi idzabwera pamene iwo sadzapirira nacho Chiphunzitso cholamitsa; koma mwakutsata zilakolako zawo adzadziwunjikira okha pamodzi, monga aphunzitsi, okhala ndi makutu oyabwa; ndipo adzatembenuzidwira kuchoka ku Choonadi, nkudzapita ku nthano." Ndipo ndaiwonapo mitengo iwiri imeneyo, yomwe ine ndinayima pafupi nayo, ikuchita chinthu chomwe chomwecho. Uko nkulondola. Ndipo apo ife tiri. Ndipo izo nzoona. Ndipo, tsopano, inu simudzati . . .

355 Kumbukirani. Ndiroleni ine ndikulimbikitseni inu panonso. Osati mudzati, "Zikomo inu," kwa aliyense, nkomwe. Musadzanene, kuganiza kuti, mtumiki winawake kapena chinachake, munthu wina wachivundi; pali chirichonse chabwino cha iye. Chifukwa, iwo siali ayi. Ine sindikusamala yemwe iye ali. Mulibe kanthu kabwino mwa munthu aliyense. Uko nkulondola.

356 Ngati pangakhale mulu wonse wa malipenga atagona apa, ndipo limodzi mwa iwo litayimba nyimbo inayake, ndi munthuyo . . . Malipenga amenewo ndithudi amakhala duu mwangwiro. Ndi munthuyo yemwe angakhoze kuliza lipengalo, yemwe amadziwa chimene iye ati achite, yemwe amatenga lipengalo. Lipengalo silimakhala ndi chochita ndi izo. Kulirako kumabwera kuchokera ku luntha la kuseri kwa ilo. Uko nkulondola. Kotero, malipenga onse amakhala chimodzimodzi.

357 Anthu onse ndi ofanana. Akhristu onse ndi ofanana. Palibe amuna opambana pakati pathu. Ife si amuna opambana, palibe akazi opambana. Ife tonse ndife abale ndi alongo, tonse ofanana, mu gulu limodzi. Ife sitiri "opambana." Wina asamamupange mzake kukhala wamkulu kumuposa winayo, palibe kanthu nkomwe, kakuti wachita. Ayi, bwana. Koma ife tonse ndife anthu basi.

358 Osati muziyesera kutanthauzira zinthuzo. Musamayesetse kumachita chirichonse kuposa kungokhala moyo wapafupi, mukupereka matamando ndi ulemu kwa Yesu Khristu. Aliyense akumvetsa zimenezo tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—

Mkonzi]. Ndipo mukatero zimukondani Iye ndi mtima wanu wonse. Kodi inu mumachita zimenezo?

Ndinkonda Iye, (Ndipo ine ndidzatero!)
Ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

359 Mulungu alemekezeke! Kodi aliyense akumvetsa mwathunthu? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kodi aliyense akukhulupirira? ["Ameni."] Kumbukirani pamene ine ndinkayamba, "Ndani wakhulupirira uthenga wathu? Ndi kwa ndani komwe nkono wa Ambuye wawululidwa?" Kodi Iye wawulula kwa inu, chifundo Chake, ubwino Wake? Ameni. Ingokumbukirani, muzimukonda Iye ndi mtima wanu wonse.

360 Ine ndikubwerera kwathu tsopano. Ine ndidzabwereranso kuno, Ambuye akalola, chakumayambiriro kwa Juni.

361 Mwinamwake, ngati Ambuye adzachiyike icho pa mtima wanga, mwinamwake nthawiyina koyambirira kwa chirimwe ichi, monga Juni kapena penapake, mwinamwake koyambirira kwa kugwa kwa masamba, ngati Ambuye achedwa, ine ndikufuna kudzabwerera ndi kudzakhala ndi mausiku ena seveni, a Malipenga Asanu Ndi Awiri otsiriza. Kodi mungadzazikonde zimenezo? Kodi mungadzazikonde zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kodi inu muzindipempherera ine, kuti Mulungu adzandithandize ine? ["Ameni."] Chabwino.

362 Kufikira ine ndidzakumane nanu inu kachiwiri, kumbukirani nyimbo yabwino yakale iyi:

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

363 Tsopano ine ndikufuna kuti inu muweramitse mitu yanu. Ine ndikufuna ndikupempherereni. Abusa asanakubalalitseni, ine ndikufuna ndikupempherereni.

364 Atate athu Akumwamba, mulole kuti anthuwa, Ambuye, amvetsetse. Chomwe, ine ndikutsimikiza kuti pali ena omwe sakumvetsetsa. Koma, Atate, mulole iwo—iwo adziwe cholingacho. Ndipo mulole kuti iwo amvetsetse, Atate, kuti—kuti ndi chisomo Chanu kwa iwo kuti zinthu izi zawululidwa. Ndipo ine ndikufuna kukuthokozani Inu, Ambuye, chifukwa cha chidziwitso chodziwira zinthu izi zomwe Inu mwaziwulula kwa ife.

365 Ndipo ndikupempherera aliyense yemwe ali pano, aliyense yemwe wakhalapo pa misonkhanoyi. Ngati pali ena omwe sakukhulupirira, mulole, Ambuye, kuti iwo akhale okhulupirira.

366 Ine ndikuwapempherera onse omwe ati adzamvetsere kwa Mauthengawa pa tepi. Ndipo ngati Iwo ati adzagwere, chomwe Iwo adzatero, sindikukaikira, mmakomo ndi mmalo a osakhulupirira ambiri omwe ati adzatsutse; koma, Atate, ine ndikupempherera mmodzi aliyenseyo, kuti iwo asanene mawu aliwonse amwano, kuti iwo poyamba akakhale pansi ndi kukafufuza Malemba pa zomwe zayankhulidwazi, ndipo kenako akanene kwa Inu kuti iwo mowona ali owonamtima ndipo akufuna kudziwa ngati ichi chiri Choonadi, kapena ayi. Ndipo ine ndikuwapempherera iwo, Atate.

367 Ndipo ine ndikuwapempherera awa omwe akhala akuyima pa makoma awa, omwe anayima panja, amene anakhala mmagalimoto mwawo, ana aang'ono, ndi kwa onse amene akhala ali mkati muno. Ndipo basi onse a iwo, Ambuye, ine ndikuwapempherera iwo.

368 Ndipo ine ndikupemphera kuti mapemphero anga ayankhidwe, kuti Inu muwadalitse iwo. Poyamba, Ambuye, mumpatse aliyense Moyo Wamuyaya. Ine ndikupemphera kuti pasakhale mmodzi wa iwo wotayika, ngakhale mmodzi.

369 Ndipo tsopano, Atate, ife sitikudziwa nthawi imene chochitika chachikulu ichi chiti chidzachitike. Koma pamene ife tikuwona zizindikiro izi zikuwonekera, ndi zochitika Mwamalemba, zikumatenthetsa mtima wathu mopyola muyezo. Ndipo ine ndikupemphera, Atate Mulungu, kuti Inu mutithandize ife.

370 Ine ndikupemphera kuti Inu mumuthandize m'busa wathu wokondedwa, M'bale Neville. Mpangeni iye, Ambuye, wodzaza ndi chisomo, ndi wodzaza ndi mphamvu, ndi kumvetsa, kuti iye azikatenga Chakudya chosungidwa ichi ndi kumakadyetsa nkhosa za Mulungu.

371 Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu muwaike matenda kutali ndi ife. Mulole kuti izo zidzafike pochitika, kuti pamene anthu adzadwala, kuti iwo adzakumbukire kuti Magazi apakali pano ndi okwanira mu zonse a Ambuye Yesu ali pa guwa, kuti apange chitetezero. Ndipo ine ndikupemphera kuti iwo achiritsidwe pompano.

372 Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muithamangitsire mphamvu ya Satana kutali ndi iwo, yowakhumudwitsa iwo, kapena kuyesera kuwapangitsa iwo kuti apange miyambo. Kapena, mungokhalitsa mphamvu zonse za mdaniyo kutali, Ambuye. Tiyeretseni ife ku Mawu Anu. Perekani izi, Ambuye.

373 Ndiye, Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine. Ine—ine—ine ndikuyamba kuzirala, Ambuye. Ine ndikudziwa kuti masiku anga sangakhozenso kukhala ochuluka kwambiri. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine, kundirola ine kuti ndikhale woona, Ambuye, ndi kuwona mtima ndi kudzipereka, kuti ine ndikakhoze kunyamulira

Uthenga kutali monga iwo unadzozedwera kwa ine kuti ndikawunyamulireko. Ndipo pamene idzafika nthawi yakuti ine ndidzayenera kutula pansi, ndi kudzafika ku Mtsinje, ndipo mafundewo nkuyamba kubwera mkati, O Mulungu, mulole kuti ine ndidzakhoze kupereka Lupanga lakale ili kwa winawake yemwe ati adzakhale woonamtima ndi Ilo, Ambuye, ndipo adzanyamule Choonadi. Perekani izi, Ambuye. Ndipo, kufikira nthawi imeneyo, ndithandizeni ine kuti ndikhale wamphamvu ndi wathanzi, ndi wolimba mtima.

374 Thandizani mpingo wanga. Tidalitseni ife palimodzi, Ambuye. Ife ndife Anu. Ife tikumverera tsopano kuti Mzimu Wanu uli pakati pathu. Ife tikukhulupirira kuti Inu muyankha mapemphero athu. Pakuti, tikudzipereka tokha kwa Inu, ndi Mawu Anu, kwa utumiki kwa masiku athu onse pa dziko lapansi lino, mu Dzina la Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, Mpulumutsi wathu wokondedwa, kwa ulemelero Wake. Ameni.

Ine . . . (Mulungu akudalitseni inu!) . . .
Ndinkonda Iye (ndi mtima wanga wonse),
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.

375 Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville . . . ? . . . Muzikhala pa malo antchito . . . ? . . .

CHISINDIKIZO CHACHISANU NDI CHIWIRI CHIKUPITIRIRA

376 [Inu mwangotsiriza kumene kumvetsera *Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri* choyambirira monga icho chinalalikidwa mu uthunthu wake Lamlungu madzulo, pa Malichi 24, 1963 ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana. M'bale Branham sanafune kuti kujambula koyambirira uku kuperekedwe kwa anthu. Tsiku lotsatira, Lolemba, pa Malichi 25, 1963, M'bale Branham anapita ku chipinda cha motelo cha M'bale Fred Sothmann ndi M'bale James Maguire, amene pa nthawiyo anali opanga matepi. M'bale Branham anawauza abale awa kuti, "Ine sindikufuna kuti uthenga uwu utumizidwe momwe iwo ulirimu." Atatha kumvetsera kwa tepiyo mwiniwake, iye anawalamulira abalewo kuti akaiyimike tepiyo pamalo enaake, ndipo pa malo amenewo (kuyambira pa ndime ya 261) anajambula gawo latsopano la pafupi utali wa maminiti twente (ndime ya 377-415). Gawo latsopano ili zitatero linadzagwiritsidwa ntchito kulowa mmalo mwa mapeto a uthenga woyambirira uja (ndime ya 261-375). Kujambula uku kunali ulaliki wokhawo wa *Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri* umene unatulutsidwa kufikira 1966. M'bale Branham atachokapo, gulu la William Branham Evangelistic Association lonse linagwirizana kuti atulutse tepi imene inajambulidwa moyambirira ku kachisi. Kuyambira nthawi imeneyo, maulaliki awiri onsewo akhala akuperekedwa. Ife tsopano tayika uthenga

wowonjezera uwu wa M'bale Branham pa tepi imodzi, limodzi ndi *Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri* choyambirira. Liwu lotsatira limene muti mulimve likhala la M'bale Branham mu chipinda cha motelo Lolemba, pa Malichi 25, 1963—Mkonzi].

377 Chidzakhala chinthu chabwino kuti iye sakudziwa chirichonse cha Icho. Chifukwa, ngati iye akanatero, ndiye iye akanachikopera Icho. Ndiwo machenjerero ake ochitira zinthu.

378 Kotero, chomwecho, Mulungu wachipanga Icho mobisika chomwecho kwa dziko lonse, ngakhale Kumwamba, mwakuti palibe njira yochimvetsera Icho, kokha pamene Mulungu adzachiwulule Icho, Iyemwini.

379 Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire, usikuuno, kuti mu Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, apo panali—cholinga chofutukuka patatu cha Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi.

Panali cholinga chofutukuka patatu cha okwera pa kavalo.

380 Pakhala pali cholinga chofutukuka patatu mu zinthu zonse izi. Izo zikutibweretsa ife mmbuyo ku zitatu. Ndi seveni, kachiwiri, mwaona, Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, Mbale Zisanu Ndi Ziwiri, ndi zina zotero. Tsopano, mu zitatu ndi zisanu ndi ziwiri, ndiwo mawerengero a Mulungu mu masamu Ake a kuwulula Mawu Ake.

381 Tsopano inu muzindikira, monga mu a—a—okwera aja, tsopano, panali akavalo atatu omwe anatuluka. Mmodzi wa iwo anali woyera, wina anali wofiira, wina anali wakuda. Ndiyeno, mu kavalo wachinayi, bwanji, onse a iwo anasakanizidwa pamodzi. Mwaona, cholinga chofutukuka patatu.

382 Tsopano, Mulungu anachita chinthu chomwecho. Mulungu anachita chomwecho pamene Iye anatumiza mkango Wake, omwe anali Mawu Ake, kuti akamenyane ndi wotsutsakhristu.

383 Kenako ife tikupeza kuti Iye anatumiza ng'ombe ija mu nthawi ya a—nthawi ya chisautso, chinyama chansembe. Ndipo mu nthawi ya chisautso iyi, ndizo zonse zimene anthuwo akanakhoza kuchita, kunali kugwira ntchito basi, ukapolo, ndi kudzipereka okha monga nsembe.

384 Ndiye ife tikupeza kuti, mu m'badwo wotsatira, umene unali m'badwo wa okonzanso, Mulungu anatumiza nzeru ya munthu, mutu wonga wa munthu pa Chamoyo, yomwe inali mphamvu yomwe inatuluka mwa okonzanso.

385 Tsopano kodi inu munazindikira? Monse. . . Nzosadabwitsa kuti anthu a mmasiku ano akukhalabe moyo mmatsire, monga zinkakhalira kuchokera ku m'badwo wa okonzanso, chifukwa iwo amangoziwona izo mwa—njira yachipembedzo yowonera izo. Iwo amaziwona izo mwanjira yomwe maseminare

aphunzitsira izo. Imeneyo inali njira ya Mulungu pa nthawi ina, koma ife tadutsa nthawi imeneyo.

386 Tsopano ife talowa mu m'badwo wa mphungu, vumbulutso loti liwululidwe, chinthu chonsecho. Tsopano mufanizitse izi ndi Chivumbulutso mutu wa 10, ndime ya 1 mpaka 7. Ndipo ife tiwona apa mu Vumbulutso ili, Chivumbulutso apa, 10:1 mpaka 7, kuti, "Mmasiku a kuwomba kwa Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, kunali kuti adzatsirizitsa zinsinsi zonse za Mulungu."

387 Tsopano ife tikupeza, apanso, mu izi, kuti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, tsopano pokhala kuti chatsegulidwa, icho chinali kwa cholinga chofutukuka patatu. Tsopano, apa pali zolingazo.

388 Chinthu choyamba, chinali, chakuti namwali wogona anali woti adzadutse mu nthawi ya Chisautso kuti adzayeretsedwe. Iye amayenera kuti adzayeretsedwe chifukwa cha machimo ake a kusakhulupirira ndi kukana Uthenga. Ichi, iye anachitidwa mu nthawi ya Chisautso. Ife tikuwona kuti iwo akuthera cha apa mu Chivumbulutso 7, pakati pa mutu wa 6 ndi wa 7 apa, kuti iye anali atayeretsedwa, ndipo iye anali atapatsidwa mikanjo yake. Tsopano, iye si Mkwatibwi. Koma uwo ndi mpingo, anthu oyera omwe—omwe—omwe sanakhale nawo mwayi, mwinamwake, woti alandire Uthenga, kapena mwanjira inayake kuti iwo anachititsidwa khungu ndi aneneri abodza awa. Ndipo iwo—iwo sanapeze mwayi, ndipo komabe iwo ndi owona mtima kwenikweni mu mtima mwawo. Ndipo Mulungu akudziwa mtima wawo. Ndipo apa iwo akuyeretsedwa, mu nthawi iyi.

389 Inu mukuzindikira zimenezo kuti, nthawi ina ya kuyeretsa, ndiyo ya Israeli, pamene iye akusonkhana. Kumeneko ndi kufutukuka kwachiwiri. Mulungu akumutsuka Israeli mu nthawi ya Chisautso. Kuchokera mwa mamillioni omwe ati adzasonkhane kumeneko, uko kudzakhala osankhidwa handiredi ndi forte-foro sauzande, ndipo iwo adzayeretsedwa, nawonso. Mulungu akuyeretsa Israeli.

390 Zindikirani, pali dziko lonse loti lidzayeretsedwe. Kudzakhala chinthu choterocho monga mwezi, nyenyezi, ndi chirengedwe chonse, zidzayeretsedwa. Inu mukuona chomwe icho chiri? Dziko lapansi likudzikonza lokha mwatsopano, likuyeretsedwa, kukonzekera Zakachikwi. Zakachikwi zikubwera. Ndipo, mwaona, chirichonse chimene chiri ndi uve uliwonse mwa icho chiri choti chidzayeretsedwe mu nthawi ya Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi.

391 Tsopano, tsopano, kodi inu mukuzindikira? Pa kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi, nachonso chiri mu chinsinsi chofutukuka patatu. Chimodzi ichi, ine nda . . . ndidzayankhula ndipo ndayankhula, kuti icho ndi chinsinsi cha Mabingu Asanu Ndi Awiri. Mabingu Asanu Ndi Awiri

Kumwamba adzafutukula chinsinsi ichi. Icho chidzachitika pa Kudza kwa Khristu kumene, chifukwa Khristu anati palibe aliyense akudziwa nthawi imene Iye ati adzabwerenso.

392 Kodi inu munazindikira, pamene Ayuda anamufunsa Iye zimenezo? Kudziwa . . . Pamene tinafanizitsa Lembalo apa ndi Mateyu 24, ndi Zisindikizo zisanu ndi chimodzi, Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri chinasiyidwa. Chifukwa, inu mukuona, Khristu anati, "Mulungu Yekha Mwiniwake ankadziwa; osati ngakhale Angelo." Nzosadabwitsa, Icho sichinalembedwe nkomwe. Inu mukuona, iwo anakhala chete; palibe kanthu kanachitika pamenepo. Angelo sakuchidziwa Icho. Palibe aliyense amene akudziwa nthawi imene Iye akubwera.

393 Koma padzakhala—padzakhala a—Maliwu Asanu Ndi Awiri, a Mabingu awa, omwe ati adzawulule vumbulutso lalikulu pa nthawi imeneyo. Kotero, ine ndikukhulupirira, kwa ife omwe . . . Ngati ife sitikuchidziwa Icho, ndipo ngati ife . . . Icho sichidzadziwika kufikira nthawi imeneyo. Koma icho chidzawululidwa mu tsiku limenelo, mu ora lomwe icho chikuyenera kudzawululidwamo. Chotero, chinthu choti ife tichite ndicho kukhala olemekeza pamaso pa Mulungu, ndi kumamutumikira Iye, ndi kumachita zonse zomwe ife tikuzidziwa kachitidwe kake, ndi kumakhala moyo wabwino, miyoyo ya Chikhristu. Apa, tsopano, ife tikupeza kuti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi chatsegulidwa kwa ife; ife tikuchiwona Icho. Ndipo ife tikudziwa kuti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi sichingamatulidwe kugulu kufikira ora limenelo litadzafika.

394 Tsopano, panali chifukwa china chimene Mulungu analolera kuti Maliwu Asanu Ndi Awiri awa abangule. Chifukwa, Iwo ayenera adzabwere, mwaona. Pakuti a . . . Ife tikupeza kuti Khristu, Mwanawankhosa, anatenga a—Bukhu mdzanja Lake, ndipo Iye anatsegula Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri. Koma, mukuona, icho ndi chinsinsi chobisika. Palibe mmodzi akuchidziwa Icho. Koma, Icho—Icho, motsatira kumene ndi zomwe Iye ananena, "Palibe aliyense akanati adzadziwe za Kudza Kwake." Iwo nawonso sakanadziwanso za chinsinsi cha Mabingu Asanu Ndi Awiri awa. Kotero, mukuona, izo nzolumikizana pamodzi.

395 Mwakuchuluka kumeneko, ife tiri nako kumvetsetsa kwa Icho, lero, chifukwa zina zonse za Icho zafutukulidwa; koma ichi sichinafutukulidwe. Koma nditakhala mchipinda changa, ndipo ine ndinamva ichi . . . kapena, osati kuchimva icho, kani, koma ndinachiwona Icho chikufutukuka kwa Mabingu Asanu Ndi Awiri awa. Tsopano, uwo ndi utali wa momwe ife tingakhoze kupitira, pomwe apo.

396 Ndipo tsopano ine ndikudalira kuti aliyense wa inu azimutumikira Mulungu ndi kumachita chimene chiri

cholondola. Ndi kumamukonda Iye, moyo wanu wonse, ndi kumamutumikira Iye. Ndipo Mulungu adzasamalira zinazo.

397 Tsopano, ife tiri nazo, mu kutsirizitsa apa tsopano, mwa chisomo cha Mulungu, zinsinsi zonse za Zisindikizo zisanu ndi chimodzi zomwe zakhala ziri zosindikizidwa, ndipo ife tikumvetsa ndi kudziwa apa kuti Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri sichiri choti chidzadziwike kwa gulu.

398 Tsopano, Kudza Kwake, pa ora la Kudza Kwake, pamene chiwonongeko cha dziko lapansi, inu mukudziwa. Iye ananena pamenepo, "Chidzakhala chiyani chizindikiro cha kubwera kwa kutha kwa dziko lapansi?" Mu Mateyu 24, apo pamene iwo anamufunsa Iye funso limenelo. Iye anapita mmusi kwa izo. Iye anawauza za Israeli akusonkhanitsidwa monga fuko, mu ndime ya 31, ya Mateyu 24:31. Koma kenako Iye anayamba kupita ku mafanizo, mwaona. Ndiye inu mukuwona . . . "Phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu. Pamene inu mudzawona iwo ukuphukira masamba ake, bwanji, inu mudzadziwa kuti dzinja liri pafupi. Ndiyeno pamene inu mudzawona izi zikufika pochitika, ndiye mudzadziwe kuti nthawi ili pafupi." Mwaona, Israeli akusonkhana mu dziko lakwawo lomwe. Koma, inu mukuzindikira, kuti Iye analumpha vumbulutso la Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi.

399 Ndipo apa, pamene Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, pamene Iye anachitsegula Icho, Iye anachilumphanso Icho kachiwiri, mwaona. Chotero ife tikuwona kuti Icho ndi chinsinsi chathunthu, chotero oralo silinafikebe kuti chinsinsi ichi chidziwike. Chotero, ife tafika apa, ndipo zina zonsezo za Icho zidzadziwika ikamadzakwana nthawi imeneyo yomwe Yesu ati adzawonekere pa dziko lapansi kachiwiri, kwa Mkwatibwi Wake, kapena chirichonse chimene chiti chidzachitike pa nthawi imeneyo. Tsopano, kufikira nthawi imeneyo, tiyeni tonse tizingopemphera, tizikhala moyo wabwino, wowongoka, miyoyo ya Chikhristu, kumayembekezera Kudza Kwake.

400 Ndipo tsopano ngati tepi iyi iti idzagwere mmanja mwa anthu ena kwinakwake, musati mudzayesere kupanga mtundu uliwonse wa mchitidwe kuchokera pa iyo. Chinthu chokhacho chimene inu muti mudzachite, inu mudzangopitiriza kumamutumikira Mulungu. Chifukwa, chinsinsi chachikulu ichi ndi chachikulu kwambiri mwakuti Mulungu sanamulole ngakhale Yohane kuti achilembe Icho. Icho chinabangula, koma Iye . . . akudziwa kuti, anatilonjeza ife kuti Icho chidzatsegulidwa. Koma, mpaka pa nthawi ino, Icho sichinatsegulidwe.

401 Ndipo tsopano ife tiri oyamikira kwa Mulungu pa zomwe Iye watiwonetsa ife. Ine ndakhala ndiri mu chipinda kumtunda uko kwa masiku eyiti. Ndipo Uthenga umene ine ndangotsiriza kumene kukufotokozerani inu, ambiri a inu

pano mudzamvetsetsa. Ndipo ine ndinalonjeza kuti panali chinachake chomwe chimachitika, chauzimu, nthawi zonse, chimene ine ndinali wotsimikiza kuti inu munali kuchiphonya icho. Ndipo apa pali chomwe icho chiri; ndicho kutsimikizira kwamtheradi kwa kutanthauzira uku kwa Malemba kukhala akutumizidwa ndi Mulungu.

402 Chifukwa, ife tisanalowe nkomwe mu Izo, ndipo ine ndinachoka kupita kumadzulo, Ambuye anandiwonetsa ine masomphenya tsiku lina, pafupifupi teni koloko, mmawa wina. Ndipo ine ndinabwera ndipo ndinadzawafotokoza iwo kuno, kuti ine ndinali nditawawona iwo; ine sindinadziwe chomwe iwo anali. Kunali kuwundana kwa Angelo asanu ndi awiri. Ife tikumbukira zimenezo. Inu mukazipeza izo pa tepi, yotchedwa, *Ndi Nthawi Yanji Ino, Bwana?* Chabwino, tsopano, ndicho ndendende chimene inu mukuchiwona tsopano. Angelo asanu ndi awiri . . . Ine ndinali kumadzulo.

403 Inu mukuwakumbukira, amthenga ang'ono ang'ono aja; iwo anapita kummawa. Amthenga achiwiri, nkhunda, mbalame zokulirapo, izo zinapita kummawa. Ndipo kenako ine ndinayang'ana . . . Izo zimakhala ndi ine, nthawi zonse. Zimenezo zinali Chikoka Choyamba ndi Chachiwiri.

404 Tsopano, Achitatu anabwera kuchokera kumadzulo, anadzasesera kutsogolo ndi liwiro lalikulu, lowopsya, ndipo Iwo anadzandinyamulira ine mmwamba. Omwe anali kubwerera kummawa, ali ndi chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri izi. Basi monga zinanenedwera mu—mu loto la Junior Jackson, lomwe Ambuye anandirola ine kuti ndirimasulire kwa iye uko, "Mkati mwa piramidi imeneyo, munali Mwala woyera umene unali wosalembedwa." Ndi chifukwa chake ine ndinayenera kupita kumadzulo, kuti ndikalumikizane ndi Uthenga wa Angelo awa, kuti ndibwerere kuno kudzawulula Izo kwa mpingo. Kumbukirani, ine ndinati, "Zinthu zotsatira zomwe ziti zidzachitike zidzakhala pano pa tchalitchi." Ndizo ndendende basi.

405 Chinthu china, ine ndikufuna kuti inu muzindikire chimene chinachitika. Ndipo ngati inu mukumvetsera ku tepi, ya *Ndi Nthawi Yanji Ino, Bwana?*, inu mukazindikira kuti Mngelo mmodzi anali wofunikira kwambiri kwa ine. Ena onse a Iwo basi anali kuwoneka mwawamba. Koma Mngelo uyu anali Mngelo wodziwika. Iye anali kumanzere kwanga, mu kuwundana kwa mawonekedwe a piramidi.

406 Ndipo, kumbukirani, kuti munali mu piramidi, momwe Mwala woyera wachinsinsi wosalembedwawo unali. Ndipo Angelowo ananditengera ine mkati mwa piramidi iyo ya Iwoeni, zinsinsi za Mulungu zikudziwika kwa Iwo okha. Ndipo, tsopano, Iwowo anali Amthenga omwe anali atabwera kuti adzamasulire piramidi imeneyo, kapena Uthenga umenewo wa chinsinsi cha

Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri izi zomwe ziri mkati mwa piramidiyo.

407 Tsopano, Mngeloyo, anali kumanzere kwanga, akanakhala kwenikweni wotsiriza, kapena Mngelo wachisanu ndi chiwiri, ngati ife tikanawawerenga Iwo kuchokera kumanzere kupita kumanja. Chifukwa, Iye anali kumanzere kwanga; ine ndikuyang'ana kwa Iye, kuloza kumadzulo, Iye akubwera choloza kummawa, akanakhala ku mbali ya kumanzere. Chotero, uwo ukanakhala Uthenga wa mngelo wotsiriza, wofunikira kwambiri. Kumbukirani momwe ine ndinanenera kuti Iye anali nawo Wake, analoza mutu Wake mmbuyo; ndi mapiko Ake aakulu, akuthwa; ndi momwe Iye anawulukira molunjika kupita kwa ine. Tsopano, icho ndicho Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri ichi. Icho chikadali chinthu chofunikira. Ndipo ife tiri...Ife sitikudziwa chomwe Icho chiri, panobe, chifukwa Icho sichikuloledwa kuti chimatulidwe.

408 Koma tsopano, aliyense wa inu mu msonkhano wazindikira zimenezo, wakhala uli msonkhano wotani! Aliyense amangowoneka kuti anali...pa mapeto pomwe pa mpando wawo. Ndipo aliyense ataimirira mozungulira apa, wani koloko, thuu koloko masana, kumadikirira kuti zitseko zitsegulidwe, ndi kudzakhala kuno kutsogolo. Ataimirira mozungulira makoma; miyendo yadzanzi, ndi chirichonse.

409 Ndi chiyani chimenecho? Iwo wakhala uli Mzimu Woyera ukutumiza Amthenga awa, ndipo Iwo akhala akuwulula Izo kwa ife. Ndiyeno muzindikire momwe Izo zagwirizanirana ndi Mawu, ndendende.

410 Ndiyeno kuti zikudziwitseni inu nonse kuti izi ndi Choonadi, Iye ananeneratu izo pafupifupi—pafupifupi miyezi iwiri tsopano, kapena kupitirira, izo zisanachitike nkomwe. Kuti, pamene ine ndinapita kumadzulo, ndisakuzidziwa Izo; ndinabwereranso kuno ndi kumasulira monga Iye waperekera Izo. Tsopano kumbukirani, mmasomphenya, Iye sanandiuze ine kanthu kamodzi mmasomphenya pamene Iye ananditengera ine mmwamba. Ine ndinachita mantha, ndimawopa kuti ndifa, ndiphedwa mu kuphulikako. Inu mukuona, Iwo sakanakhoza kuchita zimenezo.

411 Kumasulirako kunabwera basi pamene ine ndinali kukusowa Iko, umo munali mchipinda, ndipo ine ndinazipereka Izo basi monga momwe Iye anaziperekera Izo.

412 Tsopano, mukuona, amzanga, masomphenya samalephera. Iwo nthawizonse amakhala angwiro. Iwo ndi owona basi ndendende.

413 Tsopano, masomphenyawo, kuphatikizapo Mawu, kuphatikizapo mbiriyakale, kuphatikizapo mibadwo ya mpingo, ndi zonse, zikugwirizana pamodzi. Chotero, ine ndikhoza kunena moona, kuti, mwakukhoza kwa kumvetsa kwanga,

ndi molingana ndi Mawu a Mulungu, ndi masomphenya, ndi vumbulutso, kumasulira kwakeko ndiko PAKUTI ATERO AMBUYE.

414 Tsopano, Ambuye akudalitseni inu nonse, aliyenseyo, molemera kwenikweni, pamene ife tikuyimirira tsopano ndi kuyimba nyimbo yabwino yakale iyi ya mpingo. Mulungu akudalitseni inu, mmodzi aliyense. Ameni.

415 [M'bale Branham akuwonjezera mizere foro yotsatirayi, yotengedwa mu ndime ya 374-375 ya Uthenga wake usiku watha, Malichi 24, 1963—Mkonzi].

Ine . . . (Mulungu akudalitseni inu!) . . .
Ndinkonda Iye, (ndi mtima wanga wonse),
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.

Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville . . . ? . . . Zikhalani pa malo antchito . . . ? . . .

63-0324E Chisindikizo Chachisani Ndi Chiwiri
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chivumbulutso Cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org